

Thunthu La Munthu Wangwiro

Jeffersonville, Indiana, USA

Okotobala 14, 1962

1 Zikomo M'bale Neville, Ambuye akudalitseni.

Ndi chabwino kubweranso ku Kachisi m'mawa uno. M'mawa wabwino wa chisomo kwa inu nonse. Ndipo ine ndikudalira kuti ili likhala tsiku lopambana kwa ife tonse ndi pamaso pa Ambuye wathu. Ndipo tsopano, ine ndiri ndi phunziro m'mawa uno. Ine ndikufuna ndilowe nthawi yomwe ino ku phunziro ili chifukwa ndi^Ine ndikuganiza ndi kofunika, ndi kuteteza kuti gulu lisakwiye inu mukudziwa^ kukhala motalikirapo, ndi ambiri atayima. Ine ndikupita molunjika mu phunziro.

2 Ndipo tsopano, usiku uno ine ndinafuna kulankhula pa phunziro la Namulondola wa Moyo Wanga. Ndipo ine ndikuyembeza kuti ambiri amene angathe^onse amene angathe, adzakhalapo pa nthawi imeneyo ya usiku uno. Komabe, ngati inu muli ndi mpingo wanuwano, tiri^ndithu ife tikufuna kuti inu mukakhale muli ku mpingo wanu. Iyo ndiyo ntchito yanu: kukhala muli uko, komwe inu muli ndi malo anu otumikira, kuti muni wanu uwale.

Tsopano, ife tikungoyembekezabe kuti nthawi iliyonse imene titi tibwererensho tidzakhalala tiri ndi malo okulirapo muno. Koma ife tikukhala ndi zovuta pa izi, o, paliponse. Gulu la Mathrasti layesesa kukumba mu chirichonse. Iwo akatumiza ku malo amodzi; uko amavomereza; ndiye mkutumizanso kwina kumene amakambiranapo, ndipo amachibweza icho; amachivomereza icho cha kuno, ndi kubwerera^o, ndi nthawi yotani imene ife takhala nayo. Koma inu mukudziwa, Satana nthawi zonse ndi wa ndewu motsutsana ndi chomwe chiri cholondola. Ingokumbukirani, inu nthawi zonse muli chapafupi^

3 Ine ndimadabwa kuti iwe uli kuti, Anthony, (ine sindimamuwona iye^ine ndinakumana ndi abambo ako,) ndipo ine ndinayang'ana mu msonkhanowu; iwo anati iwe unali utakhala uko. Ife takondwa kukhala nawe kuno ndi abambo akowa kuno ndi ife_M'bale Milano wochokera ku New York. Ine ndikuyembekeza^kupita kutsidya kwa nyanja nthawi ino ine ndichokepo nthawi ya "kusungunuka kwa chisanu" ndipite ku New York, kwina kwake kumeneko, ngati Ambuye alola.

Ndipo chotero ife tiri okondwa kwambiri chifukwa cha aliyense wa inu. Ndi zabwino ndithu, kuti inu mukhale muli kuno. Ndipo ife tinali ndi nthawi yopambana usiku watha, kapenabe ine ndinali. Ine sindi^Yesaya mu Kachisi. ^ndipo m'mawa uno ife tikufuna kulankhula pa phunziro, kapena kuphunzitsa kani, ngati ife tingathe, Kumanga Kachisi Wamoyo^, Kumanga a^Kumanga Kachisi Wamoyo wa Mulungu Wamoyo, Malo Ake Okhalamo: Munthu Wangwiro_Kachisi Wamoyo wa Mulungu Wamoyo, momwe Iye amakhala.

4 Ine ndikumva kuti ali ndi kayimbidwe kabwino kuno, ndipo ine sindinakhale ndi mwayi womvera. Ndipo usiku uno ine ndiyesa kubwera kuno. Mkazi wanga wandiwuza ine za M'bale Ungren, (ine ndikukhulupirira ndilo dzina lake) wochokera ku Tennessee. Tsopano, iyeyu anali kuno usiku watha. Ine sindikumuwona iye m'mawa uno, koma ine ndikuganiza kuti ali momwe muno kwinakwake. Ndipo ine ndikanafuna nditamumva iye akuyimba usiku uno, ngati ine ndingathe, mwina ija yoti Kuchokera ku Ulemerero Wake kapena Ndinu Wamkulukulutu. Ine ndikanakonda nditamva izo. Ndi angati amene angafune atamvera M'bale Ungren akuyimba? O, ine ndimakonda kuyimba kwabwino. Ndipo Meda anati kuti iyeyu ali ndi mawu aakulu, ndipo likundikumbutsa ine za M'bale Baxter. Iye ndi woyimbanso, monga momwe ife tonse tikudziwira. Ndipo Kuchokera ku Ulemerero Wake kapena Ndinu Wamkulukulutu, ine ndikukhulupirira ine ndamuwonano pomwe iye ali tsopano^ Zikhala zotheka, M'bale Ungren, usiku uno, ngati mungathe? Ngati inu muti mukhalepobe. Kodi inu muyesa kukhalapobe mpakana msonkhano utatha usiku uno? Chabwino, ine ndingoti, bwanji choncho ngati ife^Ine sindikufuna kumuyambitsira aliyense vuto lililonse, koma bwanjino osangoti, ngati iye ati adzathe pa nthawi ya Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri pamene ife tizidzalalikirira izo, ngati inu muti mudzabwere, ine ndikanafuna nditadzazijambula, mukuona, kuti ndikhale nayo: Ndinu Wamkulukulutu ndiponso Kuchokera ku Ulemerero Wake mu nthawi imeneyo?

5 O kodi sizopambana kutumikira Ambuye? Ine sindikudziwa chomwe ine ndikanachita ngati ine sindikanakhala Mkristu. Ndi kwabwino basi kukhala Mkristu; ine ndimangomva ngati ndidumphedumphe ndi kufuula mokweza mawu anga. Kukhala Mkristu_taganizirani za izo. Ozikika wense mwa Khristu.

Ine ndikudziwa ine ndimatchula bambo uyu dzina lolakwika nthawi iliyonse. Mwina ndi "S.T.," kapena "T.S.," kapena chinachake ngati icho. Sumner, M'bale Sumner. Ine ndikufuna kumuthokoza iye palimodzi ndi mkazi wake wabwinoyo. Ine ndikuganiza kuti iye anataya pafupi, zikuwoneka ngati miyezi isanu ndi umodzi akutayipa Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo, ndipo tsopano ife tiri nayo kuno yotayipidwa kale, yokonzekera kutsimikizira, ndipo zikapangidwa kukhala bukhu_Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo. Mlongo Sumner, kulikonse komwe inu muli, ndithudi inu mutirola ife tikulipireni inu pa izo. Izo zinatengera ntchito yambiri. Bwanji, ndi lokandapala chotero. Ilo linganditengere ine pafupi miyezi isanu ndi umodzi kuti ndiriwerenge lonse, nanga kuti ulembe kuchokera pa matepi, ndikubwereranso ndi kuchotsamo zobwereza, ndi kulipanga mwa bukhu. Ife tirikonza kuti likhale lokonzekera kutumidwa kosindikiza mosachedwetsa, pakuti ife tikuganiza kuti chinthu choti anthu akhale nacho pakali pano, ndipo inu mukhoza kumaliwerenga mofatsa. Ndipo Billy amangondiwonetsa ine, pamene ine ndinabwerera uko

maminiti angapo apitawo, kuti linali_linali lokonzekera tsopano kupita kwa osindikiza. Koteru, Mlongo, Kachisi uyu akulipirani inu chifukwa cha izo. Ine sindikuyembekezera kuti inu mungachite izo popanda kanthu. Kapena ngakhale ngati ife titi tisindikizitse bukhulo ndikupanga mtengo wake pa ilo, kapena chinachake, tidzakhazikitsa mtengo, umene inu muzidzalendirapo kenakake iwo akagulitsa, njira iliyonse. Inu mungolankhula ndi Gulu, Gulu la Mathrasti, ndipo ena mwa iwo mmenemo, ndipo iwo asamalira izo kwa inu. Ambuye akudalitseni inu bwino kwenikweni.

6 Ka M'bale kathu kachikulire ndi Mlongo Kidd akhala apa, mwinamwake pansu pa zana (pang'ono pokha basi). Ndipo ine ndinakumana ndi mlongoyo posachedwapa ndipo anati, "Mwina, uku kukhala kukumana kwathu kotsiriza kuti ndikuwoneni inu, M'bale Billy," iye anati, "Ine ndikukalamba kwambiri."

Ine ndinati, "O, mai! Ine sindikufuna kumva inu mukulankhula izo." Kungokhala ngati amayi ndi abambo athu okalamba. Ife timakonda M'bale ndi Mlongo Kidd, aliyense amatero. Zimangochita chinachake kwa ine pamene ine ndiwawona iwo akulowa mu tchalitchi, anthu awiri okalambirapo pang'ono choterowo; ndipo kungogoniza, iwo anali akulalikira Uthenga ine ndisanabadwe, ndipo ine ndine bambo wachikulire. Inde, tangogonizani, iwo amalalikira ine ndisanabadwe. Ndipo ndine ndiri pano tsopano. Ine ndimakhoza kuganiza, "Ine ndikukalamba kwambiri," ndipo ndikungogoniza, nditatsala pang'ono kuganiza kuti ndingosiya; ndipo ine ndimawona M'bale ndi Mlongo Kidd akudzalowa: "Ulemerero kwa Mulungu!"

Ine ndimati, "Ayi, ine ndikumva bwino." Inde, bwana, kuwawona iwowa, iwo angathe bwanji^Momwe iwo amakudzozerwa iwe kwenikweni. Ndiye iwe umazindikira kuti pafupifupi msinkhu wangawunso, ndipo n'kumapitirirabe pa ntchitoyi. Anadza m'mawawu kudzapempha mabuku_kuti atenge mabuku azikagulitsa, amafuna matepi, kuti azipita nakatembenezira miyoyo pomvera matepi awa_komatu wasinkhu pafupi zaka zana. Tsopano, mapiko anu awiri ali kuti amene ife timawanena usiku watha aja? Inde, ndikuyamba kuganiza kuti, "Anga alikuti?" Muli ndi zaka zingati, Mlongo Kidd? (makumi asanu ndi atatu ndi chimodzi) Muli ndi zaka zingati, M'bale Kidd? (makumi asanu ndi atatu ndi ziwiri). Usinkhu wa zaka makumi asanu ndi atatu ndi chimodzi ndi makumi asanu ndi atatu ndi ziwiri, ndipo akugwiritsabe ntchito mapiko awo pochitapo kanthu, akupitabe.

7 Chirichonse chikalakwika ku Ohio chimene M'longo Kidd adziwa za icho, foni imalira kunyumba kwanga. Tsiku lina anandiimbira foni ndipo mwana wamng'ono (kamwana kakakazi, ine ndikukhulupirira anali) kanabadwa, ndipo matumbo ake anali kunjwa kwa iko_chikhodzozo chinali kunjwa kwa mwanayo. Ndipo dokotala sankadziwa choti achite za icho, ndipo iye ankachita mantha kuti achite opereshoni. Ife tinapemphera^[Mlongo Kidd akamba nkhanayo mu msonkhanowo_Mkonzi]^kubwezeretsa matumbowo mkati mwa opereshoni ndipo ankaganiza kuti sakhala moyo; ndipo anakhala moyo_opanda bowo nthawi imeneyo, ku matako ake pomwe chakudya chikanati chiziturukira. Mlongo Kidd anandiimbiranso, ife tinapempheranso, ndipo tsopano iye ali ndi bowo labwinobwino. Ndi uyu apa monga mboni, dokotala nayenso. Ndi umboni kuti Ambuye Yesu, Mlengi wopambana^ mukuona zimene Satana amayesa kuchita? Kudula moyo wa kamwanako. Ndiyeno, onanino, ine ndikukhulupirira mayiyo anabwerera, anabwera kwa Ambuye. Mlongo Kidd anamutsogolera mayi ameneyo kubwerera kwa Khristu, chozizwitsa chachikuluchi chitachitika kwa mwana wake.

8 Ine ndinali ndi kuyitana kochokera ku California dzulo, M'bale wamng'ono wotumikira kumeneko amene ine ndinali naye koyamba pamene ndinapita ku California zaka zapitazo, muzukulu wake wamwamuna anabadwa ndi zinai^modzera magazi mutatu mu mtima wake mutatsekeka. Ndipo ine ndinamuwuza iye za nkhanu iyi. Ndipo ine ndinati, "Mulungu amene angalenge zinazi nazikonza, akhoza kuchiza ndithu muzukulu wanuyo." Ingomuwuzani mnyamatayo akhale wa kulimbika kwabwino. Ndipo mnyamatayo anali kusonkhana pamene ine ndinali ku California koyamba_pafupi zaka khumi zisanu ndi zitatatu zapitazo tsopano^zaka khumi zisanu ndi chimodzi, zakhala_ndipo ine ndinali ku California, ndipo iye^msonkhanowo unamukopa kwambiri m'nyamatayo mpaka pamene analandira mwana ndipo atabadwa, iwo anawona kuti chinachake chinali cholakwika_ iye amalefuka, ndipo iwo anayesa kumupopera mpweya mkati mwake ndi zina zotero, ndipo sizima^oneka ngati akhala ndi moyo, ndipo madokotala anamuyesa napeza kuti mitsempha itatu inali yotsekeka mu mtima wake_opanda malo otseguka konse, onani_msempha umodzi wokha ndiwo womwe umapopa, ndipo iye anawayitana abambo ake, nati, "Bambo, muyitaneni M'bale Branham nthawi yomwe ino. Mumuwuze iye, 'Ingopemphani kwa Khristu; Iye achita izo.'" Ndi choncho. O, mai. Ndicho chikopa_zomwe iwo anaziwona. Onani, zomwe zinanenedwa usiku watha: Chinthu choyenera pa nthawi yoyenera.

9 Chabwino, ife tizingopitirira kulankhula ndi kusalowa mu phunziro, sichoncho? Ziri ngati uchi mmawa wozizira_kungokandapala monga momwe zingakhalire, inu mukudziwa, ndipo zonse zimangomamatirana limodzi. Ndife okondwa pokhala ndi chiyanjano monga icho. Inde, bwana.

Koteru tsopano, tiyeni tidzikhaliitse chete tsopano ndi kufika ku phunziro. Tsopano, ine kupita^mwina^Ine sindikudziwa ngati mungawone izo kapena ayi pa bolodi lakudali. Mwina ngati ndidakatembenuza icho mmwamba chotero mwa kanthawi, bwanji, ife tikhoza [M'bale Branham ayitanitsa bolodi lakuda_Mkonzi].

10 Tsopano, pamene iwo akukonzekera izo^Ine ndikuyamba mochedwa mmawa uno^Ayi, ayi, ndafulumira pafupi maminiti khumi ndi asanu, kotero ndiye ife tingotenga nthawi yathu tsopano, chifukwa ife sitikufuna kukhala mu changu. Tsopano, pamene ukhala mu changu, ndiye umangowononga zinthu zimene umati ulankhule. Tsopano, ine ndimamvera tepi tsiku lina, monga momwe ine ndinakuwuzirani inu, ndipo ine ndinadzimvera manyazi ndekha_osati pa zomwe ine ndimanena koma momwe ine ndimazinenera izo_kufulumira kwambiri. Mawu a wamanjenje. Ine ndikuwona ngati ndidikire^

11 Ine ndinangowona tsiku lina komwe iwo amafuna kuti amangeko malo aakulu okawonerako zinyama, kuno mkati mwa Louisville, ndipo Bambo Brown (ine ndikukhulupirira) anali kumeneko anapereka \$1,000,000 za malo okawonerako zinyamawo. Chabwino, ngati ine ndikanakhala nazo, ine ndikanawapatsa mwina izo kuti azimasule nyamazo. Ine sindikhulupirira zoyika mukhola china chirichonse chotero. Ine ndimango^Ine ndinafika ku malo okawonerako nyama ndi kuziwona izo zinyama zosawukazo_zimbalangondo ndi mikango ndi zinthu zikungoyenda chobwerera ndi patsogolo, ukayidi kwa moyo, mukuona. Zimakuchititsa iwe kumva kuyipa. Pakutibe, izo zinagwidwa ndi luntha la munthu amene ali wochenjera momwe izo ziri. Onani, ndipo iwo amazigwira izo naziyika mu nsinga.

Tsopano, ine ndikuganiza za, mdierekezi amachita izo. Iye amatenga anthu ofunika, amene akanamayendayenda mmalo opambana a Mulungu, mminda, ndi zinthu zotero, ndiyeno kumuyika iye mu nyumba ya ndende ya chipembedzo china, kapena chikhulupiriro china, kapena chinthu china, ndi kumumangirira iye mmenemo; chiri chinthu chonyansa chotani.

Ndipo ine sindimakonda malo okawonerako nyama. Koma ine ndimamva chinachake ngati mmodzi wa zinyama izo, pamene inu nonse muli mmakola ndipo inu mukuyesa kuti mumasuke, inu mukudziwa, kuti mutuluke muzikachita chinachake.

12 Tsopano, ife tisanayandikire Mawu, tiyeni tiyandikire Mlembi wa Mawu pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, tsopano, mwa pemphero.

Atate athu achisomo a Kumwamba, ife tasonkhana mmawa unonso mu Dzina la Ambuye Yesu, Mwana Wanu wofunika_Mulungu mu thupi, anadza ku dziko lapansi kudzatichotsera machimo athu nafa_wolungama_kuti ife mwa kulungama Kwake, pokhala osalungama tikhoza kukhalitsidwa angwiro mwa Iye. Ife tikudza kulapa kuti ndife osayenera, Ambuye.

Palibe kanthu kabwino pa ife. Ndipo ife tonse tiri mu nyumba imodzi yandende yaikulu. Ngakhale ife tiyime pa ngodya iti, ife tiri mundende tonse basi. Wina sangathandize mzake. Koma Mulungu, mwa chifundo Chake chopanda malire, anatsika nadzatsegula zitseko za ndende kuti atimasule ife. Ife sitiri mu kholabe tsopano. Ife sitiri kowonera zinyama za m'dziko, koma tsopano ndife mfulu; ife tiri kunja.

13 O, momwe ife timamukondera Iye ndi kumutamanda Iye! Momwe ife tingayende kupyola mminda yaikulu ya malonjezo Ake ndi kuwawona iwo akukwaniritsika pamaso pathu ndi mwa maso athu omwe; kuwona Mulungu wamkulu wa Muyaya akudziwulula Yekha pamaso pathu, ndi kudzipanga Yekha weniweni monga momwe anachitira kwa aneneri akale; podziwa izi: kuti iwo akupuma ndi chitsimikizo kuti tsiku lina ife tidzabwezeretsedwanso pamene moyo uwu udzatha ndi chiwukitsiro, kupita ku Moyo Wamuyaya umene siudzazirara. Matupi athu sadzakalamba, ndipo ife sitidzafa. Ndipo ife sitidzamva konse njala, ndipo ife sitidzakhala ndi chosowa konse. Koma ife tidzayenda ndi Iye. Ife tikufuna kumumva Iye akuti, "Lowa mkati ku zisangalalo za Ambuye zimene zinakonzedwera iwe chikhazikire maziko a dziko." Kale tchimo lisanalowemo, momwe Iye kukonza kutapangidwa, monga kwa Adamu ndi Eva, kuti iwo asadzadwale konse, kapena kukhala ndi vuto. Ndipo tsopano Iye wakonzera izo kwa ife, ndipo Iye amadziwiratu kuti ife timadza. Tchimo linapanga chotchinga chachikulu, ndipo tsopano tchimo lachotsedwa ndi Magazi a Yesu. Tsopano, ife tiri pa ulendo wa ku Dziko Lolonjzedwa mwa lonjezo la Mulungu, amene ali Wamuyaya.

14 Tidalitseni ife tsopano, Atate, pamene ife tikuphunzira Mawu Anu. Ife tikufuna kudziwa tikhale anthu a mtundu wanji kuti ife tidzakhalepo kumeneko. Tithandizeni ife lero mu sukulu iyi kuti ife tikhoze kukhala ndi Mphunzitsi Wamkulu wopambana pakati pathu_Mzimu Woyera amene akanabwera ndi kudzadziwulula Yekha kwa ife mwa Mawu Ake. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake ndi kwa ulemerero Wake. Amen.

15 Tsopano, choyamba ine ndikufuna kuti inu mutsegule nane ku II Petro mutu wa 1, ndipo ine ndikufuna kuwerenga gawo la Lemba ili: II Petro mutu wa 1. Ndipo tsopano kwa inu amene muli ndi mapensulo anu ndi mapepala, ndipo ine ndikukhulupirira kuti ndinawuzidwa mmawawu kuti nthawi zina, ndikapotoloza mutu wanga kuchokera uko, sizimamveka bwino pa tepi. Ine sindimatanthawuza kuti ndichite zimenezo, ndipo ine ndikukhulupirira nthawi zina ngati ife tikanaganizira zokhala ndi maikolofoni a paliponse atapachikidwa mu dengali apa^ngakhale uyime pati ndiye, iwe uzikhala bwino^zizikhala zangwiro paliponse basi. Maikolofoni ongokhala mmwamba mudengali.

16 Ndipo tsopano monga^pamene ine ndikulankhula, ndipo ngati inu pakutha pa msonkhanowu kapena mukufuna kutero, mukhoza kukopela, chomwe ndajambula apachi, ndipo inenso ndachitayipitsa kuno. Ine nditenga chomangira ndi kuchiyika patsogolopa, ngati inu mungafune kuchita izo nthawi yina. Mubwere

mofulumirirapo madzulo ano_kotero kuti ife tikhoze kumvetsa.

17 Tsopano, ife tikuyandikira Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Ife tangotsiriza kumene Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo, ndipo uwu ndi Uthenga wophunzitsa umene ukumangiriza munthu amene anati adzawomboledwe mwa mwazi wa Ambuye Yesu, ndipo adzakhala mu M'badwo wa Mpingo umenewo_M'badwo wa Mpingo wa Muyaya umenewo pamapeto a Zisindikizo. Tsopano, ife tikudziwa kuti ife tiri ndi Malipenga Asanu ndi awiri, Miliri Isanu ndi iwiri, Mbale, ndi zina zotero, zimene ife tilowamo pamene ife tikupitirira, koma ife tikudikira malo ochuluka kuti anthu akhoza kukhala.

Tsopano, ndipo ine ndinaganiza izi zikanamangiriza mmenemo pomwe ine ndimayembekezera chabe^ine sindimayembekezera kujambula choyimira chakechi, koma tsiku lina ine ndinali ndi amzanga ofunika kwa ine_a Cox komwe mu Kentucky. Ine ndinapita uko, ndimaganiza kuti ine ndingakalowemo tsiku lina limodzi kukasaka agologolo nyengo yosaka isanatsekedwe. Ndipo ine ndinali mu nkhalango ndi mzanga, Charlie amene wayima apo, ndi Rodney, m'bale wake, ndipo ine sindinawone ngakhale gologolo. Ine ndikuganiza ine ndinawawopsyezera iwo kutali, pamene ine ndinayamba kufuula mu nkhalangomo. Izi ndi zomwe zinadza kwa ine, anyamata, ndi Mlango Nellie ndi Margie, pamene ine ndinakuwuzani kuti ndidzakuuzani inu Lamlungu pamene ine ndidzafika pa izo. Izo ndi zomwe zinadza kwa ine pa Uthenga womwe ndimati ine ndidzalankhulepo, ndi momwe zina zonsezo zinamangirizira kwa izo. Ndipo, o, ine ndinakhala ngati ndinali ndi weniweni Mzimu weniweni wa kufuula mu nkhalango umo.

18 Kotero tsopano, tiyeni tiwerenge tsopano pa 1 Petro, II Petro kani, mutu wa 1, (gawo lake.)

“Simoni Petro, wantchito ndi mtumwi wa Yesu Khristu, kwa iwo amene alandira chikhulupiriro chopambana chomwechi ndi ife kupyolera mu chilungamo cha Mulungu ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu:”

Ine ndikukonda momwe zafotokozeredwa pamenepo, chifukwa phunziro langa lonse mmawa uno liri pa maziko a CHIKHULUPIRIRO, onani. Ndiroleni ine ndiwerengenso izo; mvetserani mwacheru.

“Simoni Petro, wantchito ndi mtumwi wa Yesu Khristu, kwa iwo amene alandira chikhulupiriro chopambana chomwechi^kupyolera mu chilungamo cha Mulungu ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu:”

Zindikirani: Iye akuti, “Ine ndalandira chikhulupiriro ichi, ndipo ine ndikulemba izi kwa iwo amene alandira chikhulupiriro chopambana chomwechi.” Ine ndikufuna^izi si za kwa dziko la kunja; izi ndi kwa Mpingo_iwo amene ali mwa Khristu.

“Chisomo ndi mtendere zichulukitsidwire kwa inu kupyolera mu chidziwitso cha Mulungu, ndi cha Yesu (Khristu) Ambuye wathu,

Monga momwe mphamvu zake za umulungu zatipatsa ife zinthu zonse (mphamvu Yake ya umulungu tsopano yatipatsa ife zinthu ZONSE) zokhudza ku moyo ndi umulungu, kupyolera mu chidziwitso cha iye amene wayitanira ife ku ulemberero ndi mphamvu:

Pamene ife tapatsidwa kwa_kupatsidwa kwa ife malonjezo aakulu ndi opambana: kuti mwa iwowa (malonjezo amenewa) ife tikhoze kukhala ogawana nawo khalidwe la umulungu,^”

19 Tsopano, lolani izo zilowerere mwakuya kwenikweni tsopano. Sikulalikira mmawa uno; ife tikungophunzitsa phunziro ili khalidwe la Umulungu. Dikirani ine ndiwerenge ndime ya 4 kachiwiri tsopano, kuti inu musaphonye izi:

“Pomwe [ife] tapatsidwa^”pomwe kwapatsidwa kwa ife ochuluka malonjezo aakulu ndi opambana: kuti mwa iwowa (malonjezo amenewa) ife tikhoze kukhala ogawana nawo khalidwe la umulungu, titathawa chivundi chimene chiri mu dziko kupyolera mu chilakolako.”

Onani dziko_ife tathawa izo tsopano. Iye akulemba izi kwa Mpingo. Ndicho chifukwa chomwe ife tiri pano mmawa uno kuti tipeze njira ndi yiti; Zofunikira za Mulungu ndi ziti? Palibe munthu mkati muno amene amakonda Mulungu, koma amene afuna kukhala mochuluka monga Khristu_tsopano, zayalidwa apa_Mkristu aliyense. Ine ndi wankhondo wakale. Taonani M'bale ndi Mlango Kidd apa; ndipo iwo mwina ndi okalamba zedi mnyumbayi. Koma ngati ine nditawafunsa iwo, “Chokhumba cha miyoyo yanu ndi chiyani?” Zingakhale: “Pafupi ndi Mulungu.” Pamene inu muphunzira za Khristu, pali china chake chokhudza Iye chomwe chiri chokonda chotero, iwe umangoyesetsa kulowa mpaka mwa Iye.

20 Pepani kulankhula uku: Ine ndinamuwuza mkazi wanga kuno osati kale ayi (nayenso akukalamba ndipo^) Ine ndinati kwa iye. Ine ndinati, “Kodi iwe umandikonda ine monga unkachitira muja?”

Iye anati, “Ine ndithudi ndikutero.”

Ndipo ine ndinati, “Iwe ukudziwa, ine ndimakukonda iwe kwambiri mpaka ine ndikanakonda nditakutenga iwe kukukokera iwe mkati mwanga, kotero kuti ife tikanangokhala mmodzi weniweni.” Tsopano izo^muchulukitse izo kwa mamiliyoni mazana, ndiyeno inu mupeza momwe okhulupirira, amene

anagwera mchikondi ndi Khristu, amafuna kulowa mwa Iye, chifukwa ndi chikondi; ndipo apa Iye atiwonetsa ife momwe kupyolera mu malonjezo awa ife tingakhalire ogawana nawo Chikhalidwe cha Umulungu cha Khristu. Matupi achivundiwa_momwe ife tingakhalire ogawana nawo.

21 Ine ndikhoza kunena china chake pano. Chifukwa ine ndimakhulupira^Tsopano wina anandimvetsa ine molakwika kuno osatinso kale. Ine ndinalandira kalata kuchokera ku Ministerial Association imene inati kuti ine ndimakhulupirira kuti panali_ife tinali okwatirana m'moyo, ndipo ife tiwasiye amene tiri nawo ngati ife sitiri okwatirana m'moyo kwa iwo, kuti ife tikakwatire ena amene ife tiri okwatirana m'moyo kwa iwo. O, mai! Ine ndinati, "Ine ndiribe mulandu kwa zopeka ngati zimenezo." Ine ndakhala wotsutsa zimenezo nthawi zonse. Ine sindimakhulupirira mwa izo. Ndithudi ayi. Ine ndimakhulupirira kuti ndi Mulungu amatipatsa ife okwatirana nawo. Izo nzowona. Ndiyeno ife timakhala gawo la wina kwanzake. Izo nzolondola, ndipo mwamuna asanakwatire, iye ayenera kuganizira zinthu izi bwino; kuzimvetsa izo.

22 Mnyamata Wamng'ono anandifunsa ine tsiku lina, anati, "Kodi inu mukuganiza kuti ine ndikhoza^ndiyenera kukwatira, M'bale Branham, msungwana wakutiwakuti?"

Ine ndinati, "Iwe umaganiza motani za iye?" Iye anati, "O mai, ine ndimangomukonda iye."

Ine ndinati, "Chabwino, ngati iwe sungathe kukhala wopanda iye, kuli bwino iwe kuti umukwatire iye ndiye. Koma ngati iwe ungate kukhala wopanda iye, iwe kuli bwino usatero. Koma ngati ziti zikuphe iwe, kulibwino iwe upitirire ndi kukwatirana." Ndipo kotero chomwe ine ndimayesa kumuwuza iye ndi ichi: kuti ngati iwe umamukonda iye kwambiri^Tsopano, pakali pano inu musanakwatirane zonse ziri bwino ndi mokoma, koma inu mukakwatirana ndiye zovutikira ndi mayesero a moyo amalowamo. Apo ndi pamene inu muyenera kukhala mu chikondi kwambiri kuti inu muzimvetsana wina ndi mzake. Pamene iwe ukhumudwa naye, kapena iye akakhumudwa nawe, inu mumakhozabe kumvetsana wina ndi mzake.

23 Umo ndi momwe ziriri ndi Khristu. Onani, ife tiyenera kukhala mu chikondi ndi Iye kwambiri mpaka pamene ife tipempha chinthu chinachake, ndipo Iye satipatsa ife icho, izo sizimatigwedeza ife pang'ono. Mwaona. Mwaona, bwanji? Ndipo njira yokha yomwe inu mungachitire izo ndi kuti mungakhale ogawana naye Khalidwe Lake la Umulungu, ndiye inu mumvetsa chifukwa chomwe Iye sangakupatseni inu_ogawana nawo Khalidwe Lake la Umulungu. Ndiye yang'anani kuno: "mutathawa chivundi chomwe chiri mu dziko kupyolera mu chilakolako"_utachithawa icho. Onani kuti ndi kwandani. Ndi kwa Mpingo. Iwo amene ali mwa Khristu akwezedwa pamwamba pa zinthu izi. Osati kuti iye anadzikweza yekha, koma Khristu anamkweza iye pamwamba.

24 Kwa abale anga achikuda ndi alongo amene mulipo pano mmawa uno^Ine sindikutanthawuza izi kuti ziwononge kalikonse, koma ife tinali mu msonkhano nthawi yapitayo, ine sindikudziwa ngati ine ndinazilankhulapo mu Kachisi; ine ndinazilankhula ku malo ambiri. Panali mlongo wachikuda amene anati, "Kodi ine ndingaperekere umboni, kapena kuchitira umboni?"

"Zedi, Mlongo, pitirirani."

Iye anati, "Ine ndikufuna kuchita umboni uwu mwa ulemmerero kwa Mulungu."

Iye anati, "Inu mukudziwa, ine sindiri chomwe ine ndiyenera kukhala;" ndipo iye anati, "ine sindiri chomwe ine ndikufuna kukhala, koma" iye anati, "chinthu chimodzi zedi, ine sindiri chomwe ine ndinali poyamba."

25 Onani, iye anachokera kwinakwake; iye anali atakwezedwa pamwamba. Ndi momwe ife timadziwira kuti tachoka ku imfa kufika ku Moyo. Ife timayang'ana mmbuyo ku dzenje kumene ife tinakumbidwa. Onani, ife sitiri chomwe ife tikufuna kukhala; ife sitiri ngakhale chomwe ife tiyenera kukhala; koma chinthu chimodzi chomwe ife tikuthokozera ndi kuti ife sitiri chomwe tinali poyamba. Ife tiri pa msewu; ndipo "titathawa chivundi cha mdziko"_titathawa izo_zilakolako ndi chivundi cha mdziko. Inu muli pamwamba pa izo.

26 Tsopano, uwo tsopano uwo ndi mtundu wa munthu amene Iye akulankhula naye_munthu amene wathawa zinthu izi_ mwaona, chivundi cha mdziko.

"Ndipo kuwonjezera pa ichi, pokhala ndi changu chonse, onjezerani kwa chikhulupiriro chanu mphamvu; ndi kwa mphamvu chidziwitso;

Ndi kwa chidziwitso chodziletsa; ndi kwa chodziletsa chipiriro; ndi kwa chipiriro umulungu;

Ndipo kwa umulungu chikondi cha pa abale; ndi kwa chikondi cha pa abale, chikondi."

27 Tsopano, Iye watipatsa ife dongosolo lake apa zoti nkuchita; kudziwa momwe ungachitire. Tsopano, monga ine ndinanena, ife tonse tikuyesetsa kudza pafupi kwa Mulungu. Ndicho chifukwa ine ndasankhira uthenga uwu mmawa uno kwa mpingo, podziwa kuti anthu akuyendera^Usiku watha ine ndinati, "Ndi angati muno akunja kwa mzinda." Pafupi 98 pa zana la anthu ochokera kunja kwa mzinda. "Ndi angati ali pano akuchochera mailosi zana?" Motani, anapitirira, ndiganiza, 80 pa zana. "Ndi angati ali muno ochokera

kupyola mailosi mazana asanu?" Ndipo pafupi limodzi la magawo atatu a anthu anali kuno ochokera kopitirira zana^mailosi mazana asanu kutali. Ganizani za izo. Za anthu kuyenda. Chabwino, anthu awo samangobwera ku tchalitchi chotero kuti adzangowonedwa. Palibe^ndi zimene anthu a mdziko akunja akanawona kukongola kulikonse pa malo ano. Iwo onse ndi anthu wamba, osawuka, ovala mwawamba. Palibe nyimbo yafuko yotchuka yochokera kwa ena onyengezera kukhala kwayala ya angelo, limba wa mapaipe, ndi magalasi a mazenera ojambulidwa. Inu mumakhala ndi nthawi yovuta kukhala pa mabenchi ndi kuyima cha pa makoma onse. Iwo samabwera chifukwa cha za ngati izo, koma iwo amadza chifukwa mkati mwa iwo muli chinachake chimene chikuwona kukongola kumene diso lachibadwa silimawona. Ndi diso lauzimu limene limagwira kukongola kwa Khristu. Ndicho chifukwa chomwe iwo amadza.

28 Kotero, kwa masiku ife tisanakhale ndi msonkhano, ine ndimapemphera mosalekeza. Kupita ku nkhalango, kutenga mu thumba langa^Kumuwuza mkazi wanga, "Ine ndikupita kukasaka agologolo mmawa uno." Ndipo ine ndimayika pensulo ndi mapepala mu thumba langa. Pamene kukangoyamba kuwala kokwanira kuti uziwona, ine ndikhala chotsamira mtengo kwinakwake, manja atawakwera mmwamba, ndi kunena, "Ambuye, ndingachite chiyani ine lero? Mundipatsa ine chiyani inu cha kwa ana Anu?"

Ndiye pamene ine ndikhudza chinachake chimene chikuwoneka kuti chikuyaka mkati, kumadza chinachake monga ichi. Pamene Kukhalapo Kwake kufika pafupi, ine ndimayamba kumva chinachake chomvekera kutali ndithu, chinachake mwa dongosolo ili. "Ziwiri^ndi^ziwiri^ zipanga^zinayi." Kuyandikira, "Ziwiri ndi ziwiri zipanga zinayi. Ziwiri ndi ziwiri zipanga zinayi. Ziwiri ndi ziwiri zipanga zinayi." [M'bale Branham analankhula kubwereza kulikonse mofulumirirako_Mkonzi] Kupitiriza, kupitiriza, kupitiriza, chotero. Kumeneko ndiko Kukhalapo Kwake kukubwera mkati.

29 Dzipereke wekha, ndipo pakapita kanthawi umachoka mu umwini wako. Pamenepo pamadza masomphenya: "Pita kumalo akuti ndi akuti ndi chinthu chakuti chakuti." Mwaona, zimayambira pa kulingalira, malingaliro ako pa Mulungu, kuchoka mu dziko, kutali ndi dziko kukutali mu chipululu, kwa wekha. Ndipo chimayamba kudza, "Chimodzi_chimodzi^" Ine nditi^nambala iliyonse kapena chirichonse, chinachake basi chimayamba pang'ono- pang'ono, mosamveka kubwera mkati. Ndiye chimadza mofulumira fulumira. Iwe umakhala pamenepo ndi kukweza mmwamba manja ako; osalankhula liwu, ingokweza manja ako mmwamba. Chinthu choyamba iwe ukudziwa, thunthu lako lonse ligwidwira kutali. Ndiye iwe umawona zinthu zomwe Iye akufuna iwe kuti udziwe_kukuwonetsa iwe zinthu zomwe ziti zidze. Nthawi zina zimafika pamalo mpaka pa malo ena, ndiye zimaleka. Sizimapita mu masomphenya. Ndiye Malemba amangotsanuliridwa pamodzi. Ine ndimatenga cholemba changa, kotero kuti ine ndisayiware izo, ndi kuzilemba izo apo. Kuzilemba izo apo, ndipo ine ndimabwera kunyumba ndi kudzazifufuza, ndi kuziwerenga; ndipo nthawi zina, izo sizimakhala zomveka kwa ine pamene ndikuzifufuza, ndiye pakapita nthawi izi ziri apazi; izo zimangondikhudziratu, ndi kubwerezanso! Ndiye ine ndimatenga kabukhu kakang'ono ngati aka ndi kungoyamba kujambula momwe ine ndingathere, zomwe Iye andiwa ine. Ine ndinaganiza, "Ambuye, ine ndikupita ku Kachisi kukawauza iwo, 'Bwerani kuno,' ine ndiri ndi chinachake kwa iwo." Umo ndi momwe zimadzera. Momwemo. Mpakana poyamba Iye apereke icho kwa ine, ine sindingathe kuzipereka izo.

Koteroni pa zoyambula zazing'onozi, zimene inu mukuona ine ndikuyang'anapo; ndipo izi poyamba ine ndinayamba, ine sindinapeze gawo ili apa, mpaka pafupi chabe tsiku kapena awiri apitawo uko ku nkhalango.

30 Tsopano, anthu awa ali^Petro akuti apa momwe ife tiyenera kukhala ogawana nawo khalidwe Lake Laumulungu. Tsopano, aliyense wa ife akuyesa kukula kumka mu thunthu la Mulungu.

Tsopano, ife titatha kutsiriza Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri ndiye pa nthawi imeneyo ya kuliza kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, kapena kumasula_chifukwa ife tikudziwa chomwe Chisindikizo chiri; ndiko kumasula utumiki_kumasula Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Ndipo tiziwona bwino izo pamene ndajambulapa. Ndiko kumasula uthenga_chinachake chimene chasindikizidwa.

31 Lamulungu lathali usiku ndinalalikira pa, Fungulo, ndipo fungulo ndi chikhulupiriro. Chikhulupiriro chimagwira fungulo, ndipo fungulo ndi Malemba, ndipo Khristu ndi

Khomo. Mukuona. Kotero chikhulupiriro chimatenga zinthu zazing'ono zomangirizana mu Malemba ndi kutsegulira kunja ulemere ndi ubwino wa Mulungu kwa Anthu Ake. Kotero chikhulupiriro chimagwira fungulo limene limatsegula Khristu kwa anthu. Kutsegula izo; kuwulula Izo.

Kotero lero ife tiyesa kutenga fungulo lomwelo kuti titsegule njira yokhalira Mkhristu wa mphamvu mu thunthu la Mulungu, ndi kukhala Kachisi Wamoyo wa Mulungu Wamoyo kuti azikhalamo. Kumbukirani, Mulungu amadziwulula Yekha mu njira zitatatu. Nthawi yoyamba Iye anadziwulula Yekha mu Lawi la Moto. Icho chinkatchedwa, Utate. Ndiye Mulungu yemweyo anawonekera mwa Yesu Khristu. Pamene Iye anamanga thupi_analipanga thupi ili. Kachitatu, kupyolera mu kufa kwa thupi limenelo, Iye anayeretsa Mpingo womwe Iye angakhalemo. Uyo anali Mulungu pamwamba pathu; Mulungu nafe; Mulungu mwa ife_Mulungu yemweyo.

Ndicho chifukwa anatchedwa Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Osati a Mulungu atatu_maudindo atatu a Mulungu mmodzi. Ngati iwo akanangoganiza za izo ku Nicene Council, sibwenzi ife titakhala mu chisokonezeko chonsechi, sichoncho? Ndi zowona. Osati amulungu atatu.

32 Anthu sakanakhoza kumvetsa momwe Yesu ankalankhula kwa Atate, ndipo Iye ndi Atate ali mmodzi. Chabwino, uko ndi komwe chinthu chonsechi chiri. Zedi, kungozimasula izo, ndithudi. Onani, si amulungu atatu_maudindo atatu. Ndi chiyani? Mulungu kudzichepetsa kwa chirengedwe Chake. Mulungu akufuna kuti azipembedzedwa. Liwu loti Mulungu limatanthawuza chinthu chopembedzedwa. Ndipo ndi Mulungu kuyesa kuwafikitsa anthu Ake pa khalidwe lakuti Iye azikhoza kulandira kuchokera kwa iwo chomwe Iye anawalengera.

Iye sanakupangeni inu kuti mukhale chinthu chinachake pambali pa mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu. Ngati inu mwaphonya icho, (cha kukhala mwana wamwamuna kapena wamkazi wa Mulungu) inu mwaphonya malo oyenera. Ndipo kuphonya^Liwu loti T-C-H-I-M-O limatanthawuza kuphonya malo oyenera. Kuphonya malo oyenera. Ndiye, ngati ine ndikuwombela pa chandamale, kukhomera chizindikiro pa mtunda wa mapazi makumi asanu, ndipo ine nkuwombera, kutenga mfuti yanga ndi kuwombera, ndipo ine nkuchiphonya icho mainchesi anayi kapena asanu, chachitika ndi chiyani?

Mfuti yanga ikusowa kuyikonza. Pali china cholakwika. Ndipo ngati ine ndiphonya chikhulupiriro mwa Mulungu, ngati ine ndiphonya kukhala Mkristu^Mulungu anakusiyani inu pano kuti mukhale Mkristu, ndipo ngati inu muthawira kumbali yina_bwererani nimukonzedwe bwino. Ndipo pali chinthu chimodzi chokha chomwe chingakukonzeni inu, ndicho Malemba. Mzimu Woyera mu Malemba umakukonzani inu. Kukufikitsani inu molunjika pa chandamalenso.

33 Tsopano ife, tiphunzira Mawu Ake.

Stefano anati pa Machitidwe 7 ndiponso mu^Tiyeni tingowerenga apo. Kulankhula za^Tsopano ife tikulankhula za Kachisi wa Mulungu. Tsopano Stefano anati_pokhala kuti akhala Kachisi Wamoyo wa Mulungu Wamoyo_Stefano anati mu Machitidwe mutu wa 7, ndipo ine ndikukhulupirira mu Machitidwe 7, kuyambira cha pa ndime ya 44;

"Makolo athu anali ndi chihema cha umboni mchipululu, monga adalamulira Iye wakulankhula ndi Mose, kuti achipange ichi monga mwa chithunzi cha chomwe adachiwonacho.

Chimenenso makolo anali nacho_makolo athu amene anadza pambuyo pa icho, nalowa nacho ndi Yesu potenga dziko la amitundu amene Mulungu anawaingitsa pamaso pa makolo athu, mpaka mu masiku a Davide;

Amene anapeza chisomo pamaso pa Mulungu, nakhumba kuti ampezere kachisi Mulungu wa Yakobo.

Koma Solomoni anammangira Iye nyumba.

Komabe Wammwambambayobayo sakhala mu nyumba zomangidwa ndi manja; monga mneneri anena,

Kumwamba ndi mpando wachifumu wanga ndipo dziko lapansi ndi chopondapo mapazi anga: Mudzandimangira nyumba yotani? Ati Ambuye: kapena malo a mpumulo wanga ndi otani?"

34 Tsopano, mu Kachisi, ndithudi ndi malo amene ife timapita kukapuma, tsopano, kupeza chitsitsimutso, ndi zina zotero, monga kupuma kwa kugona, ndi zina zotero. Tsopano, Ahebri 10, ndipo ndime ya 5, Paulo akubweretsamo ichi.

"Mwa ichi polowa mu dziko, anena, Nsembe" (ameneyo ndi Khristu) "Nsembe ndi chopereka inu simunazifuna, koma thupi Inu munandikonzera Ine:"

Kachisi ndi chiyani tsopano? Thupi. Mulungu mu kachisi wa thupi.

Mulungu amafuna^mmwamba umo, pamene Iye atsikira pa phiri, ngakhale ng'ombe yaimuna kapena yaikazi ikakhuza phirilo, iyenera kuphedwa Mulungu ndi Woyera.

Usiku watha pamene angelo aja anaphimba nkhope zawo_ Aserafi oyera okhala ndi nkhope za chiyero_sadziwa ngakhale chomwe tchimo limatanthawuza, ndipo iwo ayenera kuphimba nkhope zawo pamaso pa Mulungu_kuphimba mapazi awo mwa kudzichepetsa.

Tsopano, Mulungu Woyera sangalekerere tchimo. Kotero palibe chomwe chikanakhudza phiri pamene Mulungu anali. Ndiye Mulungu anapangidwa thupi nadzakhala pakati pathu mwa maonekedwe a Yesu Khristu, Mwana Wake_wolengedwa Wake. Ndiye Mwana ameneyo anapereka Moyo Wake, ndipo khungu la Magazi a Mulungu linaswedwa kuti Moyo ukhoze kutulukamo mu Magazi, kwa ife. Kupyolera mu Magazi amenewo ife tayeretsedwa. Ndipo tsopano magazi athu, moyo wathu, umene unadza mwa kukhala kupyolera mu kukhumba kwa kugonana, kunabweretsa moyo wathu mdziko. Magazi a Yesu Khristu amatiyeretsa ife, amasintha khalidwe lathu potumiza pa ife Mzimu Woyera; ndiye ife timakhala mu

khalidwe laumulungu la Mulungu; ndiye ife timasandulika malo okhalamo Mulungu.

35 Yesu anati, "Pa tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate, ndipo Atate ali mwa Ine; Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine." Kudziwa momwe Mulungu aliri mu Mpingo Wake.

Mpingo tsopano ukuyenera kumatenga malo a Khristu_ kupitiriza utumiki Wake. "Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndichita iye adzazichitanso. Pakangopita kanthawi ndipo dziko silidzandiwonanso Ine konse; koma inu mudzandiwona Ine pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu mpakana kumapeto a dziko." Ndi zimenezo kupitiriza ntchito Yake.

36 Tsopano Mulungu^Baibulo linati apa, kuti Stefano analankhula za Solomoni kumanga kachisi, ndipo Wammwambamwamba samakhala mu makachisi omangidwa ndi manja. Pakuti "Kumwamba ndi mpando wachifumu Wanga ndipo dziko lapansi ndi choponderapo phazi Langa. Ndipo malo a mpumulo Anga alikuti? Koma thupi Inu mwandikonzera Ine." Amen! Ndi zimenezotu. "Thupi Inu mwandikonzera Ine."

Mulungu amakhala mu thunthu la munthu; kudzinyezimiritsa Iyemwini mu chinthu chimenecho_ kupembedza kwangwiro. Mulungu mwa ife, kukhala Kachisi Wake; Mulungu kuwonekera. O, momwe ife tikanakhoza kukhala apo mpaka kuti inu mukanangotsala pang'ono kukomoka ndi kutentha.

37 Zindikirani, kuti Mulungu wakhala kawirikawiri, kwa nthawi zonse, akudzinyezimiritsa Iyeyekha mwa munthu. Uja anali Mulungu mwa Mose; muyang'aneni iye. Anabadwa mtsogoleri; Khristu_mu nthawi imene iye anabadwa kunali kuphedwa kwa ana poyesa kumupeza iye_mofanana zinali ndi Khristu. Ndipo iye ana^iye anawomboledwa mu nthawi imeneyo; momwenso anali Khristu. Iye anali wopereka lamulo; momwenso anali Khristu. Mose anakwera pamwamba masiku makumi anayi, natenga Malamulo, nabwerako; Khristu anapita ku chipululu masiku makumi anayi, nabwererako, nati, "Inu munamva kalelo kuti 'Musachite chigololo' koma Ine nditi kwa inu, 'Aliyense amene angayang'ane pa mkazi namukhumbira iye, wachita naye kale chigololo!'" Zinthu zosiyana zonsezi zimene Mulungu akudzinyezimiritsiramo Iyeyekha.

38 Yang'anani pa Yosefe, anabadwa mnyamata wauzimu pakati pa gulu la abale ake. Onsewo anali anthu abwino, mbadwa zonse zija, koma pamene Yosefe anabwera iye anali wosiyana. Iye ankakhoza kuwona masomphenya, kumasulira maloto, ndipo iye anadedwa ndi abale ake chifukwa cha izo. Chifukwa cha ntchito yomwe Mulungu anamuyikira iye pansu pano kuti ayichite, abale ake anamuda iye chifukwa cha iyo, mukuona, ndipo izo zonse zinali kulozera ku mtanda. Ndipo yang'anani, iye anagulitsidwa ndi mtengo pafupi ndalama za siliva makumi atatu ndi abale ake, anaponyedwa mu dzenje kuti afe ndi abale ake, anatulutsidwa mu dzenjelo, ndipo anapita nakakhala pa dzanja lamanja la Farao, ndipo palibe munthu akanadza kwa Farao, (amene ankalamulira dziko lonse masiku amenewo) palibe amene akanadza kwa Farao pokha kudzera kwa Yosefe. Palibe munthu angadze kwa Mulungu pokha kudzera mwa Khristu. Ndipo pamene Yosefe anachoka ku nyumba yachifumu, iye asanachoke, kunali kulizidwa lipenga, ndipo othamanga anali kumtsogolera iye akufuula, "Gwadani bondo, Yosefe akudza." Ziribe kanthu komwe unali, kapena chimene unali kuchita, kapena momwe ntchito yako iliri yofunika, umagwada pa maondo ako mpaka Yosefe atakafika kumeneko. Ndipo pamene Lipenga lidzalira tsiku linali, bondo lililonse lidzagwada ndipo lirime lililonse lidzavomereza. Pamene Khristu, Yosefe wathu, adzachoka ku ulemerero nadza, ntchito yanu siidzakhala yofunikanso. Bondo lililonse lidzagwada ndi kumuvomereza Iye kuti ndi Mwana wa Mulungu. Uko nkulondola.

39 O, momwe ife tikumuwonera Iye mwa Davide. Momwe Davide, mfumu yokanidwa, wokankhidwa pa mpando wachifumu wake womwe ndi abale ake, mwana wake yemwe, anakakhala pa Phiri la Azitona, pamene iye anakwera pamwamba pa Phiri la Azitona nayang'ana mmbuyo ku Yerusalemu nalira; pakuti kumeneko anthu ake omwe amene Iye anawatumikira ndi kuwaphunzitsa iwo za Mulungu, ndipo anthu ake omwe anamutaya iye nagenda zinthu pa iye, kumulavulira iye, ndi kumunyoza. Pamene iye anayamba kukwera phiri, iye anakanidwa. O, ndi mwangwiro bwanji za Mwana wa Mulungu patatha zaka mazana asanu ndi atatu_Mfumu yokanidwa pakati pa anthu Ake omwe anakakhala pa phiri nalirira Yerusalemu, monga Mfumu yokanidwa. Chinali chiyani? Mulungu kudzinyezimiritsa Iyeyekha. Mwa aneneri aja kunyezimiritsa Khristu.

Ndiye kunadza Mmodzi amene anali ungwiro wa Mulungu. Iye anali Mulungu pakati pathu. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, iye wadzinyezimiritsa Yekha mu Mpingo Wake mbali iyi ya Golgota. Kotero, inu mukuona, ife tonse tikuyesa kufika mu malo okhalamo awa, Kachisi wa Mulungu Wamoyo.

40 Tsopano pali anthu ena amene ife tikuwazindikira apa^ Iye anati, "Poyamba ife tiri ndi chikhulupiriro, mphamvu, chidziwitso, chodziletsa, chipiriro, ubwino kapena umulungu ndi chikondi cha pa abale." Chabwino, chikondi cha paubale ndiyeno onjezerani chikondi. Lolani ine ndiwerenge izi mobwerezanso, kuti inu mutsimikize kuti muzimvetse tsopano. Tsopano, ife tiyambira pa ndime ya 5.

"Ndipo kuwonjezera kwa ichi, pokhala ndi changu chonse, onjezerani kwa chikhulupiriro chanu mphamvu: ndi kwa mphamvu chidziwitso:

Ndi kwa chidziwitso chodziletsa; ndi kwa chodziletsa chipiriro; ndi kwa chipiriro umulungu;

Ndipo kwa umulungu chikondi cha pa abale; ndi kwa chikondi cha pa abale chikondi. (Chimene chiri chikondi).

Pakuti zinthu izi zikakhala mwa inu, nizichuluka, zimakupangani inu kuti musakhale owuma kapena opanda zipatso mu chidziwitso cha Ambuye wathu Yesu Khristu."

Tsopano Petro akundandika chinachake pano kwa ife, cha momwe ife tingafikire apo.

41 Tsopano, ine ndikufuna kunena ichi: kuti pali anthu ena amene ali ndi gawo la mphamvu izi, chidziwitso, nzeru, chipiriro ndi zina zotero, amene savomereza nkomwe kukhala Akhristu. Tsopano ife tingo^Ife tikuphunzitsa Sande Sukulu, ndipo izo ndi zowona. Pali anthu amene ali ndi gawo la izi amene sanyengezera nkomwe kukhala Akhristu. Koma izi sizima_izo sizingachite icho. Ziri ngati mbalame yakuda kuyesa kuvala nthenga za pikoko mu mapiko ake kuti zimupange iye kukhala pikoko. Iye apa amangodzichititsa manyazi yekha. Kukanakhala bwino kukhala mbalame yakuda. Mukuona? Pamene iye ayesa kuchita izi asanakhale Mkristu, iye ali pa malo osayenera basi. Ziri ngati mtengo wa Nkhuyu kuyesa kupanga maapulo. Iwo siwungathe konse ngakhale uli mtengo; koma iwo siungapange maapulo.

Ziri ngati bulu kuyesa kupanga ubweya_kuyesa kukhala nkhusa pamene iye ali ubweya^ali bulu. Mukuona, iye sangapange ubweya. Iye sangathe kutero. Ubweya ndi mphatso kwa nkhusa_Osati kwa bulu. Iye angathe kuyesa kuchita ngati nkhusa, koma Iye ndi bulu basi. Mukuona. Kotero inu mukuti, "Ine ndikhoza kudya ngati nkhusa; Ine ndikhoza kuchita ichi ngati nkhusa," koma ziribe kanthu chomwe iwe ungachite, iwe uyenera kukhala nkhusa polinga kuti ukhale ndi ubweya.

42 Ndipo lolani ine ndiyime apa kwa miniti. Nkhusa siimapanga ubweya. Iyo ili ndi ubweya, chifukwa iyo ndi nkhusa. Ndipo anthu ambiri akuyesa kunena kuti, "Chabwino, ine ndiyesa kukhala wabwino. Ine ndiyesa kuchita ichi." Musapange kalikonse. Ayi, inu simungathe kuchita ichi. Nkhusa siimachita^simafunsidwa, iyo imayembekezeredwa, kuti ipange ubweya_uyo imabereka ubweya. Iyo imachita izo chifukwa ndi nkhusa. Ndipo pamene inu muli Mkristu, inu mumangobala zipatso za Mzimu. Inu simuma^inu simumapanga izo. Inu simumayesa kuzipanga izo. Inu simumadzipanga kukhala chinachake chomwe inu simuli. Inu mumangokhala chomwe inu muyenera kukhala, ndiyeno izo zimazisamalira zokha.

43 Kodi inu munawamvapo anthu akuti, "Chabwino, ine ndikukuwuzani inu, ine ndinalowa mpingo; ine kwenikweni ndiyenera kuleka bodzali." Inu mukuyesa kupanga chinachakenso, tsopano. Inu simungachite izo, kotero ndi zosasowa kuyesanso_monganso momwe bulu sangadzipangitse kukhala ndi ubweya. Iye sangathe kutero.

Kapena mwimba kuti uyese kumadya ndi nkhusa_ mwimba ukuyesa kukhala nkhusa. Kodi inu mungalingalire kuti khungubwe kunjako, kumati, "Inu mukudziwa kuti ine ndi nkhusa." Kusomeka nthenga zingapo pa iye nati, "Onani, tsopano, ine momwe ndikuwonekera^" Mwaona? Iye akhoza kuwoneka mosakhala bwino. Ameneyo ndi munthu amene akudzinenera kuti ali chinachake pamene sali. Onani, inu simungathe kuchita ichi.

Inu simunganene "Tsopano onani, ine ndikuyenera kukhala ndi mphamvu, kotero ine ndikhala ndi mphamvu. Ine ndiyenera kukhala mwaumulungu, kotero ine ndingokhala nawo." Bwanji inu mukungoyesa kusomeka nthenga, ngakhale mungathe kuzipeza, koma inu simungayike nthenga pa mbalame yolakwika. Sizigwira ntchito basi. Ndipo zikungosonyeza kuti mbalame imeneyo ndi yonyenga chotani. Mukuona?

44 Kodi inu mungalingalire khungubwe wokalamba kuyesa kukhala ndi nthenga zingapo za nkhusa namati, "Tayang'anani kuno, onani, ine ndi nkhusa." Mukuona? Ife poti tikudziwa kale kuti iye ndi khungubwe. Basi. Ife tikhoza kudziwa kuti iye ndi khungubwe.

Chabwino, tsopano umo ndi momwe kuliri poyesa kupanga Chikristu. Inu simungachite izo. Chinthu choyamba chimene inu muyenera kuchita ndi kubadwa kachiwiri. Inu muyenera kusinthidwa. Ndipo pamene inu mwasinthidwa, inu musandulika cholengedwa chatsopano. Tsopano, inu mukukhala bwino, tsopano. Tsopano, inu simumasowa kudandaula za nthenga; izo sidzisamalira zokha pamene_ pamene inu muti mubadwe kachiwiri. Inde, bwana.

Monga ine ndakhala ndikulankhula kuti: Inu mukatenga nkhumba, kuyisambitsa bwino, kuyiveka suti ya takisodi_suti ya takisido kani, ndi kuyitulutsa ipite panja; iyo ipita molunjika ku dzenje la matope ndi kukagudubuka, chifukwa inu mukuona kuti sizingayichitire chabwino chirichonse. Iyo ndi nkhumba_ilo ndi khalidwe lake. Kugubuduka ndi khalidwe lake. Inu muyenera kuyisinthira khalidwe lakelo, ndipo zina zonsezo zidzadzisamalira zokha.

45 Tsopano, zindikirani, inu muyenera kubadwa kachiwiri; uko ndiko kusinthidwa; payenera kukhala kusinthira. Inu mukuti, "Chabwino, M'bale Branham, ine ndikudziwa mkazi wina wake kuno; bwanji, iye sanachitepo kanthu kolakwika kalikonse. Iye ndi mkazi wabwino, kapena bambo 'wakuti- wakuti' uyu; iye

ndi bambo wabwino. Iye samachita kanthu kalikonse; iye samalakwira aliyense." Izo sizitanthawuza kanthu kamodzi. Iye akhoza kukhala woyandikana naye wabwino, koma iye si Mkristu mpaka iye atabadwa kachiwiri.

Yesu anati, "Pokhapokha munthu abadwe kachiwiri (Yohane Woyera 3) kuti iye sangakhoze kuwona nkomwe Ufumu." Tsopano izo zikutanthawuza_kuwona kumatanthawuza kumvetsa. Iwe umayang'ana pa chirichonse ndi kuti, "Ine sindikuchiwona konse icho;" iwe ukutanthauza "Iwe siukuchimvetsa icho."

46 Munthu sangamvetse chifukwa chake anthu amafuula. Munthu sangamvetse chifukwa chake chilankhulidwe cha munthu chingasinthe, ndipo iye namalankhula m'malirime. Munthu wa chibadwa sangawone momwe ulemmero wa Mulungu ungabwere pa maso a munthu, ndipo iye nawona masomphenya ndi kumuwuzwa munthu zinthu zina zake ndi zoyenera kuchita_kuwauza iwo zinthu zomwe ziti zichitike, zinthu zoyembekezeka kuchitika_monga momwe Ambuye anachitira nafe pano ngakhale usiku wathawo. Mwaona?

Malingaliro a chibadwa amayesa kuganizirapo, "Chabwino, kodi iye anachita chiyani?" kapena "Ndi ndale yamtundu wanji yomwe akugwiritsa? Kodi iye ali ndi matsenga amtundu wanji?"

Kumuona munthu akulankhula mmalirime, iwo amati_ ndipo wina namamasulira nanena molondola kwa membala wina wa thupilo zomwe iwo achita, ndi zinthu zomwe iwo sayenera kuzichita. Onani, iwo amaganiza kuti ndi tsenga la mtundu winawake. "Pali chinachake chimene amagwirizana pakati pawo." Iwo sangazimvetse izo. Mpaka munthu ameneyo atabadwa kachiwiri_ndiye pamene iye abadwa kachiwiri, ndiye iye ali mu mzere wachiyanjano chifukwa iye ali wolengedwa watsopano. Kufanizira zoyipa koyamba kuja, khalidwe lokayikira lomwe iye anali, lafa; tsopano iye ndi wolengedwa watsopano. Kotero inu mukuwona, iye sayenera kuchita kuwonjezera chinachake ku zake_tsopano, chifukwa zidzawonjezereka zokha.

47 Zindikirani, inu muyenera kubadwa kachiwiri. Ndipo pamene inu mwabadwa kachiwiri, inu simungabadwe kachiwiri opanda kukhala ndi chikhulupiriro. Uko nkulondola. Kotero inu mukuona, pojambula panga apa, ine ndiri ndi maziko omwe_chikhulupiriro ndi maziko a zonsezi. "Pakuti kopanda chikhulupiriro ndi kosatheka kumukondweretsa Mulungu: pakuti iye amene adza kwa Mulungu akhulupirire kuti Iye ali, ndipo kuti Iye ali wopereka mphotho kwa iwo amene amufuna Iye modzipereka." Iye ayenera kutero. Ndipo pamene iwe uli wokayikira Baibulo, pamene iwe uli wokayikira Mawu kukhala owona, iwe mwina ukanangokhala mmbuyo mpaka poyamba iwe ukhulupirire izo.

Tchimo ndi chiyani?_Kusakhulupirira. Pali zinthu ziwiri zokha zimene zimalamulira umunthu. Ndizo kukayikira kapena chikhulupiriro_chimodzi kapena chimzake. Inu mumagwidwa ndi chimodzi chomwe chiri ndi gawo lalikulu mmoyo wanu. Zimangotengera kuchuluka kwa chikhulupiriro chomwe iwe uli nacho, momwe iwe ungakwerere patali. Koma poyamba chiyenera kukhala chikhulupiriro. Ndiroleni ine ndikhale pa maziko amenewo kwa kanthawi.

48 Tsopano, chikhulupiriro ndi chomwe iwe uyenera kukhulupirira. Chikhulupiriro ndi chimene_"Chikhulupiriro ndi thunthu la zinthu zoyembekezereka^" Iwe uli nacho kale pamene uli ndi chikhulupiriro, chifukwa chikuwululidwa mu chikhulupiriro. "Chikhulupiriro ndi thunthu la zinthu zoyembekezereka^" (Ahebri 11) Umboni_umboni wa mtundu wanji?_Umboni wopatulika.

Kotero, pamene inu munena, "M'bale Branham, ine ndikukhulupirira kuti Mulungu ndi Mchiritsi." Chabwino, ngati inu mukukhulupirira izo ndiyeno nkumulandira Iye monga Mchiritsi wanu_ndipo osati kunama, koma kukhulupirira kwenikweni kuti, ndi mikwingwirima Yake inu mwachiritsidwa_palibe chimene chiti chikutembuzeni inu kuchoka kwa icho, ndi chinthu chokhazikika.

Tsopano, inu mukhoza kukhala ndi chiyembekezo_kumangothawira ku ichi ndi kuthawira ku icho, koma pamene inu muli ndi chikhulupiriro inu mukuchidziwa icho, chifukwa ndi umboni_inu muli nacho kale.

49 ^Ndi angati amene anamumvera Oral Roberts mmawa uno_pamene iye anali kulalikira mmawa uno_Oral Roberts? Ndipo ine ndinamumva iye akulankhula chinachake kapena zakuti pali chikhulupiriro cha chiwombolo_kupemphera pemphero la chikhulupiriro la chiwombolo. Iye anati, "Chitani kukhudza kwanu pakugwira wailesi_chitani kukhudza kwanu pakugwira chinachake ndi cholinga^" mwamunayu amachita izo kuti awapatse anthu chinachake chimene iwo akanakhoza kuyikapo manja awo_chinachake kuti anene, "Ine ndachipeza icho tsopano, chifukwa iye anandiwuza ine kuti ndigwire wailesi yanga. Ine ndachipeza icho." Mwaona? Tsopano, izo zonse nzabwino. Koma tsopano chikhulupiriro chenicheni sichisowa kugwira kalikonse ka zinthu izo. Tsopano, ine sindikunyozeza M'bale Oral, ayi konse. Iye akugwira ntchito yaikulu ndipo ndi munthu waumulungu, ndipo ine ndimaganizadi kwambiri za Oral Roberts. Zangoyipa kuti ife tiribe ambiri otero. Koma chomwe ine ndikuyesa kunena: ndi chakuti chikhulupiriro sichimasowa chinthu chirichonse. Chikhulupiriro chimakhulupirira Mawu a Mulungu! Pakuti chikhulupiriro chimadza pa kugwira_ayi. "Chikhulupiriro chimadza pakumva, ndipo kumva [kwa] Mawu a Mulungu." Iwo amazika icho. Ndi pamenepo. Ndipo chikhulupiriro (monga ine ndinanena) chiribe kutalikirira kwa icho. Chikhulupiriro ndi pakali pano. Chikhulupiriro ndi pano.

50 Tsopano monga, ngati pali winawake_mwana wamng'ono uja tsiku lina lija. Mayi uja amene Mlongo Kidd ndi enawo amawanena kuti anali ndi mwana amene anali ndi matumbo ake kunja_wopanda bowo pathako potulukira chakudya_ tsopano, mayi uyu, kumumva Mlongo Kidd ndi iwo akuchitira umboni, anakhulupirira kuti iye ngati akanandiyitana, ndipo ine ndikanadzamupempherera mwana ameneyo^Tsopano onani Mulungu amapereka kwa anthu ife^Ena a ife zatichitikira ndi Mulungu kwenikweni mwakuti Mulungu amangokhala ngati_kupita umu ndi kukalankhula ndi M'bale Neville kapena winawake amene mumadziwana naye. Ndipo ife nthawi zina timawafunsa anthu amenewo kuti atipempherere. Izo ndi zomwe ife tiyenera kuchita. Ndiye, ngati ife tiri ndi chikhulupiriro kuti mwamuna ameneyo, mkazi, kapena wina aliyense amene akutipempherera ife, akulankhula kwa Mulungu, ndiye chikhulupiriro chathu chagwira; chakhomererereka; chakhazikika.

51 Pano, Mroma anapita kukakumana ndi Yesu, ndipo iye anati, "Ine sindiri woyenera kuti inu mubwere pansu pa denga langa. Ine sindine woyenera; ndipo ine sindina^Ine sindikudziwerengera ndekha mwa njira imeneyo." Koma anati, "Mwana wanga akudwala kwambiri, ndipo Inu mungolankhula Mawu, mwaona? ndipo mwana wanga akhala moyo." Chinali chiyani? Kutalikirira kunalibe kanthu, chifukwa Mulungu ndi wopezeka paliponse. Mulungu ndi wamphamvuzonse. Ndipo paliponse Mulungu ali, umphamvuzonse uli pamenepo. Ndipo Mulungu pokhala wopezeka paliponse, izo zimapanga Mulungu paliponse_ponseponse. Mwaona, Mulungu ali wopambana chimodzimidzi mu Germany, mu Switzerland, ndi uko ku Africa miniti yomwe ino, monga momwe aliri pomwe pano. Ndi zimenezotu!"

Kotero tsopano iye anati, "Ine sindiri woyenera kuti inu mubwere pansu pa denga langa; ingolankhulani mawu." Chinali chiyani icho? Chinali chikhulupiriro cha Mroma uja. Iye anakhulupirira izo.

Ndipo Yesu anati, "Pita njira yako, mwana wako ali moyo." Ndipo iye anawuyamba (ulendo wa masiku awiri), ndipo tsiku linalo iye asanafike kwawo, anakumana ndi ena antchito ake akudza. Ndipo iwo anati, "Mwana wanu ali moyo."

Ndipo Mroma anasangalatsidwa kwambiri mpaka iye anati, "Inali nthawi yanji ya tsiku pamene iye anayamba kupeza bwino? Gawo lanji la tsiku?"

Iye anati, "Cha mu ora la khumi ndi limodzi iye anayamba kusintha."

Ndipo Mroma anadziwa kuti inali nthawi yomweyo pamene Yesu anati, "Mwana wako ali moyo," ndipo iye anakhulupirira. Amen.

52 Wamphamvuzonse, waponseponse, wodziwazonse, wopandamalire_ ameneyo ndi Mulungu. Kotero, pamene iwo ayimba foni nati, "Pempherani!" Izo zimakhudza, ndipo chikhulupiriro chanu chimabweretsa Mulungu! Ndi chinthu chimene chimabweretsa pemphero ndi Mulungu limodzi powoneka. Pemphero, chikhulupiriro chimasintha kuchokera apa kufika apa! Chimabweretsa izo pamodzi!

"Lankhulani Mawu; zonse zomwe ine ndikufuna kuti Inu muchite ndi kunena Mawu, ndipo zonse ziri bwino." Iye samasowa kukhala uko; ingonena Mawu. Motani? Mulungu ndi wopezekaponseponse. Iye ndi wamphamvuzonse. Iye ndi wamphamvu pansu pa dziko monga momwe analiri pamwamba pa dziko, kapena ku mbali iliyonse. "Iye ndi Mulungu. "Ndipo chinthu chokha Inu muti muchite ndi kungolankhula Mawu," iye anatero.

Ndipo tsopano chikhulupiriro chimachita zina zonzese; chikhulupiriro chimachita zinazo, kotero inu muyenera kukhala ndi chikhulupiriro ngati maziko. Chikhristu chonse, zonse inu muli, zonse inu muti mudzakhale nkonse, maziko ake ali pa chikhulupiriro mu Mawu.

53 Icho ndi chifukwa chomwe ine ndimakhulupirira Mawu. Ine sindingayike chikhulupiriro changa pa china konse ayi. Ngati ine nditatu ndidzachiyike pa mpingo, ine ndidzachiyika pa mpingo uti?_Katolika, Lutherani, Methodisti, Baptisti, Chipentekoste? Ine ndidzachiyika pa uti? Ine sindikudziwa. Iwo onse amasokoneza ndi china chirichonse_kupiringiza mizere ndi zina zonse_koma pamene ine ndiyika chikhulupiriro changa mu Mawu Ake, icho chazikika. Palibe amene akumasulira icho, ndi ichi: PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndiye ine ndimakhulupirira izo. Pamenepo ndi pokhazikitsa.

54 Dokotala wabwino wamng'ono, (mu mzinda uno) mzanga wa ine_Dokotala Sam Adair. Ife takhala tiri anyamata limodzi. Inu nonse mukumudziwa Sam. Ndipo iye anatero kwa ine; iye anati, "Bill^" Masomphenya aja atadza kale. Ndinamuwuza iye pomwe iye akanadzamangapo malo ake, momwe iwo azidzawonekera, (tsopano, pitani kalowenimo pitani mukamufunse iye nthawi ina ngati izo ziri zowona)_zaka ziwiri kapena zitanu izi zisanachitike_ndinamuwuza iye pomwe adzakhala zikanachitikira, ine ndinati, iwe udzatenga pafupi buloko ya Mzinda imeneyo;" ndipo palibe ngakhale chinthu chimodzi pakati pa iye ndi iyo, ndipo ndi malo osamalirirapo anthuwo. Dokotala Adair tsopano anatenga malo ena onsewo ndi chipatala. Ndi zokhazo.

Dokotala Adair anadzaza apo chimodzimidzi basi_masomphenya aja_pamene malo amene iye anati, "Iwo sangagwiridwe ngakhale kwa zaka makumi awiri ndi zisanu; ndi mabwalo."

Ine ndinati, "Dokotala, Ambuye akupereka iwo kwa iwe, chifukwa cha kudzichepetsa kwako."

Iye anati, "Ine sindine wabwino."

Ine ndinati, "Iwe ndi kamba. Iwe uli ndi chikumba kunja kwako, chigaza chomwe umayang'aniramo amzako kunja kuno, koma mkatimo iwe ndiwe mwamuna weniweni. Tuluka mu chigaza chimenecho." Ine ndinati, "Mulungu wakupatsa iwe izi."

Iye anati, "Ine sindinakukayikirepo iwe, Billy, koma ine ndiyenera kukayikira izo."

Ine ndinati, "Pita ku ofesi yako." Kotero anaturuka napita.

Mmawa wakewo iye anandiyitana ine nati, "Ine ndikuzidwa mwa pafupi kufa."

Ine ndinati, "Chavuta ndi chiyani?" (munali cha mu Julaye)? Ine ndinati, "Chavuta ndi chiyani Doc?"

Iye anati, "Ine ndagula kale malo aja, Billy. Iwo anali ndi msonkhano usiku wathawu mu Boston, ndipo ine ndagula kale malowo mmawa uno."

Ndinati, "Ine ndinakuwuzwa iwe."

Ine ndinali kumeneko tsiku lina kukalankhula naye (pamene mfuti inaphulikira mu nkhope yanga.) Iye anati, "Ine ndikuganiza kuti ine ndawawuzwa izo anthu mpakana chikwi amene amabwera kuno, chotero." Ndi chiyani icho? Tsopano, pamene Mulungu alankhula chirichonse, chiyenera kuchitika!

55 Usiku wathawu amzanga ena anabwera. Iwo anamva za masomphenya aja ndinawafotokoza za mphalapala ija imene inali ndi nyanga zotalika ma inchesi makumi anayi mphambu ziwiri ndi chimbalangondo cha siliva pamwamba pa ubweya wake. Ine sindikudziwa kuti ndi anthu angati amene akubwera kunyumba amene akufuna kuziwona izo. Ine ndinati, "Muyezo wake ndi uwu; pitani pa nyangazo." Inu munazimva izo zikufotokozedwa zisanachitike. Mwaona. Motani?_Pamene Mulungu alankhula chirichonse, icho chiyenera kuchitika! Ndicho ndi chifukwa_chakhazikitsidwa.

Tsopano apa pali dongosolo la chipulumutso. Ndiyeno ngati masomphenya Ake achitika mwangwiro chimodzimodzi momwe iwo ananenera kuti adzachita (ndipo mpingo uwu kuno ukudziwa kuti izo nzolondola) Ndiye nanga bwanji Mawu Ake? Awo ndi okhulupirika kwambiri koposa masomphenya. Ngati masomphenya sanalankhule mogwirizana ndi Mawu, ndiye masomphenyawo ndi olakwika. Koma ndi Mawu poyamba, chifukwa Mawu ndiwo Mulungu. Kotero Iye ali waponseponse. Iyeyo analankhula izi kuno, nazipanga kukwaniritsika mu Canada. Amen. Onani, iye ali waponseponse.

56 Chabwino, choyamba inu muyenera mubadwense, ndiyeno pamene inu mwabadwanso, inu muli ndi chikhulupiriro; inu mukukhulupirira Mawu. Mpaka inu mutabadwanso inu muzitsutsana nazo. Ngati inu mwangokhala otsamira pa chipembedzo, nimukhala ndi kachidziwitso ka umunthu kuti muzichita molondola, inu simudzakhoza kutha kugwirizana pa Mawu a Mulungu. Inu simudzatha kutero. Inu muyenera kubadwanso; ndipo kubadwanso, iko kumabala chikhulupiriro.

Chabwino, ndiye inu mutatha kukakhala ndi chikhulupiriro, ichi apa_c-h-i-k-h-u-l-u-p-i-r-i-r-o (chikhulupiriro), ndiye inu muli mu malo a kukula basi.

57 Tsopano, anthu ambiri amapita ku guwa, napemphera, nati, "Ambuye, ndikhululukireni ine," ndipo chochitika chachikulu cha chiyeretso chimadza pa iwo ndipo^ndiye iwo amakhala ndi nthawi yabwino_kupita pa guwa kufuula. Inu mumabwerera nimuti, "Mulungu adalitsike, ine ndachipeza." Ayi, iwe wangoyamba ku malo komwe iwe ukhoza kukula. Iwe siunachite kanthube. Onani, chinthu chokha chimene iwe wachita iwe wangoyika maziko.

Tsopano, inu muyamba kumanga nyumba, ndipo inu mukakhuthulira maziko anu ndi kuti, "Bwanawe, ine ndiri nayo." Onani, inu muli ndi maziko oti mumangepo nyumba yanu. Tsopano inu muyenera kumanga nyumbayo.

Tsopano pamenepa ndi pomwe chinthu ichi chimadza mmawa uno za chomwe titi tilankhule tsopano. Chabwino, nyumba; maziko awa ali poyamba. Kodi maziko a Chikristu ndi chiyani? Chikhulupiriro mu Mawu a Mulungu. Amenewo ndi maziko anu. Ndiye inu mumayamba kukula. Ndiye inu mumayamba. Inu mumayamba kuwonjezera ku maziko amenewa.

58 Tsopano, kumanga nyumba, inu mumayamba mwazika zotetezera zanu ndi zina zonse, M'bale Wood, ndipo ena mwa makalipentala awa ndi omanga zinyumba kuno akhoza kutiwuzwa ife momwe umamangira nyumba yako, mwaona; koma ine ndikuwuzani inu momwe mungamangire nyumba yanu yauzimu, momwe Mulungu angakhalemo. Iye akufuna kumakhala mwa inu. Iye akufuna kukupangani inu monga Iyemwini. Iye akufuna inu kuti munyezimiritsidwe^ kunyezimiritsa kani, umunthu Wake.

59 Inu mukudziwa mu nthawi yakale pamene iwo ankapanga golide, iwo asanakhale ndi ng'anjo yomuwotcheramo, iwo ankachita kumumenya golideyo, kumumenya kuchotsa zitsotso, zitsulo, ndi kopala

ndi zina kuzichotsa, ndi kumangomenyabe, ndi kutembenezira kwinako, ndi kumumenya iye_Amwenye amachita zimenezo tsopano. Kumumenya golide; ndipo iwo amamumenya iye. Inu mukudziwa momwe iwo ankakhoza kudziwira kuti zitsulo zachokamo, ndi zinyatsi zonse, ndi dothi kuti zachokamo? Pamene yemwe amamenyayo amakhoza kuwona chinyezimiro chake chomwe ngati pa kalilore. Iye anali waukhondo ndi woonekera mokwanira mpaka kuti anali kunyezimiritsa womenyayo.

Ndiyo njira imene Mulungu amachitira. Iye amatenga golide amene Iye wamupeza mu dziko, ndipo Iye amamumenya uyo mwa Mzimu Woyera_kumutembenuza kuseri ndi kuseri ndi kuseri, namumenya iye mpaka Iye atalandira^akhoza kuwona chinyezimiro Chake; ndipo izo ndi zomwe ife timayenera kuchita_kunyezimiritsa Mwana wa Mulungu.

60 Ndipo tsopano ife timayenera kuchita ntchito Yake. Iye anati, "Iye amene akhulupirira mwa ine^" (Yohane Woyera 14:7[12]) "Iye amene akhulupirira ine, ntchito zomwe ine ndizichita adzazichita iyenso;"

Inu mukuyamba kunyezimiritsa ntchito za Khristu. Koma ambiri a ife timayesa kuchita ntchito za Khristu chinyezimiro cha Khristu chisanakhale mwa ife. Tsopano apo pali vuto. Ife timapeza zinthu izo zikuchitika. Inu mukudziwa izi. Ine ndikudziwa izi. Ife timawona kupunthwa konseku mu njirayi. Ife timapeza mulu wa ziphakasa za alaliki, Akhristu, atawunjikidwa mu msewu'wu. Izi ndi chifukwa chakuti iwo sanalowemo moyenera.

Ndicho chifukwa ine ndiri pano mmawa uno_ndiko kuyesa kuphunzitsa mpingo waung'ono uno, ndi ine mwini, momwe ife tingakhalire malo okhalamo a Mulungu Wamoyo; Ndi angati akufuna kukhala zimenezo? Malo okhalamo a Mulungu Wamoyo.

61 Tsopano apa pali chomwe ife tichita. Kodi chinthu choyamba ndi chiyani? Kukhala ndi chikhulupiriro ndi kubadwanso_kumeneke ndiye kuyika maziko. Ndiye, titatha kuyika maziko, kachiwiri, muwonjezere kwa maziko anuwo. "Muwonjezere kwa chikhulupiriro chanu," Petro anatero apa. Onjezerani kwa chanu_choyamba inu mukhale ndi chikhulupiriro, ndiye inu muwonjezere ukoma kwa chikhulupiriro chanu. Awa ndi malo otsatira. Choyamba khuthulirani maziko anu_chikhulupiriro. Ndiye kwa chikhulupiriro chanu onjezerani ukoma.

Tsopano, pomwepo pamatigwetsa ambiri a ife pansi. Inde, bwana. Inde, onjezerani ukoma kwa chikhulupiriro chanu. Izo sizitanthawuza kumangokhala moyo wa unamwali, mukudziwa, monga mkazi kapena mwamuna, ndi zina zotero. Izo ziribe chochita ndi izi. Baibulo linati, (ife timawerenga apa mu Bukhu la Luka pamene linati,) "Ukoma unachoka mwa Iye." Kodi izo nzolondola? Ngati ife titi tikhale monga Iye, ife tiyenera kukhala ndi ukoma ndiye. Ife tiyenera kukhala nawo kuti tikhale monga Iye.

62 Ngati nyimbo imene ija imene ine ndinaikondapo konse mu bukhu la nyimbo (imodzi ya zopambana kwambiri) inali: "Kukhala monga Yesu." Chabwino, ngati ine nditi ndikhale monga Yesu, ine ndiyenera kukhala ndi ukoma ndi chotulutsa, kuti ndizichipereka kuchokera kwa ine kumka mwa anthu, chifukwa mphamvu inatuluka mwa iye kumka kwa anthu_ukoma. Ndipo inu musanautulutse, inu muyenera kukhala nawo choyamba. Ngati iwe ulibe iwo, siungatuluke. Palibe malo oti uchokerepo.

Bwanji ngati wina akanafuna kukoka ukoma kuchokera mwa ife_cheke icho chikanabwezedwa "ndalama ndi zosakwanira." Ayi, kulibe koti angatengeko_cheke chanjanja. Wina wake kuyang'ana pa inu ngati Mkhristu ndipo mawa kukuwonani inu kuno mukuchita ngati wochimwa_mulibe ukoma wokwanira womwe ungatengedwe kuchokera apo. Onani, izo nzolondola.

Ukoma ukhale uli mwa ife, ndipo mpaka ife tipeze ukoma_ndiye pamene ife tipeza ukoma woona, ife tikhoza kuwuwonjezera iwo kwa chikhulupiriro chathu. Limenelo ndi khoma lotsatira la maziko.

63 Tsopano, poyamba iwe ukhale ndi chikhulupiriro. Chikhulupiriro chokha sichingachite izo. Iwe uyenera^Petro anati, "Ndiye onjezerani ukoma kwa chikhulupiriro chanu." Inu muyenera kukhala ndi ukoma polinga kuti muwonjezere kwa chikhulupiriro chanu. Tsopano, ndiye, izo mwina zingakhale chifukwa chomwe inu mulibe iwo ndi chifukwa mipingo yambiri ya lero imaphunzitsa kuti inu simusowa kukhala nawo, kapena masiku a iwo anapita. "Inu simusowa kukhala nawo. Chinthu chokha inu muyenera kuchita ingojowinani mpingo. Inde, masiku apita." Ukoma_aliyense amadziwa chimene mawu oti ukoma amatanthawuza; ndipo ife tiyenera kukhala nawo.

Ngati ukoma unatuluka mwa Iye kukachiza mkazi amene amadwala, Iye akuyembekezera ukoma womweyo mu Mpingo Wake, chifukwa Iye anali Chitsanzo chathu. Ndipo ngati Iye anali ndi ukoma woti apereke kwa anthu, Iye akuyembekeza kuti ife tikhale ndi ukoma kuti tipereke kwa anthu, ndipo kodi ukoma ndi chiyani? Ukoma ndi mphamvu_nyonga. Ena aiwo sakhulupirira konse mu mphamvu ya Mulungu. Iwo amati, "Izo zinatha. Chinthu chokha iwe ungachite ndikulemba dzina lako pa bukhu. Kukonkhedwa madzi kapena kutsanuliridwa, kubatizidwa, kapena china chowonjezera, ndipo ndi zimene inu muyenera kuchita." Koma Petro ananena apa, "Onjezerani ukoma."

64 Tsopano, Petro akulankhula za kumanga Nyumba ya Mulungu, mukuona? Kachisi wa Mulungu. Kuyikonza iyo mpaka pa malo_ndipo inu mutakhala ndi ukoma inu muyenera kukhala ndi_inu mutakhala ndi

chikhulupiriro, inu muyenera kukhala ndi ukoma nacho. Ndi zolondola. Kukhala ndi ukoma wa kwa dziko lonse.

Ine ndinalalikira uthenga pafupi zaka makumi awiri zapitazo, ine ndikuganiza, pa M'busa Bambo Kakombo_ Kakombo, m'busa. Ndinautenga mu phunziro la Mawu Yesu anati, "Lingalirani kakombo mmene samavutikira kapena kaluka koma ine ndinena kwa inu, Solomoni mu ulemerero wake wonse sanavale monga mmodzi."

Yang'anani pa kakombo. Iye amachokera kutali pansi mmatope, ndipo miniti iliyonse ya tsiku ayenera kumakoka kuchokera mu dziko. Mwaona? Ndipo amachita nawo chiyani ukoma umene iye amakoka? Iye amapereka iwo kunjira. Iye amapanga maonekedwe okongola kwa woyamikira. Iye amadzitsegula yekha chifukwa cha uchi, kuti njuchi zibwere ndi kudzatenga gawo lake. Osadandaula; ali nawo iwo basi kuti aziwupereka. Nanga bwanji njuchi italowa mmenemo_ "ndalama zosakwanira"_palibe uchi. Njuchi imeneyo ikhoza kukanda mutu wake ndikuti, "Ndi kakombo wamtundu wanji uyo?"

65 Ngati munthu abwera kuyesa kudzapeza chipulumutso napita ku mpingo umene umakhulupirira kuti masiku a zozizwitsa anapita^Monga Jack Coe nthawi ina anati akulowa modyera chakudya ndipo anali ndi mndandanda wa zakudya wawukulu. Anayamba kuwerenga mndandandawo "Nyama ya T-bone," ndi zinthu. Iye anati, "Ine nditenga T- bone."

"Chabwino, izo zinali za tsiku lapitalo. Ife tiribe iyo." Ukhoza kungosiya mndandanda pansi ndikutuluka. Uko nkulondola, chifukwa alibe chirichonse choti nkudya basibe. Kotero ukhoza kungopita kumene malo odyerako ali ndi chinachake choti nkudya.

Ndipo munthu wauzimu_kukula kumasowa chinachake choti nkumadya. Ndiwo Mawu a Mulungu. Ine ndimakhulupirira mawu Ake onse.

"Mulungu wakonza gome

Pamene oyera a Mulungu akudyetsedwa, Iye akuyitana anthu Ake osankhidwa 'Bwerani mudzadye;'

Ndi manna Ake Iye amawadyetsa Iye amapereka zosowa zathu zonse:

O, ndi kokoma kudya ndi Yesu nthawizonse!"

Iye ali nawo, inde, bwana_Mpingo uli nawo. Mpingo wa Mulungu Wamoyo wamangidwa mwa munthu wangwiro wa chidziwitso cha Khristu.

66 Tsopano, tsopano inu muyenera kukhala ndi ukoma. Ine ndinati ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa wina amakonda kununkhiza fungo. Iye si waumbombo; iye ali ndi fungo. Iye asanapereke fungolo, iye ayenera kukhala nalo. Asanapereke uchi iye ayenera kukhala nawo. Iye asanapereke kukongola, iye ayenera akhale ali nako. Musanapereke ukoma, inu mukhale nawo. Kotero onjezerani kwa chikhulupiriro chanu ukoma. Amen. Mwamvetsa? Ife tikhoza kukhala pamene; nthawi yaitali, koma nthawi yathu ikutithawira ife. Kuwonjezera ukoma kwa chikhulupiriro chanu.

67 Tsopano, choyamba, ndi chikhulupiriro, ndiye ukoma, ndiyeno kachitatu, inu muwonjezere chidziwitso. Chidziwitso_ tsopano izo sizitanthawuza kudziwa kwa mdziko, chifukwa uko ndi kupusa pamaso pa Mulungu, koma chidziwitso kuti uweruze. Kuweruza chiyani? Cholondola kwa cholakwika.

Inu mumaweruza bwanji ndiye ngati inu muli ndi chidziwitso cha Chikristu palimodzi ndi ukoma wanu ndi chikhulupiriro, inu mumaweruza ngati Mawu ali olondola kapena olakwika. Ndipo ngati inu mutasiya ziphunzitso zanu zonse ndi kusakhulupirira kwanu konse_ zonse zimene inu mukuti mwazichita_ ndiye inu muli ndi chidziwitso kuti mukhulupirire kuti Mulungu sanganame. "Lolani Mawu a munthu aliyense kuti akhale abodza, koma Anga akhale Owona." Mwaona, tsopano inu mukupeza chidziwitso. Ndicho chidziwitso chapamwamba. Simusowa kukhala ndi madigrii anayi a ku koleji inayake kapena chinachake ngati icho kuti mukhale nacho, chifukwa mphamvu zonsezi zaperekedwa kwa inu ndi Mulungu kuti aziyike pa maziko a chikhulupiriro chanu kuti mukhoze kufika pa usinkhu wonse wa munthu wamoyo weniweni wa Mulungu. Inde, bwana.

68 Onjezerani chidziwitso chifukwa_ chidziwitso cha Mawu Ake. Inu mukhulupirire izi mwa njira iyi. Monga ngati_inu muyenera kukhulupirira lero kuti_ ndi kuvomereza kuti masiku a zozizwitsa sanathe. Chidziwitso kuti chomwe Mulungu akulankhula, Mulungu akhoza kuchichita.

Abrahamu anakhulupirira izo, ndipo pamene iye anali wa zaka zana, iye sanagwedezeke pa lonjezo la Mulungu kupyolera mkusakhulupirira. Tayang'anani momwe Mawuwo ankawonekera opusa.

Apa pali mwamuna wa zaka zana akuyembekezera mwana kuti abadwe mu banja lake mwa mkazi wa zaka makumi asanu ndi anayi. Mwaona? Pafupi zaka makumi asanu zinapita_ ali wosabereka. Anakhala naye kuyambira pamene iye anali msungwana wamng'ono kapena msungwana wongopitirira zaka khumi, ndipo pano ndi uyu: msempha wake wa moyo unali utafa, ndipo mimba ya Sara inali itafa, ndipo

chiyembekezo chonse chinali chitapita (pokamba za chiyembekezo) komabe mopanda chiyembekezo, iye anakhulupirira mwa chiyembekezo, chifukwa iye anali ndi chidziwitso kutibe Mulungu anali wokhoza kusunga chirichonse chomwe Iye analonjeza.

69 Tsopano, pamene inu muli nacho chotero, ndiye muwonjezere icho ku chikhulupiriro chanu. Pamene inu muli ndi ukoma wona, uwonjezerani iwo kwa chikhulupiriro chanu. Pamene inu mungakhoze kuyenda kuno mu msewu, kukhala moyo monga Mkristu; kuchita monga Mkristu, kukhala Mkristu_onjezerani izo kwa chikhulupiriro chanu. Pamene inu muli ndi chidziwitso_inu mukuti "Chabwino, ine sindikudziwa tsopano ngati Lembo ili liri lolondola chabe. Tsopano, apa pali Machitidwe 2:38_Ine sindikudziwa momwe ndingachitire molondola izo; Machitidwe 28:19^" Chabwino, musawonjezerepo kalikonse, chifukwa inu simunakhale nachobe. Mwaona? Kodi inu muchita chiyani? Chifukwa inu mulibe chidziwitso chokwanira kudziwa za Mulungu pakali pano kuti Baibulo silidzitsutsa Lokha. Zisiyeni zokha. Musalankhulenso za izo. Mukuona? Zisiyeni zokha, koma pamene inu mungakhoze kuwona kuti Malembo sakusutsana, kuti inu mungati kuti_ndipo mungawone kuti mwa vumbulutso la Mulungu, Mawu onse analembedwa mwa zinsinsi, ndipo chidziwitso cha Mulungu chokha ndi chomwe chingawawulule Iwo. Ndiye pamene inu mupeza titi_kuvomereza liwu lirilonse la Mulungu ndi "Amen," ndiyeno onjezerani icho kwa chikhulupiriro chanu.

70 O, inu mukuyamba kukhala munthu wabwino zedi pakali pano, onani. Inu mukubwera m'mwamba. Mukuona? Ndi chiyani? Ndi chikhulupiriro, ndiye ndi ukoma, ndiye chidziwitso. Mukuona momwe zikumumangira munthu uyu? Inu mungawone kuti palibe_palibe njira yothawira izo. Iyi ndi njira yokhalira mu thunthu lonse la Khristu. Inde, bwana.

Kuweruza_kuweruza molondola; kuweruza ngati ziri zolondola kapena zolakwika kukhulupirira Mawu a Mulungu. Kuweruza ngati ziri zolondola kapena zolakwika kaya kuti ine ndizitumikira zikhulupiriro kapena kutumikira Mulungu; kuweruza ngati ziri zolondola kapena zolakwika: "Ine ndiyenera ndibadwenso, kapena kulowa mpingo." Ndiye inu muyamba_kuweruza molondola. Pamene wolalikira ati, "Masiku a zozizwitsa anapita." Baibulo linati "Yesu Khristu ndi yemweyo dzulo, lero, ndi nthawi zonse." Tsopano, inu mukhulupirira ziti? Pamene inu muti, "Ine nditenga Mulungu." Tsopano, inu simungonena izo kunena kuti, "Chabwino, ine_ine ndikungotenga izo zomwe zachokera mu mtima wanu." Koma chinachake mkati mwanu_chikhulupiriro chanu chinakankhira kumeneko. Ndi zimenezo. Chikhulupiriro chanu chikuti, "Ine ndikudziwa kuti Iye ali yemweyo. Ine ndachitira umboni Iye chimodzimidzi." Palibe chirichonse chingachotse icho mkati mwanu. "Ine ndikudziwa Iye ndi weniweni." Ndiye onjezerani icho kwa chikhulupiriro chanu. Ziyikeni izo pa maziko.

71 Inu mukubwera mmwamba tsopano. Kukwera mpaka mmwamba cha ku Ufumu. Mwafika pa malo awa tsopano, chabwino.

Tsopano, chinthu chotsatira wolalikira akuwuzwa iwe, ndi anthu ambiri kuti, "Zinthu izi zimene iwe umawerenga mu Baibulo, izo zinali za tsiku lina. Tsopano, ine ndikuwuzwa iwe chifukwa chake: Chifukwa ife sitikumangira zinthu izo lero. Ife sitikumangira izo. Mukuona, ife sityenera kapena ife sitisowa kumachita zinthu izo: machiritso auzimu; ife sitimachita za kulankhula mmalirime mu mpingo kuti mpingo wathu ukhale molunjika. Ife sitimachita izi." (Chabwino tsegulani pamene; ine ndiri ndi Lemba lomwe ndalemba pano lokhudza zimenezo_ngati kuli kofunika kuti ife tizichitabe kapena ayi.)

Tsopano, koma akuti, "Ine sindikudziwa, ife sityenera kumachita izo lero. Chinthu chokha chomwe ine ndikuganiza kuti ife tizichita: Ife tiziphunzira kulankhula bwino patsogolo pa gulu; ife tizipita ndi kukawalola adotolo opima misala kuti azipima malingaliro athu ndi kuwona ngati ife tiri oti tingakhoze kulankhula moyenera, ngati IQ yathu ndi yapamwamba mokwanira kuti tichite izo, ndi zina zotero, monga choncho; ndikuganiza kuti ife tiri ndi mipingo yaikulu zedi; ife timange bungwe lathu."

72 Ife sitikumanga bungwe. Ine sindiri pano mmawa uno kumanga bungwe! Khristu sananditume ine ndidzamange bungwe! Khristu anandituma ine kuti ndimange aliyense payekha kuti afike pa thunthu la Yesu Khristu kuti iwo akhale nyumba ya mphamvu mwa Mawu Ake_mwa Mawu Ake. Kumanga munthu payekha kuti afike pamalo amenewo. Osati kumanga bungwe kuti likhale chipembedzo chopambana, koma kumanga aliyense payekha kuti akhale ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ilo ndiro lingaliro.

Onjezerani kwa chikhulupiriro chanu ukoma; kwa ukoma wanu, onjezerani chidziwitso. Chabwino, tsopano, inu mukudza pa malo.

73 Tsopano, pamene iwo ati ayambe kunena, "Chabwino, ife sitikusowa kuvomereza izo lero." Inu mukusowa kutero. Ziyenera kukhala. Malembo sanganame ndipo "Palibe tanthawuzo la mseri," Baibulo linatero. Inu ingokhulupirirani iwo momwe alembedwera mmenemo. Onani, inu muyenera kukhala ndi zinthu izi. Ndipo njira yokha inu muti mudzakhoze kukhala nazo ndi pokhala ndi chidziwitso chobadwira-kumwamba. Ndipo chidziwitso chobadwira- kumwamba chidzatsimikizira Mawu.

Onani, inu muyenera kukhulupirira_osati kudzipangitsa kukhulupirira izo. Palibe chirichonse cha izi chomwe chiri cha kudzipangitsa kukhulupirira. Onani, ngati inu muti muyese kunena, "Ine ndiri nacho," musakhale mbalame yakuda ikusomekera nthenga za pikoko pa iyo yokha, chifukwa izo zitha kugwapo.

Izo sizinamere pamenepo mwa chirengedwe; izo zangosomekedwamo.

74 Ine ndikuganizira za zomwe Davide ananena pamenepo, Masalimo 1, iye anati, "Iye adzakhala ngati mtengo womwe wabzalidwa mphepete mwa mitsinje ya madzi." Iye akudziwa kusiyana kwa kubzalidwa ndi kuyikidwapo^ kusomekedwapo. Monga mtengo wokalamba wa chiwale; wobzalidwa, umaluka mizu yake pansipo nugwira molimba bwino. Mtengo wakale umene wasomekedwa apowo, inu simukudziwa chomwe chiti chichitike kwa iwo. Ulibe mizu; ulibe maziko. Mwaona? Izo ziri ngati anthu ena ochokera ku Seminare kapena zina zake inu mukuona. Alibe izo^ "Chabwino, dokotala wakuti-wakuti anandidzoza ine mu utumiki. Sizikusintha kalikonse komwe kanalipo. Khristu anakubadwitsani inu mmenemo, mwa chikhulupiriro chanu. Inu munasinthika nimubadwira mmenemo. Ndiye inu mutabadwira mmenemo, izi ndi zinthu zimene Iye akuyembekezera kuti inu muwonjezere. Ingopitirirani kuwonjezera izi. Tsopano, ife tikupita mu mzere wake umene."

75 Tsopano, pakhala chinthu china pa chidziwitso ichi ife titi tikambe za icho_chidziwitso chaumulungu. Mwaona? Kodi Baibulo mu tsiku lino lataya tanthawuzo lake? Onani iwo_anthu ambiri amakuwuzana kuti Baibulo silikutanthawuzana kwenikweni izo. Ngati Mulungu amandiyang'anira ine, nandikonza ine mu tchimo langa; ndipo ngati ine ndiri mwana wa Mulungu, Iye amachita izo. Amakuchitirani inu njira imeneyo. Ngati inu mulakwitsa kalikonse, Iye amakukonzani inu. Ndiye ngati Mulungu ali wosamalira chotero za inu mwakuti Iye amakuyang'anirani inu, nakukonzani inu, ndi mochulukana chotani ali nako Iye, Mawu Ake; amene ali chitsanzo chanu; amene ali Iyemwini:

"Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.

^ndipo anasandulika thupi nakhala pakati pathu."

76 Mawu ndi vumbulutso la Yesu Khristu; Baibulo linatero_ Khristu kukhala akuwululidwa mu Mawu Ake. Ndipo ngati Iye wayang'anira pa inu pamene inu munalakwira malamulo awa_Iye amakuweruzani inu kaamba ka iwo_nanga Iye amasamalitsa motani malamulo Ake amene amakuweruzani inu?

Kupitirira pitirirabe^?^Musandiwuze ine zinthu zimenezo. Ine ndimakhulupirira chidziwitso chenicheni cha Mzimu Woyera. Chidziwitso cha Mzimu Woyera nthawi zonse chidzavomerezera Mawu ndi, "Amen." Pamene inu mupeza zinthu izi zimene zimawoneka ngati zikutsutsana mu Baibulo, iwe ukhala pansu nuwerenga izo mwa pemphero, chotero; ndipo chinthu choyamba chimene umadziwa Mzimu Woyera umayamba kulowa mkati. Pakangopita nthawi umawona zikumangirizana palimodzi, ndipo pamenepo inu mwachipeza. Ndicho chidziwitso.

77 Ena mwa iwo amati, "Chabwino tsopano, Baibulo linati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawi zonse. Ndipo mpingo umati, "Mwa kulingalira kwinakwake, Iye ali yemweyo. Ha- ha. Aa. Inu simukulumikiza mpatawo pamenepo. Inde, bwana. Ayi, bwana, Iye ali yemweyo. Inde, bwana. Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zonse. Palibe kusiyana mwa Iye konse. Iye amakhala mu Mpingo Wake nachita zinthu zomwezo.

"Pakangopita kanthawi_monga ine ndinalankhulira kanthawi kapitako_"pakangopita kanthawi ndipo dziko lapansi silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine. Pakuti^" Iye anati, "Ine ndidzakhala ndi Inu, ngakhale mwa inu, mpakana kumatsiriziro a dziko." Ndiponso Iye anati, "Ntchito zimene Ine ndikuzichita, mudzazichita inunso," Ndiponso Iye anati, "Ine ndidzakhala mpesa; inu mudzakhala nthambi." Ndipo nthambi zimangokhala moyo mwa moyo wa mpesa. Chonse chomwe chiri mu mpesa chimadza kupyola mu nthambi. Ulemerero! Ndiye Khristu ndi yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse; umabala Moyo wa Ambuye Yesu Khristu. Amen.

78 Chidziwitso, osati cha chidziko_chimalingalira. Mtundu uliwonse wa chidziwitso cha chidziko chimalingalira. Onani, koma chikhulupiriro chiribe kulingalira. Mulungu amawululira kwa inu china, chinachake chiti chichitike, wa sayansi wina aliyense akhoza kunena kuti ndi zosiyana, izo sizingatheke; iwe umakhulupirira izo ngakhalebe.

Inde, bwana. Icho sichimalingalira. Baibulo linati, kuti ife timaponya pansu kulingalira. Iwe siumalingalira nacho chikhulupiriro. Chikhulupiriro chiribe kulingalira; chikhulupiriro chimadziwa pamene chiri. Chikhulupiriro chimachita! Chikhulupiriro chimagwirisitsa!" Icho sichingasunthe. Palibe chomwe chingasunthe icho. Ine sindikusamala kaya anena izi, izo, kapena zina; icho sichimasuntha pang'ono konse. Chimakhala pomwepo basi. Kudikira, kudikira, kudikira, kudikira_palibe kusiyana kulikonse, icho chimakhala pomwepo.

Mulungu anamuwuzana Nowa zinthu izi zidzachitika; iye anakhulupirira Izo. Mulungu anamuwuzana Mose zinthu izi kuti zidzachitika; iye anakhulupirira Izo. Mulungu anawawuzana atumwi zinthu zina zake zomwe zikanadzachitika_napita ku Pentekoste nakadikira; iwo anakhala pomwepo. Inde, bwana.

79 Chabwino, tsopano, chidziwitso_Tsopano, osati chidziwitso cha chidziko, koma ndi chidziwitso chakumwamba, ndipo chidziwitso chakumwamba pamene Mulungu ali kasupe wa chidziwitso chonse, ndipo Mulungu ndi Mawu, ndiye ngati iwe uli ndi chidziwitso chakumwamba, iwe umakhulupirira Mawu,

ndipo umalingalira, chirichonse mwa Mawu.

Mulandu wa msonkho uwu womwe mpingo unalimo, kapena ine ndakhala ndirimo, mmodzi wa amuna tsiku lina pa kuzenga kwakung'ono anandiwuza ine, nati^Ine ndinati^ iwo samakhoza kupeza kalikonse kolakwa. Ndipo chotero iwo anayamba ku^Ine ndinati, "Chabwino, ndiye ngati palibe cholakwika, bwanji inu simukuchoka kumbuyo kwanga?"

80 Iye anapitirira kundiwuza ine za Malembo ena. Iye anati, (munthu wamkulutu zedi ali ndi ndudu mu dzanja lake) "Bambo Branham, ine ndi wophunzira za Baibulo." Ine ndinati, "Ine ndakondwera kumva izo."

Iye anati, "Tsopano, ine ndikufuna kudziwa kuti ndi matsenga a mtundu wanji amene iwe umagwiritsa ntchito popempherera pa mipango iyi ndi kuyitumiza iyo kunja; timatsenga tija topempherera pa timipango ndi kutitumiza kwina; zovala zija zomwe iwe umati ndi zodzedwa, zovala." Iye anati, "Ndiye, iwe umawalipiritsa kwa izo."

Ine ndinati, "Ayi, bwana, palibe malipiro kwa izo." Ndipo iye anati, "Chabwino, pa matsenga amenewa^"

Ine ndinati, "Inu kodi mukudzitcha izo matsenga, bwana? Inu munandiwuza ine mphindi zingapo zapitazo kuti inu munali wophunzira Baibulo."

Iye anati, "Ndinedi."

81 Ine ndinati, "Ndiwuzeni ine Machitidwe 19:11." Chidziwitso_iye anadzitchera yekha mpaka mkati_anayesa kusintha nkhani. Ine ndinati, "Ndiye ndiwuzeni ine Yohane 5:14: sanathe kutero. Ine ndinati, "Nanga Yakobo 5:14_iye sanathe kutero. Ine ndinati, "Kodi inu mukudziwa^Yohane 3:16?" Chidziwitso, kuphunzira, dziko, koma pamene^

Iye anati, "Koma Bambo Branham, inu mukuyesa kuwuzenga mlandu uwu mwa Baibulo. Iye tikuwuzenga iwo mwa malamulo a dziko lino."

Ine ndinati, "Bwana, kodi malamulo a dziko lino sali okhazikitsidwa mwa Baibulo? Ndiyetu ndi chilungamo." Amen!

82 Zedi, chidziwitso_osati cha chidziko, chidziwitso chazimu cha Mawu. Kudziwa chomwe Mulungu ananena. Chita chimene Mulungu ananena_ndiko kulondola. Ndiye ngati iwe uli nazo izo ndipo ukhoza kukhulupirira zinthu zonse izi, kuti Iye ali yemweyo mu zinthu zonse izi; Mawu akuti ndi zowona, iwe umavomereza alionse ndi, "Amen" zonse ziri bwino; wonjezerani icho ku chikhulupiriro chanu. Izo ziri bwino.

Inde, ngati wina wake ayesa kukuwuzani kuti Baibulo linatha mphamvu, palibenso zinthu ngati za Ubatizo wa Mzimu Woyera_musawonjezere zimenezo. Izo sizigwira ntchito. Izo zidzagwapo. Ziri ngati kumata dongo pa thanthwe_ilo silingalimbe. Ilo lidzagumuka.

83 Ndiye anthu amakuwuzani inu, "Baibulo silingaliridwe lero. Inu musamalire tsopano. Musapiteko^" Inu mwakhala mukumva izo nthawi zonse. Kamwambi kakuti: "Inu simungalidali Baibulo." Chabwino, ngati inu muli ndi izo mmalingaliro anu musayese kuwonjezera izo, chifukwa sizigwira ntchito. Nyumba yonse idzagwa pansu pomwepo. Iye ayenera kulumikizidwa mwa Mzimu Woyera_ ndikutanthawuza monga kuphatikizanita limodzi, matope omwe amazimatanitsa izo; ndipo chinthu chomwe chimamatanitsa izo^Inu mukudziwa momwe chubu chomatiridwa chimakhala nthawi yaitali kusiyana ndi chubu chachikale chochita kumamata zigamba_kutentha kwapang'ono kukangofika pa chigamba chakale pa tayalalo, choyamba kuzindikira ndicho teyalalo likayamba kutentha pang'ono, mukathamanga mofulumira pang'ono, icho chidzanyembetelapo.

Inde, bwana. Mwaona? Izo ndi zomwe zikuwavuta anthu ambiri lero: iwo amayesa kuphatika chidziwitso chawo pa chidziwitso chachidziko, ndi kaulimbo kakale kapadziko, ndipo pamene mayesero adza, "Chabwino kapena mwina ine ndinalakwa." Mukuona ndiye mpweya umachoka_inu mumaphwetsedwa mu maminiti ochepa. Kufuula kwanu konse ndi kudumphadumpha sikunakuchitireni inu ubwino uliwonse. Anthu amakuwonani inu mu chithaphwi chomwe chijanso. Ndi zowona! Koma ngati inu mukhala pomwepo ndi kutentha kokwanira kwa Mzimu Woyera mpakana zikupangitsani inu ndi chubu mmodzi! Ndizo izo! Inu ndi chubu mumakhala mmodzi! Pamene inu mukhala pamenepo mpakana inu, ndi lonjezo lirilonse la Mulungu, mukhala mmodzi, ndiye onjezerani icho kwa chikhulupiriro chanu. Ngati inu simutero, musawonjezere icho konse.

84 Inu mukuti, "Mawu sangadaliridwe." Inu musayese kuwonjezera izo. Ngati inu muti, "Malonjezo mkatimu a Ubatizo wa Mzimu Woyera unkatanthauza kwa atumwi khumi ndi awiri okha," monga mipingo ina imatero lero. Musamayese kuwonjezera izo. Apo ndi pamene maziko awo onse anagumukira.

Monga Uziya anali usiku watha, pamene iye anawona maziko a munthu amene iye anamudalira onse atagumuka_kukanthidwa ndi khate. Anali opanda ubwino. Tsopano, "za atumwi khumi ndi awiri basi,

atumwi khumi ndi awiri okha.”

85 Ine ndinali kwa M'bale Wright (Ine ndikuganiza kuti ali kumbuyoko kwina kwake) usiku wina, ndipo kunali mlaliki kumeneko. Ine ndimalankhula alaliki anayi kapena asanu pamodzi. Mlaliki uyu anadzuka nati, “Tsopano, ine ndikufuna kukuwuzani anthu abwino inu chinachake. O, ine ndikuganiza kuti ndinu anthu abwino zedi.”

Ine ndinati, (Ine ndinamuwuza wina wake) “Ndi uyo wakhala apoyo; mupenyetseteni.” Kotero, Junie Jackson, kumbuyoko, anali atangotsiriza kulankhula ndipo iye anati_ (polankhula za chisomo cha Mulungu)^O, mai, iye amangoyaka ndi kuyembekezera. Ndipo iye anafika pamwambapo ndipo iye amayesetsa. Kunena, “Tsopano, ine ndikufuna kunena kuti Bambo Branham, pano, ine ndikukuuzani inu, ndi wotsutsakhristu,” ndipo iye anayamba kulankhula chotero.

Chabwino, alaliki ena anayamba^Ine ndinati, “Tsopano, dikirani miniti, musanene kanthu, abale. Iye ali yekha ndipo ife tiri gulu.” Ine ndinati, “Ingomusiyani yekha tsopano; iye wapalamula ine.” Ine ndinkafuna ine mwini ndiyankhe kwambiri, ine sindinadziwe choti nkuchita, onani.

86 Iye anati, “Bambo Branham ndi wotsutsakhristu,” ndipo iye anapitirira kulankhula chirichonse, inu mukudziwa za^Iye anati, “Ubatizo wa Mzimu Woyera^Baibulo linati panali khumi ndi awiri okha analandira ubatizo wa Mzimu Woyera. Kukamba za machiritso auzimu atumwi khumi ndi awiri amene anali ndi machiritso auzimu.” Iye anati, “Ife timalankhula pamene Baibulo likulankhula, ndi chete pamene Baibulo liri chete.”

Ine ndinadikira mpaka iye atabwebweta pamenepo kwa theka la ora, ndipo ine ndinati, “Dikirani kwa miniti. Ine ndalemba apa zambiri,” ine ndinati, “Ndipatseni ine mwayi woti ndiyankhe zina.” Ndipo pamene ine ndinadzuka ine ndinati, “Abwana, iye wati iwo amalankhula pamene Baibulo likulankhula mpingo wawo umatero mpingo wake umatero_ ndipo anali chete pamene ilo linali chete_inu nonse ndi mboni.” “Inde.” Ine ndinati, “Tsopano, iye anati panali Atumwi khumi ndi awiri okha analandira Mzimu Woyera. Baibulo langa linati anali anthu zana limodzi ndi makumi awiri kuwombera koyamba.”

Amen! Kumuponyera chidziwitso cha mtundu wotero kumeneko, inu mukuona. Kuti iye amayesa ku^

87 Ine ndinati, “Ndiye ine ndikulingalira kuti Paulo sanalandire Mzimu Woyera pamene iye anati analandira. Ine ndinati, “Kuja ku_pamene Filipino anapita nakalalikira kwa Asamaria, iwo anabatizidwa mu Dzina la Yesu kokha; Mzimu Woyera unali usanadze pa iwo, ndipo iwo anatumiza uthenga ndipo anakamtenga Petro ndi Yohane abwere nadzayika manja pa iwo, ndipo Mzimu Woyera unadza pa iwo. Ine ndimaganiza kuti anali anthu khumi ndi awiri okha.” Ine ndinati, “Machitidwe 10:49 pamene Petro anali pamwamba pa nyumba ndipo iye anawona masomphenya kuti apite kwa Korneliyo, pamene Petro anali akulankhula mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo amene anamva Mawuwu.” Ine ndinati, “Baibulo likulankhulabe; mpingo wanu uli kuti? Zabwerera mu “zikanadzakhala.” Zoono, mwaona.

Ine ndinati, “Machiritso auzimu_inu mumati atumwi khumi ndi awiri okha ndi omwe anali ndi machiritso auzimu. Baibulo linati kuti Stefano anapita ku Samaria nakatulutsa ziwanda ndi kuchiritisa odwala, ndipo kunali chisangalalo chachikulu mu mzindawo_ndipo iye sanali mmodzi wa khumi ndi awiriwo. Iye sanali mmodzi wa atumwi_ iye anali dikoni.” Amen!

88 Ine ndinati, “Ndipo Paulo sanali mmodzi wa khumi ndi awiriwo amene anali mu chipinda chapamwamba, ndipo iye anali ndi mphatso ya machiritso.” Ine ndinati, “Tangoyang'anani mphatso za machiritso. Ndipo mpakana zaka makumi atatu zotsatirapo, iye anali adakali ku Akorinto kukhazikitsa mphatso ya machiritso mu thupilo.”

Tsopano, chidziwitso cha mtundu umenewo chimene inu mumachiphunzira mu mabuku ena ake, kuli bwino inu muwataye iwo mu chitini cha zinyalala. Idzani ku chidziwitso ichi_chimene Mulungu anati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse,” nenani, “Amen!” Inde, bwana. Inde, bwana. Osati kwa khumi ndi awiri, ndi kwa onse. Pamene inu muyamba kukhala ndi chikhulupiro cha mtundu umenewo, pamene chikhulupiro chanu chivomereza gawo lililonse ndi “Amen,” ndiye inu mkuti, “Zonse ziri bwino,” onjezerani izo kwa izi.

89 Chachinayi^(Ife tiyenera tifulumire chifukwa ine ndango^) Zikungokhala bwino kuyima pano ndi kumalankhula za izo. Chachinayi (zikomo)^onjezerani kudziletsa. O, mai. Ife tikudza pa kudziletsa. Tsopano, inu muli ndi chikhulupiro poyamba. Inu muyenera kukhala ndi icho poyamba. Ndiye inu muwonjezere ukoma kwa chikhulupiro chanu (ngati uli ukoma woyenera). Ndiye muwonjezere chidziwitso (ngati chiri chidziwitso choyenera). Tsopano, inu muwonjezera kudziletsa.

Kudziletsa sikutanthawuza: kuleka kumwa mowa apa konse. Ayi, ayi. Kudziletsa sikukutanthawuza kuchiza uchidakhwa. Osati mu nkhani iyi. Uku ndi kudziletsa kwa Baibulo_kudziletsa kwa Mzimu Woyera. Ndicho chimodzi chokha cha zokhumba za thupi. Koma ife tikulankhula za kudziletsa kwa Mzimu Woyera. Uko kukutanthawuza momwe mungaligwirire lirime lanu_osakhala wamanong'onong'o; momwe mungagwirire kupsya mtima kwanu, osamangokwera mmwamba nthawi iliyonse pamene aliyense alankhula

motsutsa kwa inu. O, mai, Ambuye, ambiri a ife tigwa pamenepa ife tisanayambe kumene. Sititero ife? Ndiye ife tikumadabwa chifukwa chomwe Mulungu sali mu Mpingo Wake kumachita zozizwitsa ndi zinthu zomwe

90 Iye ankazichita.

Onjezerani zinthu izi. Onjezerani kudziletsa kwa izi. Kudziletsa_momwe ungayankhire mwa chifundo pamene mkwiyo walankhulidwa kwa iwe." Winawake akati, "Inu gulu la odziyeretsa uko." Osadumpha ndi kukwinya mikono yanu, tsopano_osati izo, koma kulankhula ndi chikondi chaumulungu. Kudziletsa_chifundo. Kodi umo ndi momwe inu mukufunira kukhala?

Pamene inu mulalampiridwa, osalalata chobwezera. Lolani Iye akhale chitsanzo chanu. Pamene iwo anati, "Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, sandutsa miyala iyi ikhale mikate." Iye akanakhoza kuchita izo, nawonetsa kuti Iye anali Mulungu, koma Iye anali ndi kudziletsa. Pamene iwo anamutcha Iye, "Belezebule," Iye anati, "Ine ndikukhululukirani inu pakutero." Uko nkulondola? Iwo anamwetula ndevu zodzaza dzanja pankhope Yake namulavulira mu nkhope Yake, ndipo anati, "Tsika pa mtandapo."

Iye anati, "Atate akhululukireni iwowa; iwo sakudziwa konse chomwe akuchita."

91 Pamene Iye anali ndi mphatso_Iye amadziwa zinthu zonse pakuti mwa Iye munali chidzalo cha umulungu mthupi. Iwo anamuwona Iye akuchita zozizwitsa pakuwawuza anthu zomwe zimawavuta iwo, ndi zina zotero, monga choncho. Iwo anayika chinsanza mozunguliza mutu wake chotero, pa maso Ake, namugogoda Iye pamutu ndi ndodo nati, "Nenera; tiwuze ife amene wakumenya Iwe; ife tikukhulupirira Iwe." Iye anali ndi kudziletsa!

Tsopano, ngati inu muli nako kotero; onjezerani iko kwa chikhulupiriro chanu. Ngati inu mukufufumabe, kumenyana, ndi kukangana, ndi kukwiya, ndi kumangopitirizabe. A, a. Inu mulibe ayi^Inu simungawonjezere izo, chifukwa sizingawonjezereke.

Onani, izo sizingawotchererane. Inu simungatenge chidutswa cha rabara, inu mukudziwa, ndi kuwotcherera icho ku chidutswa cha chitsulo. Icho sichigwira ntchito basi. Ayi, chiyenera kukhala chadebadeda monganso rabara aliri, onani. Tsopano pamene chikhulupiriro chanu ndi kudziletsa kwanu kukhala kwa mtundu womwewo wa kudziletsa kwa Mzimu Woyera kumene Iye anali nako, ndiye izo ziwotchererana ndi Iye. Inu mwawonjezedwera kwa icho.

92 Pamene ukoma wanu uli monga ukoma Wake, ndiye iwo udzawonjezedwera kwa icho. Pamene chidziwitso chanu chiri ngati chidziwitso Chake_"Ine ndinadza kudzachita chifuniro Chanu, O Mulungu." Ndi Mawu a Atate, iye anagonjetsa mdierekezi aliyense. Miyamba ndi dziko zidzachoka koma Mawu sadzachoka. Onani pamene inu muli ndi chidziwitso cha mtundu uwo, icho chidzawotchererana ndi chikhulupiriro chanu. Pamene inu muli ndi chipiriro cha mtundu woyenera monga Iye anali nacho; icho chidzawotchererana. Ngati inu mulibe_kungokhala chopangidwa ndi munthu, cholekeza pakati, chikhulupiriro chongoviika, kapena chipiriro_"O, ine ndikanamuwomba khofi iye, koma koma mwina ine ndisatero, chifukwa akhoza kulemba dzina langa mu pepala za izo." Uwo si mtundu woyenera wa chipiriro chomwe Iye ankachinena. Musayese kuwonjezera icho; icho sichigwira ntchito. Koma pamene inu mukhoza kwenikweni mwa kukoma kochokera mu mtima wanu kukhululukira munthu aliyense_gwirani mtendere wanu. Lolani icho kuti chipite, mwaona. Ndiye icho chiwotchererana. Inu mukhoza kuwonjezera icho ku chikhulupiriro chanu.

Fyuu! Ndi zosadabwitsa kuti mpingo uli wosowa choncho.

Kodi izo sizolondola? Ndi zosadabwitsa.

93 Pamene ine nditi, "Lapani ndipo mubatizidwe_Baibulo linati_mu Dzina la Yesu Khristu." ndipo wautatu molimba samakhulupirira izo, akhoza kuti, "Wosutsakhristu wakale uja; Iye ndi wa Dzina la Yesu; Iye ndi wa Yesu yekha." Samalira, mnyamata! Ine sindikudziwa za chipiriro chako pakali pano.

Bwanji iwe usakubwera ndi kunena, "Tiyeni tiringalire ichi limodzi, M'bale Branham. Ine ndikanakonda kumva ichi chikufotokozedwa." Ndiye bwerani kuno ndi kudzamvera kwa ichi; ndiyeno icho chayikidwa patsogolo panu pomwe, ndiyeno inu mumachokapo_ife tifika ku icho mu maminiti angapo chabe, mu umulungu.

Koma pamene inu^pamene inu muchita ukali, kufuna kudumphira potsiriza paliponse, a_a; izo si ndizo. Mwaona? Inu mulibe chipiriro cha Baibulo, apabe pamene inu muchita izo. Momwe mungayankhire wina. Ndiye, ngati inu muli ndi zonse izi, inu mukhoza kuwonjezera ichi kwa chikhulupiriro chanu.

94 Ndiye, zitatha izo, kachinayi, inu mukufuna kuwonjezera chipiriro kwa chikhulupiriro chanu. "Ngati inu muli ndi chikhulupiriro, icho chimayambitsa chipiriro," Baibulo linatero. Kotero ichi ndi chipiriro. Tsopano, icho ndi chinthu chotsatira chomwe chiti chimange thunthu ili. Inu mukudziwa Mulungu ali ndi zipangizo zenizeni mu nyumba Yakeyi. Onani momwe ife titaperewerera, abwenzi. Onani pamene ife tiri? Onani, ife

tiri ndi ulemerero, ife tiri ndi mifuu, ndi zinthu, chifukwa ife tiri ndi chikhulupiriro. Koma pamene ife tibwera mpaka ku zinthu izi apa, Mulungu sangatimangire ife mu thunthu ilo. Iye sangatipange ife mpaka pa malo a mtundu umenewo. Uli ndi zinthu zina zonsezi ife timagwa ndi kutererekerera kutali palimodzi nazo. Mwaona? Iye sangamange Mpingo Wake.

95 Kupirira kwa chiyani? Chipiriro cha mtundu wanji? Choyamba ndi kukhala ndi chipiriro naye Mulungu. Ngati muli ndi chikhulupiriro chenicheni choona, mudzakhala ndi chipiriro chenicheni choona, chifukwa chikhulupiriro chimapanga chipiriro. Pamene Mulungu anena chirichonse, inu mukhulupirira icho. Ndi izo zokha. Inu muli ndi chipiriro ndiye. "Chabwino, ine ndinamufunsa Iye usiku watha kuti andichiritse ine, ndine wodwala chimodzimidzi mmawa uno." O, mai! Chipiriro chanji! Mulungu anamuwuzwa Abrahamu, ndipo patatha zaka makumi awiri ndi zisanu panalibe ngakhale chizindikiro chimodzi; iye anakhulupirirabe izo. Iye anapirira naye Mulungu. Kumuyika Iye nthawizonse patsogolo panu. Kumulola Iye kukhala chinthu chotsatira kuwoloka. Inu simungamuwoloke Iye kotero ingomusiyani Iye patsogolo panu. Iye anatero, tsopano icho chichitika. Msungeni Iye patsogolo panu. Uko nkulondola.

96 Nowa anali ndi chipiriro. Nowa anali ndi chipiriro chenicheni cha umulungu. Mulungu anati, "Ine ndiwononga dziko lonseli ndi mvula," ndipo Nowa analalikirira zaka zana limodzi ndi makumi awiri. Chipiriro chochulukana ngakhale mame sanagwe kuchokera kumwamba. Panalibe kalikonse. Fumbi lokha monga momwe kunaliri kwa zaka zana limodzi ndi makumi awiri, koma iye anapirira.

Ndiye Mulungu amayesa chipiriro chanu. Uko nkulondola. Mulungu amawayesa iwo. Iye atamuwuzwa Nowa, tsopano Iye anati, "Nowa, ndikufuna upite ukalowe mu chombo. Ine ndisakira zinyama mkatimo. Ndikufuna iwe kuti ulowe mkati ndi kukakwera mpaka mu chipinda cham'mwamba, tsono, kuti uziyang'ana kunja kupyolera pa zenera la pamwamba. Tsopano, ine ndikufuna iwe kuti ulowe mmenemo. Ine ndikufuna iwe uwawuze anthu awa; "Mawa chimene ndakhala ndikulalikira kwa zaka zana limodzi ndi makumi awiri chidzachitika." Chabwino, pita kumeneko nukawawuze."

Chizindikiro choyamba chinali chiyani? Nowa analowa mu chombo. Uko kunalibe mvula.

97 Nowa anakonzeka, navala chodzitetezera mvula ndi chirichonse kuti azikhoza kumayang'ana kunja kamodzi pakapita nthawi anakonzeka, koma tsiku lotsatira, mwina analiwuza banja lake ndi azipongozzi ake aakazi ndi ena onsewo anati, "O, mai mawa inu muwona chinthu china chimene simunawonopo konse, chifukwa kumwamba konseko kudzakhala mdima, bingu ndi mphenzi zizidzachitika. Lupanga lalikulu la Mulungu lidzathwanima mmwamba. Iye alanga gulu ili la anthu ochimwa limene latikana ife kwa zaka zana limodzi ndi makumi awiri. Ingoyembekezzerani muwone." Onani, ena mwa okhulupirira mwa theka kukhala ali pafupi ndipo osalowamo konse, inu, mukudziwa; tidakali nawobe iwo, inu mukudziwa.

Kotero iwo anadza nati, "Mwina bambo wokalambayu mwina akulondola, kotero ife tipita komweko ndi kudikira masiku angapo kapena kudikira ma ora angapo mmawa kuti tiwone."

98 Tsiku lotsatira, mmalo mwa mtambo wakuda, dzuwa linatuluka monga momwe limachitira nthawi zonse. Nowa anayang'ana kunja. Nati, "Eee, kulibe ayi mitambo!"

Njonda ina inadza niti, "A-a-a-a-ha, ine ndimadziwa kuti iwe unali mmodzi wa iwo. Ine ndakuwona iwe ukupezeka pano!"

"Chabwino, pepani, Bwana, ha-ha; mwina ndango^Inu mukudziwa mwina ndinangotentheka^ha-ha-ha."

Koma Nowa, iye anali ndi chipiriro. Anati, "Ngati, siinabwere lero, ikhala kuno mawa." Ndiko kulondola. Motani? Mulungu anatero.

"Ndi liti lomwe Iye anakuwuzwa iwe izo, Nowa?"

"Zaka zana limodzi ndi makumi awiri zapitazo. Ndafika mpaka lero, kotero ine ndingoyembezera pano tsopano." Onani, patapita nthawi tikupeza kuti Mulungu wafikanso mpaka kutali kuno kuyembekezzeranso Mpingo, koma zidzakhlapo, inu musadandawule. Iye analonjeza izo.

99 Kuyembekezera nthawi yonse chiwukitsiro. Chidzakhlapo, musadandawule. Mulungu analonjeza icho. Ingoyembekezzerani mopirira. Iwe ukagona tulo; ukhoza kuyamba kuyiwalirako pang'ono zisanachitike, koma inu mudzawuka pa nthawi imeneyo_Iye analonjeza icho. Chomwe timachitcha kugona kwa imfa, mukudziwa; chomwe timachitcha imfa_kungogona pang'ono, kapena kugona mwa Khristu. Palibe chinthu chotchedwa kufa mwa Khristu. Moyo ndi imfa sizimakhalapo limodzi. Mwaona. Iye timangoutsu. Kuutsa kokuti anzathu sangatiyitaneko. Iye ndi Mmodzi yekha amene angayitane. "Iye adzayitana ndipo ine ndidzamuyankha Iye," anatero Yobu. Yobu tsopano wakhala akugona kwa zaka zikwi zinayi. Musadandawule, iye adzawuka, musadandawule. Iye akuyembekezerebe.

100 Nowa amayembekezera; tsiku lachinayi linapita_popanda mvula. Ziri bwino, zichitika basi. Ndikukhoza kumva akazi a Nowa akudza nadzati, "Bambo, mukutsimikizadi?"

“Osalankhula chotero.” Iye anali ndi chipiriro, chifukwa iye anali ndi chikhulupiriro. Inde, bwana, Iye anali ndi ukoma. Iye anali ndi chidziwitso kuti Mulungu amalondola. Iye anali ndi kudziletsa Iye samangonyanyuka nati, “Chabwino, ine sindikudziwa kuti zonsezi ndi zotani. Ine kutchuka kwanga kwatayika pamenepa.” Ayi, ayi. “Anthu sakusamalanso za ine.

Ine ndikutuluka ndipite kunja uko ndikayambirensa mwatopano.” Ayi, ayi. Iye anali ndi chipiriro. Mulungu analonjeza; Mulungu adzazichita. Mulungu adzazichita chifukwa Mulungu anatero.

101 Ine ndikukhoza kumuwona mwana wake akudza nati, “Adadi mukudziwa^”(akusisita dzanja lake pa tsitsi lake lalitali la imvi, mukudziwa, ndipo iye anali wa zaka mazana, mukudziwa atakhala pamenepo) nati, “Ndikudziwa kuti inu ndi khola lakale. Ine ndimakukondani inu, Adadi, koma kodi zingakhale zotheka kuti mungakhale mutalakwitsa pang'ono?”

“O ayi, ayi,”

“Motani?” “Mulungu anatero.”

“Chabwino, Adadi, awa ndi masiku asanu ndi limodzi amene ife takhala muno. Kukhala mu chombo chowuma chachikulu chakalechi, kukhala muno. Ndi chomatidwa paliponse mkati ndi kunja, ndipo ife takhala tikuchimanga zaka zonsezi; ndipo inu munkayima kunjako nkumalalikira mpaka pomwe munayamba imvi, ndi dazi, ndipo ndinu muli apanu tsopano kuyesa kunena kuti zinthu zakuti-zakuti, ndipo anthu kuno akuseka ndi kumaponya matimati ovunda ndi zinthu zina mmbali mwa ichi. Tawonani uko zimene mukuchita. Bwanji inu mukudziwa^”

“Khala wopirira, mwana wanga.” “Kodi inu mukutsimikiza?”

“IYO IDZAVUMBA!”

Mpongozi wake wamkazi anati, “Bambo, inu mukudziwa ine^”

“IYO IDZAVUMBA!”

“Koma ife takhala zaka zonsezi tikuyembekezera; ife takhala tikukonzekera, ndipo inu munatiwuzwa ife kuti ivumba sabata lathalo. Ndipo ife tiri muno, ndipo zitseko zonse ndi zotseka, ndipo ife muno tikungoyendayenda muno ndipo dzuwa likungowotcha molunjika pansipa monga momwe linaliri.”

“KOMA IYO IDZAVUMBA!”

“Inu mukudziwa bwanji?” “Mulungu anatero.”

102 Tsopano pamene inu mukhala chotero, onjezera icho. Koma ngati inu mulibe icho mwa njira iyo, musayese kuwonjezera izo. Sizigwira ntchito. Sizigwira ntchito pa machiritso, sizigwira ntchito pa chinthu chirichonse. Mwaona? Chiyenera kugwirizana ndi mtundu womwewo chomwe chiwotchereredwako. Ndiko kulondola. Muyenera kuwonjezera icho. Kupirira nalo lonjezo la Mulungu. Inde bwana. Nowa anakhulupirira izo ndipo anali ndi chipiriro naye Mulungu kwa zaka zana limodzi ndi makumi awiri.

103 Mose_ iye anali nacho chipiriro naye Mulungu. Inde, bwana. “Mose, ine ndamva kulira kwa anthu Anga. Ine ndawona kuzunzika kwawo. Ine ndabwera kudzawawombola iwo. Ine ndikutuma iwe kumeneko.” Ndipo kusiyana pang'ono pakati pa iye ndi Mulungu, ndipo Mulungu anamuwonetsa iye ulemerero Wake. Iye anati, “Pano ndikupita.” Pamene iye anawona kamodzi ulemerero wa Mulungu, mukuona, iye anali ndi chikhulupiriro.

Anati, “Ndi chiyani icho mu dzanja lako, Mose?” Iye anati, “Ndodo.”

Iye anati, “Iponye iyo pansu.”

Iyo isandulika njoka. Iye nati, “O mai.”

Nati, “Inyamule, Mose. Ngati ine ndikukhoza kuisandutsa iyo kukhala njoka, ine ndikhoza kuisandulizanso.” Amen. Ngati Mulungu angandipatse ine moyo wa chilengedwe, Iye angandipatsenso ine Moyo wauzimu! Ngati Mulungu angandipatse ine kubadwa koyamba, Iye angandipatsenso ine Kubadwa kwachiwiri! Amen! Mulungu angachize uyu ndi machiritso auzimu, Iye akhozanso kumuwukitsa iyenso kwa ulemerero Wake mu masiku otsiriza!

“Ine ndingaponye pansu ndodoyi; iyo nisandulika njoka; ine ndingayibwezerenso iyo kukhala ndodo.”

“Itenge ndi kumchira!” Mose anatambasula dzanja lake nayitenga iyo_ apo inali ndodo. Iye anayamba kuwonjezera chidziwitso ndiye. Mwaona?

“Chavuta nchiyani ndi dzanja lako, Mose?” “Palibe.”

“Liyike mu chifuwa chako.”

“Chabwino, bwanji tsopano?”_layera ndi khate.

“O, Ambuye, taonani dzanja langa!”

“Libwezerenso mu chifuwa chako, Mose.” Kulibwezera chotero_linasanduka chabe monga^

Iye anayamba kuziwonjezerapo monga ichi ndiye. Inde, bwana.

104 Iye anakafika kumeneko, ndipo kusiyana koyamba^iye anakafika kumeneko. Anatulukira kumeneko nati, “Ambuye Mulungu ati, 'Alole anthu anga apite.' Farao, ine ndikufuna iwe udziwe ichi: Ine ndabwera monga woyimira Mulungu. Iwe uyenera kundimvera ine.”

Farao anati, “Kumvera? Kodi iwe ukudziwa yemwe ndiri?”

Ine ndi Farao. Kukumvera iwe_kapolo?”

Anati, “Iwe undimvera ine kapena kuwonongeka. Ukhoza kuchita china chomwe ukufuna kuchitapo.” Bwanji? Iye ankadziwa chomwe ankalanikhula. Iye anali ndi utumiki. Iye anali kumeneko, ndipo iye analankhula kwa Mulungu. Iye anali ndi chikhulupiriro. Iye ankadziwa komwe anali.

“Iwe ukufuna ine ndikumvere iweyo? Choka pano!” “Ine ndikusonyeza iwe.”

“Ndisonyeze ine chizindikiro.” Iye anaponya ndodo pansu; inasandulika njoka.

105 “Bwanji,” iye anati, “amenewo ndi matsenga otchipa a anyanga! Bwera kuno kaye kaminiti. Bwerani kuno Yane ndi Yambure. Ponyani ndodo zanu pansu.” Iwo anaziponya izo pansu, ndipo zinasanduka njoka. Nati, “Tsopano, iwe chinthu chotchipa ungabwere kwa ine, M'Igupto, Farao wa Igupto. Ndiye iwe kubwera kuno ndi matsenga ako ena otchipa a anyanga”_zonama zako zina mukudziwa_kuwerenga maganizo, (Inu mukudziwa chomwe ndikutanthawuza. Ndikuyembekeza kuti mukuwerenga.) Kuwerenga maganizo kapena chinachake. “Kubwera kuno ndi zina za izo.” Nati, “Chabwino, ife tikhoza kuchita chinthu chomwecho ukuchichita.”

Kodi Mose anatani? Iye sanati, “O, Bambo a Farao, pepani, bwana. Ine ndikhala kapolo wanu.” Ayi, bwana. Iye anayima mosagwedezeka! Amen! Anangokhala pomwepo! Mulungu anati_mu mtima wake munalibe kukayika. “Khala bata, ine ndikuwonetsa chinthu china.”

106 Pamene wachita chimodzimodzi ndi chomwe Iye anati uchite: zikuwoneka ngati zalakwika, yima mosasuntha. Khala wopirira. Mose anati, “Inu mukudziwa pamene ine ndimayika pa mazikowo panali chipiriro chinayikidwa pamenepo, kotero ine ndingodikira ndi kuwona chomwe Mulungu ati achite.

Kuja njoka zinali, zikukwawa paliponse, kufufuma ndi kulavulirana ina kwa imzake. Chinthu choyamba inu mukudziwa njoka ya Mose inayamba, “mezu, mezu, mezu,” ndi kuzimeza zonsezo. Iye anali ndi chipiriro.

“Oyembekezera pa Ambuye Adzawonjezera mphamvu zawo.

Adzakwera ndi mapiko monga mphungu.” (Kodi uko nkulondola?)

Adzathamanga ndi kusatopa, Kuyenda ndi kusatha phuma^”

Ingoyembekezera pa Ambuye. Khalani ndi chipiriro.

107 Inde, bwana. Ndiye Israeli amadzatulutsidwa. Zosiyana zopambana zinadza ndipo Mose anayembekezera. Ndiye iye analowa mu chipululu. Ndi ulendo wa pafupi masiku atatu kapena anayi okha_ndi mailosi makumi anayi okha kuchokera pamene iye anawolokera paja, kudutsa ndi njira yomwe anadzerapo kale_koma Mose mu Chipululu anayembekezera zaka makumi anayi. Kupirira, uko nkulondola. Iye anayembekezera zaka makumi anayi. O, inde, bwana.

108 Ndipo ife tizikhala ndi chipiriro naye wina ndi mzake, nafenso. Nthawi imodzi, ife timakhala osapirira kwambiri kwa wina ndi mzake. Ife tikuganiza tiyenera kukhala monga Mose. Mose anali ndi chipiriro nawo anthu. Yang'anani, izo ndi zomwe zinawachititsa iwo kuti asawoloke. Onani, ngati inu mukuyesa kuchita chinachake_monga momwe ndayesera kupereka Uthenga uwu kwa Kachisi, uyu kuti ndiwone kuti membala aliyense wa mu Kachisi, uyu akhale ichi. Ndi zovuta kuzichita. Ndayesa kukhala ndi chipiriro_izino ndi zaka makumi atatu ndi zitatu. Kukhala ndi chipiriro. Akazi akudulabe tsitsi lawo (chimodzimodzibe). Koma kungokhala ndi chipiriro_kungokhala ndi chipiriro, kuyembekeza. Uyenera kutero. Ngati ulibe icho, usayese kumanga pa zinthu izi pansipa. Khala ndi chipiriro.

109 Ngakhale nthawi imodzi pamene gulu lowukira lija linalibe kupirira chotero iwo anachititsa Mose kuchita chinthu china chomwe chinali cholakwika. Komabe pamene zinafika pa chiwonetsero, Mulungu zimamunyansa zochita zawo. Iye anati, “Dzipatule wekha, Mose. Ine ndipha gulu lawo lonseli ndi kuyambanso mwatsopano.”

Iye anadziponyera yekha pakati nati, "Mulungu, musachite izo." Bwanji? Kupirira ndi anthu amene anali kumuwukira iye.

Ine ndikudabwa ngati ife tingachite izo? Ngati simungatero, musayese kumanga pa izi, chifukwa sizimasintha. Umo ndi momwe choyamba chija chinawotchereredwa ku ichi, ndipo umo ndi momwe aliyense wa iwo ayenera kuwotchereredwa. Ngati siutero, iwe siufika pa thunthu la malo okhalamo Mulungu Wamoyo. Iwe ulibe kupirira. Kupirirana wina ndi mzake.

110 Chabwino, ana a Chihebri anali ndi chipiriro. Zedi anali nacho. Mulungu anawalonjeza iwo_anawawuza iwo, "Musagwadire konse fano lirilonse." Koma iwo anali ndi chipiriro. Anati, "Mulungu wathu akhoza, koma ngakhale asatero ife sitigwadira fano lanu." Kupirira_kudziwa ichi, kuti Mulungu adzawawukitsa iwo mu masiku otsiriza. Moyo uwu sutanthawuza zambiri ngakhalebe. Mukuona? Mulungu adzalidzutsanso mu masiku otsiriza, koma, zikakhala zogwadira fano, ife sitichita izo.

"Tsopano, ife timupatsa Kaisara zomwe ziri za Kaisara, koma pamene zikadza pa kuti Kaisara azilowerera za Mulungu, Mulungu akhale woyamba. Mulungu anati, "Inu musagwadire fano ilo; ndipo ine sindichita izo. Mulungu wathu akhoza kutiwombola ife, ndipo ngati Iye satero, ine sindigwadira fano."

Iye anati, "Chabwino, ng'anjo ndi iyo apo."

"Chabwino," iye anati, "Ine ndikungoganizira kuti ivumba kwambiri usiku uno ndikuwuzimitsa wonse," koma sinatero. Wopirirabe.

111 Mmawa wake pamene zinafikitsidwa ku bwalo, uko kunali Nebuchadnezzar; iye anati, "Chabwino, anyamata, kodi mwakonzeka kundikumbukira ine monga mfumu yanu?"

"Zedi, khalani ndi moyo kwa nthawi zonse, o, mfumu." "Tsopano, gwadirani kwa fano langa."

"O, ayi!"

"Chabwino, inu mukawotchedwa. Inu ndi anthu anzeru ndinu ochenjera. Inu mwakhala othandiza kwambiri kwa ife. Inu mwakhala dalitso, kwa ufumu wathu. Simungamvetse inu kodi kuti ine sindikufuna kuchita izi, koma ine ndalengeza apa kwa onse, ndipo ziyenera kuchitidwa. Ine sindikufuna kukuponyerani inu mkatimo. O anthunu, chakuvutani ndi chiyani inu?"

"Ine ndikudziwa izo zikumveka bwino, koma Mulungu wathu akhoza kutiwombola ife komabe^" Kukhala ndi chipiriro. Kotero anayamba kuyenda wa ku ng'anjo; akuyang'anana wina ndi mzake," Zonse ziri bwino? Zonse ziri bwino. Tiri nako kupirira." Anapita sitepe imodzi_Mulungu panalibe. Masitepe awiri_Iye panalibe. Masitepe atatu^ masitepe anayi^masitepe asanu; ankangopitirira_komabe Iye panalibe; ndipo iye anapatuka nalowa mu ng'anjo yamoto. Iwo anali ndi chipiriro; koma Iye anali mmenemo. Onani, moto wokwanira unawafika nungowotcha zingwe pa mikono yawo ndi mapazi, ndiyeno pamene iwo anagunda pansu pa dzenje, Iye anali pamenepo. Iwo anali ndi chipiriro.

112 Daniele, njira yomweyo. Daniele anali ndi chipiriro. Zedi. Iye sakanadzalekerera. Ayi, Bwana. Kodi iye anachita chiyani?_anatsigula mawindowo napemphera basi_chinali chofunika cha Mulungu. Iye anali ndi chipiriro. Iye anayembekezera pa Mulungu, kudziwa Mulungu anali wokhoza kusunga Mawu Ake, Iwo anamuponya iye mu khola la mikango; nati, "Ife tisiya kuti mikango ikudye."

Iye anati, "Zonsezo nzabwino." Iye anali ndi chipiriro. Bwanji? "Chabwino, ine ndakhala ndikuyembekezera nthawi yonse pa Mulungu. Ngati ine ndiyenera kuyembekezera zaka zikwi zingapo zina, ine ndidzawukitsidwanso mu masiku otsiriza, kotero ine ndiri ndi chipiriro; kungodikira."

Paulo anali ndi chipiriro. Ndithudi anali. Yang'anani zomwe Paulo anasowa kuchita.

113 Kunena za kupirira; nanga bwanji anthu a Chipentekoste? Bola iwo ali ndi ulamuliro, "Dikirani mpakana_dikirani mpakana mutavekedwa ndi mphamvu."

"Motalika bwanji?"

"Sizofunsa kutalika komwe kuti kudzakhale"_iwo anangokhala ndi yankho. Dikirani mpakana. Iwo anapita mmwambamo nati, "Chabwino, anyamata, mwina pa maminiti khumi ndi asanu tsopano Mzimu Woyera akhala pa ife, ndipo tikhala ndi utumiki wathu." Maminiti khumi ndi asanu anadutsa_palibe. Tsiku limodzi linapita_popanda mmodzi.

Awiri, atatu, anayi, asanu, asanu ndi limodzi, asanu ndi awiri. Ena a iwo akanakhoza kunena, "Hei, kodi inu simukuganiza kuti tiri nawo kale?"

"Ayi, ayi, ayi, ayi."

"Kuli bwino mutuluke kunja, anyamata."

Mdierekezi anati, "Inu mukudziwa kuti muli nacho kale chimene mukuchifuna. Pitani kayambeni utumiki wanu."

"Ayi, ayi, sitinakhale nawobe, chifukwa Iye anati, 'Kudzabwera ujeni^(zomwe ziti zidzachitike mu masiku otsiriza). Ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena ndidzalankhula kwa anthu awa, ndipo uku ndi kupuma komwe Ine ndinati'." (Yesaya 28:19) Iye anati, ichi ndi icho. Inu mudzakhala nawo pamene_inu nonse mudzadziwa pamene ubwera. "Ife tidzadziwa pamene iwo ubwera. Ife tidzadziwa iwo_wolonjezedwa ndi Atate." Iwo anayembekezera masiku asanu ndi anayi, ndiyeno pa tsiku la khumi_tsopano inu muli pamene; iwo anali ndi chipiriro kuti adikire.

114 Tsopano, ngati inu muli ndi chipiriro cha mtundu umenewo Mulungu atakupatsani inu lonjezo nimuliwona mu Baibulo_"Ndi langa;" ndiye dikirani. Ndiye ngati inu muli ndi chipiriro cha mtundu umenewo, onjezerani icho ku chikhulupiriro chanu. Kodi mukuwona momwe mukukwerera mmwamba tsopano? Inu mukufika pamwamba pano tsopano. Chabwino. (Mivi ya wotchi ikufika poti yazunguliranso.)

Chabwino, onjezerani ichi kwa chikhulupiriro chanu, nthawi zonse kumuyika Iye patsogolo panu, kukumbukira, ANALI IYE AMENE ANALONJEZA. Sindinali ine amene ndinalonjeza; sanali m'busa amene analonjeza, (M'bale wathu Neville); sanali mlaliki wina amene analonjeza; sanali wansembe wina kapena papa; sanali munthu wa pa dziko; anali Mulungu, anapanga lonjezo, ndipo Mulungu akhoza kusunga chirichonse Iye analonjeza.

115 Chabwino, ngati inu muli ndi chikhulupiriro cha mtundu umenewo ndi kudziwa kuti Mulungu analonjeza icho^Kuti, "M'bale Branham, ine ndikudwala. Ine ndikusowa machiritso kwambiri zedi." Landira iwo. Ndi mphatso yopatsidwa kwa iwe. Inde, bwana, ngati inu mutakhulupirira. "Chabwino," inu mukuti, "ine ndikukhulupirira." Ndiye iwalani izo. Ndizo zonse. Izo zonse zatha. Onani, khalani ndi chipiriro.

Ngati muli ndi chipiriro_ngati simuli, ndiye inu mukugumula chimango ichi. Zigwetsa zina zonsezi pansipa; chinthu chimodzi chokha. Muyenera kukhala nacho icho. Musawonjezere icho, chifukwa chidzagwetsa nyumba yanu. Ngati mulibe chipiriro_ngati mulibe ukoma kuti muwonjezere ku chikhulupiriro chanu (chomwe mukuti muli nacho) ndipo ngati inu mulibe chikhulupiriro ndi kuyesa kuyikapo ukoma, zigumulira chikhulupiriro chanu pansi. Kotero inu mukuti, "Chabwino tsopano, dikirani kaminiti. Mwina zonse izi ndi kuphonyetsabe. Mwina Mulungu si Mulungu. Mwina kulibe Mulungu ayi." Onani, muswa chinthuchi pawiri ndithu. Mwaona?

116 Koma ngati inu muli ndi chikhulupiriro chenicheni, ndiye ikani ukoma weniweni kwa icho, ndiye chidziwitso chenicheni, ndiye kudziletsa kwenikweni, ndiye chipiriro chenicheni. Mukuona? Inu mukuyendabe pa mzere.

Chabwino, kachisanu, onjezerani umulungu. O mai. Umulungu uwonjezedwe. Kodi umulungu umatanthawuza chiyani? Ine ndinayang'ana mu madikishonare anayi kapena asanu ndipo sindimakhoza kupeza konse chomwe umatanthauza. Potsiriza, ndinali kwa M'bale Jefferies uko_ tinapeza mu dikishonare. Umulungu umatanthawuza kukhala monga Mulungu.

O, mai. Utakhala ndi chikhulupiriro, ukoma, chidziwitso, kudziletsa, chipiriro, ndiye khala monga Mulungu. Fyuu! Inu mukuti, "Ine sindingathe kuchita izo, M'bale Branham." O inde mungathe. Lolani ndikuwerengereni Malembo angapo pano kaminiti chabe_Mateyu 5:48. Ife titenga ili kuti tiwone momwe likumvekera_Mateyu 5:48_tiwone ngati ukuyembekezeredwa kukhala monga Mulungu. Inu mukudziwa Baibulo limati, "Inu ndinu milungu." Yesu anatero. Bwanji? Ukoma wonse^Zinthu zonse zomwe ziri mwa Mulungu ziri mwa inu. Mateyu 5:48. "Khalani inu^" (Yesu akulankhula pa chiphunzitso cha pa phiri) "Khalani inu kotero" A-N-G-W-I-R-O_(nchiani icho "Angwiro, monga Atate anu Kumwamba ali angwiro." Mwafika pamwamba pomwe apa tsopano musanati muchite izo. Zinthu zonse izi ziyambe zawonjezedwa poyamba. Ndiye timafika pamwamba apa, Iye wakufunsani tsopano kuti mukhale angwiro_umulungu_ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Uko nkulondola. Ndinene zinthu zingati ine ndikananena pa mzere umenewo.

117 Tiyeni titembenzire ku Aefeso 4 ndi kupeza apa chimene_mu Bukhu la Aefeso ananena za chinthu ichinso, za momwe ife tiyenera^momwe ife tiyenera kuchita. Aefeso mutu 4 ndipo kuyambira ndi ndime ya 12. Aefeso 4 kuyambira pa ndime 12. Chabwino, tiyeni tiyambire pamwamba apa ndime ya 11.

"Ndipo iye anawapatsa ena akhale atumwi; ndi ena, aneneri;" (kumbukirani usiku watha_musamayese kutenga udindo wa munthu wina) "ndipo ena, alaliki; ndipo ena, abusa ndi ena aphunzitsi;

Kwa ungwiro wa Mulungu," (Kodi zikuwerengeka chotero? Ungwiro wa chiyani? Oyera_Oyera ndi ayani?_Iwo oyeretsedwawo.)

Iwo amene anayambira pansi apa. "Ungwiro wa oyera, kwa ntchito ya utumiki," (utumiki wa Yesu Khristu) "kwa kumangiriza kwa thupi la Khristu:" (kwa kumangiriza, kumanga cha mmwamba, kumangiriza)

"Mpakana^Mpaka ife tonse tifika mu chiyanjano cha chikhulupiriro, ndi [cha] chidziwitso cha Mwana

wa Mulungu, mpaka kwa munthu wangwiro,” (mpaka ku chitsimikiziro, o, mai) “mpaka ku muyeso wa thunthu la chidzalo cha Khristu:”

118 Ungwiro; umatengera umulungu. Muyenera kuwonjezera ku chikhulupiriro chanu, umulungu. Onani kuti mumayambira pansipa ndi ukoma, ndiye mumapita ku chidziwitso, ndiye mumapita ku kudziletsa, ndiye kupita ku chipiriro, tsopano muli pa umulungu_umulungu. O, mai, nthawi yathu ikupita, koma inu mukudziwa chomwe umulungu ukutanthawuza. Inu mumayimba nyimbo:

“Mongatu Yesu, Mongatu Yesu;

Pansi pano ndifuna kukhala monga Iye. Paulendo wamoyo wanga wonse Kuchokera pansi mpaka ku Ulemerero, Ndikungofuna ndikhale monga Iye.”

Ndiwo umulungu. Pamene Iye anamenyedwa pa mbali imodzi ya nkhope, Iye anatembenusa inayo. Pamene anamunenera mwankhaza, Iye sanalankhule, Iye sanabwezere mwano. Onani, mwaumulungu. Nthawi zonse kuyang'anira chinthu chimodzi. “Ine nthawi zonse ndimachita izo zimene zimakondweretsa Atate.” Inde, bwana, nthawi zonse; ndiwo umulungu.

119 Onani, inu mukakhala mutachokera apa, kufika apa, kufika apa, kufika apa, kufika apa, kufika apa; tsopano mukubwera kudzalowa mu thunthu lonse, tsopano, la mwana wa Mulungu. Koma inu muyenera kukhala ndi ichi, kuwonjezera zonse izi ndipo simungayambe konse mpaka mutapeza ichi.

Tsopano, kumbukirani mbalame yakuda ndi nthenga za pikoko. Musamuyiwale iyeyu onani. Musayese kuwonjezera izi mpaka mutabadwanso kwenikweni, chifukwa sizigwira ntchito. Simungazipangitse izo kugwira ntchito. Zifika ku ichi kapena ku ichi apa izo zigumuka pena pake. Koma pamene mufika pansi apa pa kubadwa mwatsopano kwenikweni kwa nkunda, ndiye inu simumawonjezera kalikonse. Izo zimawonjezekerera kwa inu, kumabwerabe mmwamba.

120 Chabwino, kubwera mu ungwiro tsopano. Chabwino, ndiye ka chisanu ndi chimodzi, tiyeni tiwonjezere (Baibulo apa linati kuwonjezera) chikondi cha pa abale_chifundo cha pa abale. Tsopano, icho ndiye chabwino. Pomwe apa, cha chisanu ndi chimodzi. (Chachisanu ndi chiwiri) Chabwino, kuwonjezera chikondi cha pa abale. Chabwino, tikafika mpaka apo, (chikondi cha pa abale) dziyikeni nokha mmalo ake pa nkhaniyo. Tsopano, inu mukuti, “M'bale wanga anandichimwira ine,” anatero Petro, “Kodi ndimukhululukire iye?” Iye anati, “Kasanu ndi kawiri pa tsiku?”

Iye anati, “Makumi asanu ndi awiri, kasanu ndi kawiri.”

Onani, chikondi cha pa abale. Tsopano, inu onani, ngati m'bale wasokonezeka mmayendedwe, musakhale osapirira naye. Ayi. Mchitireni iye chifundo. Pitani basi.

121 Wina anatero osakhala kale, anati, “Inu mungakhulupirire bwanji zinthu izi mwa njira yomwe mukuchitirayi ndi kumapitabe kwa Assemblies of God ndi a Oneness ndi malo ena onsewo?” Chikondi cha pa abale kuyembekezera kuti tsiku lina^kupirira naye, kudziletsa_kupirira naye; chidziwitso kumvetsa chomwe iye amakhulupirira, ndipo kumbukirani ndi mu mtima mwake, ndi chomwe chiri; ukoma mwa inuyo, kuulola kuti utuluke ndi chifundo, kufatsa naye, kukhala ndi chikhulupiriro kuti tsiku lina Mulungu adzamubweretsa mkati. Chikondi cha pa abale_chinthu cha chisanu ndi chiwiri. Chimodzi, ziwiri, zitatatu, zinayi, zisanu, zisanu ndi chimodzi, zisanu ndi chiwiri. Zinthu zisanu ndi ziwiri.

Ndiye, tsopano inu mukudzano. Chinthu chotsatiranso onjezerani chifundo, chomwe chiri chikondi. Uwo ndi mwala wa pamutu. Limodzi la masikuwa mu mpingo^

122 Tsopano, chonde (zidziwidwe pa tepi^kwina kulikonse ine sindikuphunzitsa) izi monga chiphunzitsa_chomwe nditi ndinene tsopano. Koma ine ndikungofuna kukusonyezani inu izo, mwa chithandizo cha Mulungu, chomwe chiri kwenikweni kuti Baibulo loyamba limene Mulungu analilemba linali Zodiac mu mlengalenga. Ilo limayamba ndi namwali. Limatsiriza ndi Leo mkango. Ndipo pamene nditi ndifike mu Chisindikizo cha Chisanu ndi chimodzi ndi cha Chisanu ndi chiwiri, mudzapeza kuti pamene Chisindikizo chinacho chinatsegulidwa, chidindo cha Zodiac cha pamalo amenewo chinali khansara, nsomba zopingisana. Ndiwo m'badwo wa khansara umene tikukhalamowu tsopano. Kuwululidwa. Ndipo chinthu chotsatira chake chisindikizo chitamatulidwa, chinawulula Leo mkango_kudza kwachiwiri kwa Khristu. Iye anadza koyamba kwa namwali; akudza kenaka Leo mkango. Ine ndidzabweretsa izi mu izi^Tsopani, ine sindiku_kaya tikhala ndi nthawi mmawa uno^ndichita chomwe ndingathe kuti ndikuwonetseni inu kuti masitepe awa ali mu Mapiramidi mongofanana_Baibulo lachiwiri analilemba Mulungu. Enoki analemba ilo naliyika mu chipiramidi.

123 Ndipo chachitatu, (Mulungu nthawi zonse amakhala wangwiro patatu) ndiye Iye anadzipangira Yekha Mawu Ake. Tsopano kumbukirani, mu piramidi,^(ine ndikuganiza ambiri a asirikali inu ndi ena munali ku Igupto) Chipiramidi chiribe mwala wa pamwamba pake. Siunakhalepo konse. Mwalawo unali wosongoka ndi chirichonse chomwe iwo ali nacho, komabe^

Ngati inu muli ndi dola ya pepala mthumba lanu, inu muyang'ane pa pepala ya dolayo ndipo mupeza kuti cha ku dzanja lamanja ili ndi mphungu ndi mbendera ya Chimereka. Ndipo apo anati. "Chisindikizo cha United States." Ku mbali inayo ili ndi piramidi ndi mwala wapamwamba pake waukulu womwe uli ndi diso la munthu; analemba ku mbali iyi. "Chisindikizo Chachikulu." Chabwino, ngati lino liri fuko lalikulu, chifukwa chiyani chisindikizo ichi sichiri pa zisindikizo zake, za fuko? Mulungu anawachititsa iwo kuti achitire umboni ziribe kanthu komwe iwo apita.

Ine ndinkalankhula kwa dokotala nthawi yina, ndipo iye ankangondinena mopsyetsa mtima pa za machiritso auzimu.

Tinali titayima pa msewu. Iye anati, "Bambo Branham, inu mumangowasokoneza anthu." Nati, "Kulibe machiritso, kupatula mwa mankhwala."

124 Ine ndinapotoloka ndipo ndinayang'ana pa chisindikizo chake pa galimoto_chinali njoka yozengezedwa pa mtengo. Ine ndinati, "Chotsani kaye chizindikiro icho pa galimoto chifukwa chizindikiro chanu chomwe chikuchitira umboni kuti Mulungu ndi mchiritsi." Dokotala weniweni amakhulupirira izo. Awa ndi awambawo. Njoka pa mtengo_ Mose anakweza njoka pa mtengo nati, "Ine ndi Ambuye amene ndimachiza matenda anu onse," ndipo iwo anayang'ana pa njoka imeneyo kuti achiritsidwe mwauzimu. Ndipo komabe iwo akuchita umboni wotsutsa iwo; komabe chizindikiro chawo chomwe chikuchitira umboni wowatsutsa iwo!

125 Kuno fuko lathu likunena zinthu zomwe iwo ali, ndi kumazinyoza zinthu izi, ndipo ndalama yawo yomwe (ndalama zawo) zikuchitira umboni kuti Chisindikizo cha pansi ponse pano ndi Mulungu. Mukuona diso ilo liri pamwamba pa dola ya pepala? Ndicho chisindikizo chachikulu.

Icho chinali chisanayikidwe pamwamba pa piramidi. Iwo samakhoza kumvetsa. Bwanji? Mwala wodzavundikira pamwamba unakanidwa, mutu_Khristu. Koma iwo udzabwera tsiku lina.

126 Tsopano pomanga ukoma. Pomanga chimango ichi. Kumanga choyimikidwa ichi. Onani chikuyambira pa maziko a chikhulupiriro_ukoma, chidziwitso, kudziletsa, chipiriro, umulungu, chikondi cha pa abale. Tsopano icho chimachita chiyani? Ndiye akuyembekezera mwala wa pamutu umene uli chikondi; pakuti Mulungu ndi chikondi, ndipo Iye amalambulira, ndipo Iye ndi mphamvu ya iliyonse mwa zinthu izi. Inde bwana. Momwe muno. Onani, ine ndiri nazo pakati pa ntchito zonse izi umu, ndipo apa timafunde iti tikutsatirato. Ndi chiyani izo? Mzimu Woyera kubwera pansi kupyolera mwa Khristu Mzimu Woyera. Mzimu Woyera uli pamwamba pa zonsezi, kuwotcherera izi limodzi. Kumanga chiyani? Mpingo wangwiro kuti mwala wa pamutu udzavindikirepo! Wakhala ukuchitanso chiyani? Iwo wakwaniritsidwa kupyola mu Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo ndi atumiki Asanu ndi awiri a Mpingo.

127 Iwo unayambira mmbuyo apa^Mpingo unakhazikitsidwa kuti poyamba? Mpingo wa Pentekoste unakhazikitsidwa kuti poyamba_ ndi Paulo Woyera ku Efeso. Nyenyezi ya M'badwo wa Mpingo wa Aefeso_Efeso. M'badwo wa Mpingo wachiwiri unali Smurna_ukoma. Ireniasi_ mwamuna wopambana amene anaugwira kwambiri Uthenga wa Paulo. M'badwo wa Mpingo wotsatira unali Pergamo, amene anali^Marteni anali mwamuna wopambana amene anakhazikika. Paulo, Ireniasi, Marteni, kenako ku Tiyatira, anadza Kolamba. Kumbukirani, apa zinajambulidwa pomwepo. Kolamba. Atatha Kolamba, ndipo mibadwo ya mdima inadza, ndiye nkudza Sarde chomwe chimatanthawuza imfa_Lutera. Aleluya! Kenako chiyani? Chinabwera kenako ndi chiyani? Atatha Sarde, Lutera. Ndiye anadza Filadefiya_umulungu. Wesile_chiyero. "Olungama akhala ndi moyo mwa Chikhulupiriro," anatero Lutera. Chiyeretso kupyolera mwa Wesile. Ndiye kunadza Chikondi cha pa abale kupyolera mu Laodikaya, ndipo ife tikukhulupirira Uthenga wopambana kuwonekera kachiwiri kwa Eliya, mmasiku otsiriza, udzasesa dziko lonse.

128 Ndi inu apa_Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo, masitepe asanu ndi awiri. Mulungu kumanga Mpingo Wake kuli ngati munthu mmodzi mwa iyeyekha_mwa Iyemwini. Ulemerero, mphamvu ya Mulungu kubwera pansu kupyola mu ichi, kutiwotcherera ife limodzi. Koteru, anthu Achipentekoste atulutsa Aluterani, atulutsa Achiwesile ndi zinthu_sakudziwa za chomwe akulankhula. Mukuona, iwo akukhala mu gawo ili la kachisi. Umo ndi momwe anthu ena amakwerera pamwamba chotero kenako nkugwapo. Koma pali gawo lenileni la izo lomwe limangopitirira kumanga chimangocho. Tiyeni, "Ine ndidzabwezeretsa," atero Ambuye.

Inu mukukumbukira izo_Mtengo wa Mkwatibwi? Inu mukukumbukira ulaliki wa "Mtengo wa Mkwatibwi? Iwo anawudya mpaka pansu, koma Iye amawusadza iwo. Iwo unali ndi nthambi za zipembedzo; Iye anazisadzapo izo. Iwo anayambitsa mpingo wina, nthambi za zipembedzo; Iye anazisadzapo izo. Koma mtima wake wa mtengowo unapitiriza kukula. Nthawi ya madzulo kudzakhala kuwala. Mwaona? Ndi pomwe amadza Khristu Mzimu Woyera. Yesu amatsika nadzikhazika Iyeyekha pa mutu wa Mpingo, ndiye Iye adzawukitsa Mpingo uwo pokhala thupi Lake lomwe. Mmenemo muli thupi, ndipo momwe Mulungu akuyembekezera ife monga munthu payekha kuti tidzikula ndi chotero_njira yomwe Iye wadzeretseramo Mpingo Wake kuti ukule. M'badwo wa Mpingo uliwonse_iwo umasandulika Mpingo umodzi waukulu.

129 Onani, anthu awa sankasowa zomwe anthu awa anali. Awa sankasowa zomwe awa anali. Onani, koma Iye anakulitsa Mpingo Wake chimodzimodzi^Iye anakulitsa Mpingo Wake chimodzimodzi ndi momwe

Iye akukulitsira anthu Ake. Ndiye Petro apa anati koyamba: (zinthu zisanu ndi ziwiri) chikhulupiriro, ukoma (mwaona, kukwera mmwamba) chidziwitso, kudziletsa, chipiriro, umulungu, chikondi cha pa abale ndi chifundo cha pa abale NDIYENO chikondi cha Mulungu; Mzimu Woyera. Khristu mwa umunthu wa Mzimu Woyera amadza pa inu mwa ubatizo woona wa Mzimu Woyera, ndipo inu muli ndi zimphamvu zonsezi zitasindikizidwa mwa inu, ndiye Mulungu amakhala mu kachisi, wotchedwa chimango_Kachisi Wamoyo wa Mulungu Wamoyo momwe akhalamo.

130 Pamene munthu akhala ndi zinthu izi za mtundu uwu, ndiye Mzimu Woyera umadza pa iye. Ziribe kanthu, mukhoza kulankhula ndi malirime, mukhoza kuchita mowonera mphatso iliyonse imene Mulungu alinayo. Inu mukhoza kuchita izo, koma mpaka mphamvu izi apa zilowa mwa inu, mudakali kunja kwa maziko enieni a chikhulupiriro. Koma pamene mphamvu izi zikula mwa inu, ndipo inu mutawonjezera icho pa icho, ndiye ndinu chimango Chamoyo. Inu ndinu fano Lamoyo loyenda.

Inu mukudziwa, achikunja, iwo amadzigwetsera chafufumimba pamaso pa fano (mulungu wongomuganizira) ndipo mwa njira yongoganizira, iwo amakhulupirira kuti mulungu wongoganiziridwayo amalankhulanso kwa iwo. Izo ndi zachikunja.

Icho ndi Chiroma. Iwo amagwada pamaso pa oyera a mitundu yonse ndi china chirichonse. Iwo ali ndi Cecelia Woyera, Nyumba ya Mulungu, ndi zinthu zambiri zosiyana zotero; iwo amazigwadira izo namakhulupirira kumene izo mwa njira yoganizira. Chotani^Ndi choyimira chotani ichi cha Mulungu Wamoyo woona.

131 Koma pamene ife, osati mwa njira yongoganizira, koma kudzigwetsera tokha pamaso pa Mulungu Wamoyo, ukoma wamoyo, chidziwitso chamoyo, chipiriro chamoyo, umulungu wamoyo, mphamvu yamoyo, kubwera ndi Mulungu Wamoyo kumapangitsa munthu wamoyo fano lamoyo_thunthu la Mulungu!

Kodi Iye akuchita chiyani? Zinthu zomwezo zimene Yesu anachita. Kuyenda chimodzimidzi momwe Iye ankayendera. Kuchita zinthu zomwezo Iye anachita, chifukwa sizinthu zongoganizira. Pali chenicheni chimene chikutitsimikizira!

Mukuona zimene ine ndikutanthawuza? Onani momwe ukoma, zida zomangira izi, zinayimiridwa ndi atumiki a Mpingo, ndi Mibadwo ya Mpingo?

Tsopano limodzi la masiku awa ife tidzatenga limodzi palokha la mawu awa ndikuwaphunzira ndi kuwonetsa kuti akutsimikizira izi. Izi zonse zimayendera palimodzi. Zedi. Mukuona? O mai, ndi zodabwitsa chotani izo, kuwona zomwe_zomwe zimachita.

132 Tsopano, iyo ndi nyumba imene Mulungu amakhalamo_ osati nyumba yokhala ndi belo lalikulu pamwamba pake ndi chichiri chachitali, mukuona, koma, "thupi inu mwandikonzera ine." Thupi lomwe Mulungu angakhalemo, Mulungu angayendemo, Mulungu angapenyere, Mulungu angalankhuliremo, Mulungu angagwiriremo ntchito_Amen! Chida Chamoyo cha Mulungu. Mulungu kuyenda pa mapazi awiri mwa inu. Ulemerero! "Mapazi a wolungama amatsogozedwa ndi Mulungu," Mulungu kuyenda mwa inu, "pakuti inu ndi akalata olembedwa, owerengedwa ndi anthu onse." Ndipo ngati Moyo umene uli mwa Khristu ukhala mwa inu, mudzawonetsera Moyo umene Khristu anawonetsera.

133 Monga momwe ndakhala ndikulankhulira nthawi zonse: Mukachotsa utomoni womwe uli mu mtengo wa pichesi, ndipo ngati mutawusamutsa uwo nkuwulowetsa mu mtengo wa apulo, mtengo wa apulo, ukhoza kumabala mapichesi. Zedi, ndithudi ukhoza. Ngakhale nthambizo ziziwoneka motani, ziri ndi utomoni wa maapulo mwa iwo. Onani, kapena chirichonse chomwe mtengowo uli. Mukatenga moyo womwe unali mu mtengo wa apulo, kuwuchotsamo wonse, ndi kuwupatsa, "kulowetsa kwa utomoni," ndi kukhuthulira mtengo wa pichesi mu mtengo wa apulo_chichitike ndi chiyani? Iwo siwuberekanso mapichesi. Mwaona? Ayi, Bwana. Siu^Ngati moyo wa mtengo wa pichesi udza mu mtengo wa apulo, kani, iwo siudzabalanso ma apulo. Uzidzabala mapichesi, chifukwa uli ndi moyo mkati mwakemo.

134 Mukatitenga ife, amene sikanthunso ayi koma "mphonda zakuthengo," "zipwiza," ndipo palibe kalikonse kwa ife, pakuti ife tonse tiri akufa mu uchimo ndi zolakwa. Ife tonse tiri mu zikhaliidwe za mitundu iyi, ndiyeno ife, eni athu, tikhoza kudzigwetsa tokha, kudzipereka tokha, mpakana Mulungu atenga chubu Chake cholowezanitsira_Dzina la Yesu Khristu, (chifukwa palibe dzina lina panso pa Thambo limene munthu angapulumsidwe nalo)_ndi kusamutsa Moyo wa Khristu kulowa mwa ife, ndiye ife tiri ndi chikhulupiriro cha mtundu uwu_chikhulupiriro chomwe Khristu anali nacho. Ndipo chikhulupiriro cha Khristu sichinali chokhazikitsidwa mwa Afarisi aja kapena Asaduki, kapena mu mapoto awo, maketulo, ziwaya, kapena mu kusamba kwawo. Icho chinali chokhazikitsidwa pa Mawu a Mulungu. Amen! Mochuluka chotero mpaka Khristu anali Mawu, Mawu anapangidwa thupi. Ndiyeno pamene ife tingakhale omwetsedwa chotero mwa mphamvu Yake kuti ife tife kwa kuganiza kwathu komwe, ndipo chikhulupiriro chathu chikhale chikhulupiriro chenicheni^ALELUYA! Ndiye Moyo wa Khristu walowetsedwa mwa ife, ndipo ife tikhala zolengedwa za moyo za Mulungu_malo okhalamo a Mzimu Woyera akhoza kufalitsa madalitso Ake panso kupyolera apo, ndipo ife tiri mu thunthu la Khristu.

135 Yesu anati, "Kodi sizinalembedwe inu mukundinyoza Ine, ponena kuti ndine Mwana wa Mulungu?" Kodi sizinalembedwe kuti inu ndinu milungu. Kodi malamulo anu omwe samatero?" Monga Mose, monga Eliya monga aneneri aja amene anakhala moyo pafupi ndi Mulungu mwakuti Mulungu anangodzisamutsira Iyeyekha mpaka mkati mwawo, ndipo iwo analankhula, osati iwo okha, koma Mulungu. "Musaganizire chomwe muti munene chifukwa si inu amene mukulankhula, ndi Atate amene akukhala mwa inu; Iye ndi yemwe akulankhula." Mawu Ake si a iyeyekha chifukwa moyo wake_ iye ndi wakufa.

136 Ngati inu mufa kuchotsa magazi mwa munthuyo. Mumuwumitsa. Vuto lake ndi lakuti anthu ambiri sanawumitsidwepo. Mukachotsa magazi mwa munthuyo, wapita. Ndiye chinthu chokha inu mungachite ndi kuyikanso magazi ena mwa iye. Ngati ati akhalenso bwino; inu munachotsamo magazi ake. Ndipo tsopano tikuyikamo Magazi a Yesu Khristu! Mwaona? Ndipo izo zimabweretsa CHIKHULUPIRIRO cha Yesu Khristu; UKOMA wa Yesu Khristu: CHIDZIWITSO cha Yesu Khristu; KUDZILETSA kwa Yesu Khristu; CHIPIRIRO cha Yesu Khristu; UMULUNGU wa Yesu Khristu; CHIKONDI CHA PA ABAL cha Yesu Khristu; ndi CHIKONDI CHA MULUNGU chimene CHIRI Yesu Khristu! Iye ndi mutu umene umakulamulirani inu! Ndipo mapazi anu ndiwo maziko, chikhulupiriro. Amen! Olamuliridwa ndi mutu. Tenga chakuti^?^Ndi zimenezotu.

AMENEYO NDIYE MUNTHU WANGWIRO WA

MULUNGU_pamene Iye akhala ndi mphamvu izi.

137 Ndiye Mulungu, poyimira Mpingo Wake monga Mkwatibwi_mkazi. Mulungu amayimira Mpingo Wake monga Mkwatibwi, ndipo momwe Iye amabweretsera aliyense payekha kuti akhale mwana Wake woti apite mwa Mkwatibwi ameneyo, Iye wabweretsanso Mkwatibwi popyola mmibadwo iyi mpaka Iye atabweretsa Mpingo umodzi wamphumphuwu mu ichi.

Mapazi anga amasuntha. Bwanji?_chifukwa mutu wanga watero. Tsopano iwo sangayende monga manja anga, chifukwa iwo ndi mapazi anga. Lutera sangachite zinthu zomwe ife tachita; ngakhale Amethodisti sangathe chifukwa iwo anali chinthu chinachake. Onani, mapazi amayenda chifukwa mutu watero. Ndipo mutu sumati, "Tsopano, mapazi inu mukhale manja. Khutu, iwe ukhale maso." Mwaona? Koma m'badwo uliwonse Mulungu wayika zinthu izi mu Mpingo Wake, nawufanizitsa powonetsa kuti aliyense ali ndi izi_ali nawo makhalidwe awa. Ndipo "chinthu" ichi chikatsirizidwa, ndi Mpingo wa Mulungu ukupita mu Mkwatulo! Ndipo "chinthu" ichi chikatsirizidwa, ndi wantchito wa Mulungu mu Mpingo wa Mulungu, amene akupita mu Mkwatulo. Ulemerero! Mukuona zomwe ndikutanthawuza? Ndi zimenezotu. Apo pali chinthu chonse.

138 Kuno kunadza mwamuna, Paulo, kudzayika maziko. Ireniasi anayamba kukhuthulira ichi pa icho, ndipo wotsatirayo anakhuthulira ichi, ndipo wotsatira anakhuthulira ichi, wotsatirayo icho, ndi icho, ndi icho, ndi kumangopitirira mpaka zitafika mu m'badwo wotsiriza. Koma ndi chiyani?_Mzimu womwewo. Mzimu womwewo umene umakhala mwa ine ukuti, "Manja, fikira kwa mkate uwo." Mzimu womwewo umati, "Mapazi, suntha kamodzi." Mukuona chomwe ndikutanthawuza?

Ndiye thunthu lonse la chomwe muli likulamuliridwa ndi kutsogoleredwa ndi zinthu izi, koma silingalamuliridwe kwathunthu mpaka litakhala nazo zikhalidwe izi kwathunthu.

139 Kodi inu munayamba mwamva ichi? Tsopano ndiroleni ndikuwuzeni ichi ndipo khalani kwenikweni^Muziyike izi ku khutu lomwe mumamvera. UNYOLO NDI WA MPHAMVU KWAMBIRI POLUMIKIZIRA PAKE POFOOKETSA. Izo

nzolondola? Sichimakhala champhamvu koposa pamalo ake ofooketsawo. Ngakhale chikhale chomangidwa mwamphamvu chotani, ichi chamangidwanso, ngati chiri ndi malo ofooka, pamenepo, ndi pomwe pati padzaduke. Ndipo sichingakhale champhamvu koposa malo ake ofooketsawo. Tsopano ngati inu muli ndi^Inu mukuti muli ndi ichi, ichi, ichi; mulibe ichi, ndipo pamene chiti chidzaduke. Ngati inu muli ndi ichi, ndipo mulibe icho, chidzaduka pomwepo. Inu muli ndi ichi ndipo mulibe icho, chidzaduka. Ichi ndipo mulibe ichi, chidzaduka. Ichi ndipo mulibe ichi, chidzaduka. Mwaona? Ndipo inu simungakhale ndi ichi opanda kukhala ndi ichi. Koteropamene mukudzipereka nokha kwathunthu, ndiye Mzimu Woyera umakhuthulira mmenemo mphamvu izi. Ndiye inu ndi Kachisi Wamoyo.

Ndiye anthu amayang'ana kunjani nati, "Uyo ndi munthu wodzazidwa ndi ukoma, chidziwitso, ndipo amakhulupirira Mawu, kudziletsa, kupirira, umulungu, chikondi cha pa abale, wodzaza chikondi cha Mzimu Woyera, akuyendayenda." Ndi chiyani? Thunthu limene osakhulupirira angakhoze kuyang'anapo nati, "Uyo ndiye Mkhristu. Uyo ndiye mwamuna (kapena mkazi) amene amadziwa zomwe akunena. Simunamuwonapo munthu wachifundo, wokoma, munthu waumulungu woposa uyu."

140 Iwe wasindikizidwa. Chisindikizo chimawonekera mbali zonse. Ngakhale ukupita, kapena kubwera, iwo amawona chisindikizo chimodzimodzi. Ndi zimenezo, onani. Pamene mwamuna, kapena mkazi akhala nazo izi, ndiye mwala wodzavindikira umatsika nuwasindikizira iwo mu Ufumu wa Mulungu umene uli Mzimu Woyera.

Ndiye Mawu, kuchokera apa, amadzikwaniritsa Okha kupyolera mu chirichonse cha zinthu izi.

Mwaona? Ndipo amapanga Chinthu chonsechi Kachisi wa Mulungu Wamoyo_ woyenda, chitsanzo chamoyo cha Chikhristu.

Chimene Khristu anali, anthu awa ali, chifukwa Moyo Wake uli mkati umu; iwo ali mwa Khristu, ndipo miyoyo yawo ndi yakufa ndi yobisika mwa Khristu kupyolera mwa Mulungu ndi osindikizidwa mkatimo ndi Mzimu Woyera_1 Akorinto

Ndi zolondola. Inu mumadziwerengera nokha akufa. Ndiye mwabadwa ndi chikhulupiriro, ndiye ukoma, ndipo zinthu zina izi zawonjezedwa kwa inu mpaka ndinu Fano Lamoyo la Mulungu langwiro.

141 Kodi izo sizodabwitsa? Ndiyeno Mulungu kupyolera mwa izo, wabweretsanso Mibadwo Isanu ndi iwiri kuti awonetse masitepe asanu ndi awiri amene Iye wabweretsa kuwamanga munthu Wake payekha mpaka mu chifanizo Chake. Iye wamanga Mpingo wamphumphu mwa chifanizo Chake, ndipo pa chiwukitsiro Thupi lamphumphu ili lidzawukitsidwa kuti lidzakhale Naye kwa nthawi zosatha, chifukwa ilo ndi Mkwatibwi. Mukuona? Kotero izo zikudutsa mu m'badwo uliwonse. M'badwo uliwonse umene ukudza.

Ndipo pali zambiri zofunika, kumbukirani. Kumbukirani zimene Paulo ananena apa pa Ahebri 11. Ndiroleni ndingokuwerengerani chinachake tisanatsirize apa mwa kaminiti kokha ndiyeno inu^Zimakupangitsani mwina kumva ngati chachirendo pamene ine_nthawizonse pamene ndikuwerenga ichi. Ine ndipeza Ahebri 11 ndipo ndiyambira pa ndime ya 32.

"Chiyainso^ndinene chiyainso? Pakuti nthawi indiperewera ine kuti ndikuuzeni inu za Gideoni, za Baraki ndi Samsoni, Yefita, Davide, ndi Samueli, za aneneri:

Amene mwa chikhulupiriro anagonjetsa maufumu, nachita chilungamo, nalandira malonjezano, natseka pakamwa mikango,

Anazimitsa mphamvu ya moto, napulumuka lupanga lakuthwa, ndipo mkufooka analimbikitsidwa, nakula mphamvu ku nkondo, anapitikitsa magulu ankhondo achilendo.

Akazi analandira akufa awo mwa kuwukanso kwa akufa: ena anapyola mmazunzo_anazunzidwa, osalola kuwomboledwa; kuti akalandire chiwukitsiro choposa: (Pansi apa, onani. Chabwino)

Ndipo ena anali ndi kutonzedwa kwankhanza ndi kukwapulidwa, inde, ndiponso nsinga ndi kuwatsekera mndende:

Anaponyedwa miyala, anachekedwa pakati, anayesedwa, anaphedwa ndi lupanga: anayendayenda atavala zikopa za nkhosa ndi zikopa za mbuzi; pokhala osowa, osawutsidwa, ochitidwa zoyipa;

(Amene dziko lapansi silinali loyenera iwo:) (Onani, mawu ochepetsedwawa, inu, mukuwaona iwo mu Baibulo lanu) "iwo anasochera mzipululu, ndi mmapiri, ndi mmaphanga ndi mmauna a dziko.

Onsewa, analandira umboni wabwino kupyolera m'chikhulupiriro," (apa: umboni wabwino mwa chikhulupiriro) "sanalandire lonjezolo ayi: Mwaona?

Mulungu atakonzera zinthu zina zabwino kwa ife, kuti iwo popanda ife asapangidwe kukhala angwiro."

142 Inu mwamva izo? Anthu awa, amene anafa apa akudalira ndi kuyembekezera pa ife. Kotero Mpingo uno uyenera kufika pa ungwiro ndi cholinga choti ufikitse chiwukitsiro, ndipo iwo ali pansi_miyoyo pansi pa guwa, kuyembekezera Mpingo uwu kuti udze ku ungwiro wake. Koma pamene Khristu ati abwere_ ndipo Mpingo uwu, mukuona, ukubwera mocheperako mwa anthu pang'ono, (ndi zosongoka kwambiri kusiyana ndi izo, koma monga momwe ine ndalemba pamalo awa, onani) zikudza pa msonga yochepa, mpaka Mpingo mwa kuchepa uyenera kufika pamalo mpaka ndi utumiki wa mtundu womwewo umene uwu unasiya. Chifukwa pamene mwalawapamutu uwu uti ubwerere_uli ndi changati thumba apa pomwe uti udzakhalepo apo pa piramidi wamba. Iwo sichipewa chabe chomwe chikudzakhala pamwamba, ndi kachidutswa kodzalumikiza. Ndipo iwo uyenera kudzakhala pamenepo chifukwa umatetezera madzi. Ndipo pamene iwo ubwera, Mpingo uwu uyenera kudzasongoka. Zonse izi^miyala inayo mu piramidi yaikidwa mwangwiro chotero mpaka inu simungapitse lumo pakati pawo_yolemera matani imene ili mmenemo. Momwe iwo anayikwezera pamwamba, iwo sakudziwa, koma iyo inamangidwa. Ndipo pamwamba apa, pamene chodzavindikira pa piramidi chiti chibwere, piramidi payokha, Thupi la Khristu lidzayenera kusongoka_osati chikhulupiriro china chabe, chiphunzitsa, kapena chinthu china chimene ife tapyolamo_udzayenera kukhala mwangwiro kwambiri monga Khristu mpaka pamene Iye abwera, Iye ndi utumiki uwo zidzagwirizana bwino moyenerana limodzi. Ndiye udzadza Mkwatulo ndi kupita kwathu.

143 Onani komwe tikukhala tsopano_mu Laodikaya momwe mpingo unali M'badwo wa Mpingo woyipitsitsa womwe unakhala nawo. Mu Baibulo timapeza kuti unali M'badwo wa Mpingo wokha womwe Mulungu anali kunja kwa Mpingo, kugogoda, kuyesa kubwerera mnyumba Yake Yomwe. Zikhulupiriro ndi zipembedzo zinamuyika Iye kunja kwa Mpingo Wake Womwe "Taonani, Ine ndayima pakhomo ndipo ndi kugogoda. Ngati munthu aliyense ali ndi ludzu ndipo akatsegula chitseko, Ine ndidzalowamo ndi kudya naye."

Mwaona?

Apa Iye ali mu M'badwo wa Mpingo uwu ndipo mwa pang'ono amamutaya Iye kunja mpaka apa, iwo anamutulutsa Iye kwathunthu. Iwo sakufuna kuchita naye kanthu kalikonse.

Tsopano, inu mukuona lero kumene tikupita. Ngakhale pamene kutha kwa M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya akhala mwamaonekedwe choncho, mpaka iwo ndi Chikatolika, (amene anasiyana pomwe apa) akubwera pamodzi nagwirizana monga mpingo umodzi wopambana; ndipo chiyanjano cha mpingo. Izo ziri chimodzimodzi monga Chikatolika.

144 Pali kusiyana kumodzi kokha; ngati angakudumphitseni inu icho_ndicho kudya mgonero. Ndi chinthu chokhacho mu dayosizi chimene chimalepheretsa Chikatolika ndi Chiprotestanti kuti zisagwirizane_ndilo dongosolo la mgonero. Mpingo wa Katolika umati, "Iwo ndi Thupi." Ndipo mpingo wachiprotestanti umati, "Iwo umayimira Thupi."

Akatolika amawupanga kukhala misa. Misa ndi pamene iwo akutenga mgonero, kuyembekezera kuti akhululukidwa. Aprotestanti amadya iwo mwa chikhulupiriro, kumuthokoza Mulungu mu mgonero kuti iwo akhululukidwa. Aprotestanti amati, "Ife tiri okhululukidwa." Akatolika amati, "Ife tikuyembekeza kuti takhululukidwa." Misa ndi mgonero.

Iwo amawutcha misa; ife timawutcha mgonero. Misa ndi kuyembekezera kuti ziri choncho. Mgonero ndi kudziwa kuti ziri choncho ndi kumuthokoza Iye pa icho. Mwaona? Icho ndi chinthu chokha chimene iwo sangabwerere palimodzi. Iwo adzachita izo.

145 O, izo zimawoneka zokongola kwambiri. Iwo amagwirizana kuti ayendetse^Izo zidzayendetsa zonse^ Bwanji, Baibulo limati, "Ndipo zirombo izi zinapereka mphamvu zawo kwa hule." Mwaona, kugwirizana kwawo limodzi. Mwaona?

Chimodzimodzi basi zimene Baibulo linati iwo adzachita, iwo akuzichita izo tsopano; ziri mkati mochitidwa sabata lomwe lino. Nzolondola. Osati kuti ine ndiri ndi chirichonse chodana ndi anthu a Katolika_mosaposanso anthu a Chiprotestanti. Inu a Methodististi ndi a Baptististi ndi ambiri a inu a Chipentekoste, pamene mpingo yanu yalowa mu chigwirizano ichi cha mpingo; pamene anamanga nyumba yaikulu yosungiramo anthu akufa ku New York, ya chigwirizano cha mpingo_ndi chimodzimodzi bungwe la Chigwirizano cha Mayiko ndi zina; iwo akuyesa kugwirizansitsa Chiprotestanti chonse limodzi.

Tsopano, Akatolika ndi ochenjera kwa izo ndipo kupita kukamutenga Papa Joni wa 23, kapena wa 22, (chirichonse chomwe iye ali) iye akuyesa mwa kudzichepetsa kwake pang'ono kuti abweretse chikhulupiriro cha Aprotestanti chonse ndi chikhulupiriro cha Katolika ku chikhulupiriro chimodzi_chimodzimodzi zomwe Baibulo linati iwo adzachita. Ndi zimenezo. Ndipo Aprotestanti akufera izo mbedza, chingwe, ndi chumbu. Motani? Motani? Chifukwa iwo alibe zinthu izi. Chidziwitso_Mawu ndi olondola; chipiriro_"Iwo amene ayembekezera pa Ambuye^" Mukuona, zomwe ine ndikutanthawuza?

146 Monga bishopu wa Methodististi uja anati tsiku lina pamene iwo anapambanitsa izo_ndipo aliyense akudziwa chomwe chinadzozwa izo_kuyesa kupeza pemphero lina loti lizinenedwa mu mpingo, kapena mu sukulu, ndipo ankafuna kuti^ Ndikuganiza linali bukhu la mapemphero la Apresbateria chinachake kapena chimzake, ndipo makolo anakadulira chisamani sukulu chifukwa iwo sankalola pemphero ili lizinenedwa mu sukulu. Ndipo bishopu wa Methodististi uyu anali munthu wachikulire wanzeru. Iye anayimirira nati "Izo nzolakwika." Nati, "Ndi zosagwirizana ndi malamulo," Iye anamva mphekesera yake. Iye anati, "Monga mu tchalitchi chathu cha Methodististi^" Iye anati, "Mu tchalitchi chathu cha Methodististi^ambiri a anthu athu nthawizonse amanena za nkhani yomvetsa manyazi ya ku Hollywood ndipo makumi asanu ndi anayi ndi mphambu zisanu pa zana a iwo amapita kukawonerabe." Chovuta ndi chiyani? Iwo anasiyapo ichi. Kumene, iwo anasiyapo icho.

147 Ine ndinali kulankhula konkuno mu chipinda ichi tsiku lina kwa mkulu wina wa mpingo yaikulu ya Methodististi yomwe ili mu mzinda wa Falls_umodzi wa mpingo yauzimu zedi ya Methodististi ku Mzinda wa Fall kuja^kusonyeza m'badwo wa Methodististi womwe ukutsatira kenako kwa m'badwo wathu pamenepo_wa Chipentekoste. Ndipo iye anati, "Ku St.Louis, Missouri, iwo anatenga chiwerengero (pafupi miyezi itatu kapena inayi yapitayo) ndi kupeza^" bambo ameneyo akhoza kukhala ali muno mmawa uno. Iye ndi womanga manyumba amene akumanga iyi_amene akutikonzera nyumba ino. Methodististi ya ku Main Street ndi komwe iye amapita_Kumene M'bale Lum ndi iwo ndiye m'busa. Koteri ndiye ife tikupeza kuti mmenemo kuti ine ndikukhulupirira anali makumi asanu ndi awiri pa zana cha anthu a Methodististi mu kufufuza, ku St. Louis anapeza kuti makumi asanu ndi awiri kapena kuposerapo pa zana a Methodististi amasuta ndi kuti makumi asanu ndi limodzi mphambu zisanu ndi zitatatu pa zana onse a iwo anali oti amamwa zakumwa za mowa_a Methodististi! Ndipo chinthu chachirendo chinali pamene chiwerengerocho chinaperekedwa nawona pakati pa amuna ndi akazi, akazi anali kupitirira makumi asanu ndi awiri pa zana kwa pafupi makumi asanu pa zana cha amuna. Akazi ambiri amasuta ndi kumwa koposa amuna omwe analipo. Makumi asanu ndi awiri pa zana_makumi asanu ndi awiri nchinachake pa zana akazi kuposa cha amuna.

148 Tsopano, bwanji tikanati tipite ku chiphunzitso cha Baibulo cha kuvala makabudula, kudula tsitsi, ndi zinthu monga izo. Bwanji, ndi kupanda umulungu akazi kudzinenera umulungu ndi chiyeero maphwando a juga ndi zina zonse, amiseche, apakamwa; osati nkutha kugwira lirime_lirime lawo, kulankhula ndi kujeda, ndi kupita paliponse; bwanji nanga amuna?_maphwando a juga, masewera a gofu_kukhala kumeneko osavala mokwana, atavala tizovala tonyansato akazi ali komweko.

Zosadabwitsa ayi! Kuwona upo wonyansa anamchitira mlaliki uja, (wolalikira kundende) mmawa uno? Inde, bwana. Ine sindikuganiza kuti mwamuna uyo walakwa chotero. Kodi zinatani? Monga m'bale^Ine sindingaganizire dzina lake. Eya, Dan Gilbert, wolalikira kundende. Pamene munthu uja anangothamangira mkatimo nakamupha Dan kuno miyezi ingapo yapitayo, ndipo tsopano mkazi wake akuyembekezera kukhala ndi mwana. Indedi Dan anafa; iwo sangayese magari a mwanayo tsopano. Iye anati kuti Dan anamugwirira iye ndipo uyo ndi mwana wa Dan. Ine sindikukhulupirira zimenezonso koposa momwe sindingakhulupirire kuti khwangwala ali ndi nthenga za njiwa. Ayi bwana, ine ndikukhulupirira kuti ndi bodza. Ine ndikukhulupirira kuti Dan Gilbert anali munthu wa Mulungu. Ine ndikukhulupirira kuti ilo ndi bodza la mdierkezi.

149 Monga izo zomwe ankafuna kuyikapo za mapemphero awo. Bishopu wokalamba wa Methodisti uja anali wochenjera kokwana kudziwa izo. Ngati zimenezo zinakapyola_izo zinali zongodzozedwera ndi china chakenso. Nkulondola.

Monga ngati vuto la kusankhana mitundu Kummwela uko_chinthu chofanana. Ine ndikukhulupirira munthu azikhala mfulu. Ine ndikukhulupirira fuko lino limayimira ufulu. Ine sindikumuda Mr. Kennedy potumiza kumeneko ankhondo ngakhale sindine "Wochita zinthu Mwatsopano" ndipo ine sindine Democrat sindine wa Republican, ine ndine Mkhristu. Koma ine sindikukhulupirira mu izo. Ine sindikukhulupira anthu achikuda ayenera agulitse ufulu wa kubadwa wawo chifukwa cha zinthu zotero, nkonse. Uko kunali^Chipani cha Republican^magazi a Abraham Lincon anawapatsa ufulu anthu amenewo, chifukwa iye anali munthu wa umulungu. Ine ndikuganiza kuti inu mukanayesera kukanirira ku chipani ngati inu muti muchite masankho nkomwe. Koma ine ndikuwuzeni inu chinthu chimodzi, mnyamata uyo sanali kumeneko chifukwa cha masukulu chabe; mnyamata ameneyo ndi mbadwa. Iye ndi M'mereka. Uwu ndi ufulu kwa onse. Khungu la munthu lisanthe nilimusiyanyitsa. "Ife tonse^" (Mulungu anati) "a munthu mmodzi wopangidwa ndi magari onse, mafuko onse." Ndife tonse amodzi.

150 Koma mnyamata uyo, iye anali msirikali; anati wankhondo wakale. Iye anamenyera zomwe ziri zolondola. Iye anali ndi ufulu wopita ku sukulu. Izo nzolondola, koma iye anali ndi masukulu ambiri komwe akanapitako. Ndi chinthu chomwe chiri. Ngati ungachiyimire kumbuyo, ndi zazipembedzo zamakonozi kumeneko zomwe zikudzoza zimenezo. Motani? Iwo akutenga mavoti a akuda kuchokera ku Republican kumka ku Democrat, ndipo iwo akugulitsa ufulu wobadwa nawo potero. Zowona kumene. Mzimu Woyera suli mmenemo. "Lolani iye amene ali ndi nzeru, lolani iye amene ali ndi chidziwitso," Kumene.

Monga ngati mpingo uwu, m'badwo wa pakali panowu, kudzigulitsa wokha. Kodi simungawone zomwe ziti zichitike? Ine sindikusamala ngati izi zikujambulidwa, ndi izi zikubwerazi! Chavuta ndi chiyani? Amayi anga omwe ankazolowera kunena kuti "Mpatseni mdierkezi zake." Panali mwamuna mmodzi amene anachita chinthu chimodzi chanzeru; ameneyo anali Castro, kumusi uko. Inde bwana, iye anapita kumeneko, anthu a Chikapitolisiti anali ndi mizimbe yonse uko ndi chirichonse_ziri pa muyezo wa golide monga United States. Kodi iye anachita chiyani? Iye anagula chuma chonsecho. Amapeza ndalama mwa njira iliyonse yomwe akanatha. Iye anachita chiyani ndiye? Iye anapanga ndalama zabodza nazisintha. Nakazibwezeranso izo^Ndi chokhacho chomwe dziko lino lingachite.

151 Kodi inu munamvera Life Line mmawa wina? Bwanji, inu mukudziwa, ziri ngati inu kugulitsa chuma chanu pa golide. Chumacho chatengedwa kale, ndipo boma lomwe liripoli tsopano likuwonongera ndalama chiyani?_ndalama za msonkho zomwe iwo ati adzasonkhetse zaka makumi anayi kuchokera pano. Iye wathedwa. Izo nza pa Life Line kuchokera ku Washington D.C., kufika kwa fuko. Misonkho_ iwo akuwononga ndi kuyesa kugula akunja^ Bwanji, iwo akungozipereka izo mwa njira iliyonse. Kodi inu simukuwona, kuti izo ndi chimodzimodzi zomwe ati achite? Mwaona, izo ndi chiyani? Tsopano, ngati fuko ili likupita niliphulika_chinthu chokha chomwe lingachite kumka liphulika. Chinthu chokha chomwe lingachite ndi kulowa bankalapati. Icho ndicho chinthu chanzeru chokha kuchichita^kusintha ndalama. Koma iwo satero ayi. Pansi pautsogoleri watsopano. Mpingo wa Roma Katolika ndi womwe uli mwini wa golide wa mdziko, ndipo chomwe iwo ati adzachite ndi kudzigulitsa. Anthu olemererawa ndi ena otero pansu pano, monga momwe Baibulo linanena, kodi iwowa adzachita chiyani asanaluze_ kampani ya fodya ya Brown and Williamson (ambiri a iwo ndi Akatolika ngakhalebe) ndipo zinthu zina zonsezi; kodi iwo adzatani?_iwo adzavomereza izo ndipo adzatenga ndalama kuchokera ku Roma, ndiyeno adzagulitsana ufulu wobadwa nawo. Roma adzawathandiza iwo. Inde, bwana.

Iye adzalithandiza ilo. Ndipo iwo ayamba kukhala ndi dongosolo lokwana tsopano_kukhala ndi zokwana pafupi nawo. Kudza nazo mu nyumba ya malamulo yake. Onani zimene a Mr. Kennedy akuzipempha.

152 Ndipo pamene inu munawona izi tsiku lina_palibe kufunika kwa voti ayinso. Voti ndi ya ntchito yanji? Pamene anazilemba mu pepala natsimikizira izo pamaso pa gulu, ndipo iwo anakana kuchitapo kanthu pa izo; pamene iwo anatsimikizira kuti makina kulikonse mu dzikoli anatchedwa_kuti iwo anasankha Mr. Kennedy mwa voti yabodza. Kodi Baibulo silinena kuti iye adzadza mwa chinyengo? Monama.

Tsopano, ine sindikutsutsana ndi chipani cha Democrat_ osati mochulukira kuposa chipani cha Republican, koma ine ndikufotokoza zowona zochokera mu Baibulo. Phindu la voti nchiyani? Iwo akudziwa yemwe akupita mmenemo.

153 Ndi angati a inu amene akukumbukira zowonetsedwa pa televizioni pamene anali ndi akazi awiri atayima ndipo mmodzi anati, "Ine ndivotera^" Mkazi wa Chiprotestanti anati, "Ine ndivotera Mr. Kennedy."

Iwo anati, "Chifukwa?"

Nati, "Chifukwa ndikuganiza kuti iye ndi munthu wochenjera koposa Mr. Nixon. Iye adzakhala pulezidenti wabwinoko."

Ndiye iwo anati, "Uyu ndi mkazi wa Chikatolika. Kodi inu mudzavotera ndani?"

Iye anati, "Ine ndi wa Katolika, Mroma Katolika, Mkatolika wodzipereka." Iye anati, "Ine ndivotera Mr. Nixon."

"Chifukwa?"

Nati, "Chifukwa ndikuganiza Mr. Nixon adzakhala pulezidenti wabwinoko, chifukwa iye ndi wozolowera kwambiri zinthu izi. Iye akudziwa bwino za Komyunisimu." Mkazi ameneyo ananena bodza.

154 Ine ndiri ndi zomwe iwo amadzitcha, "Zowona za Chikhulupiro chathu," bukhu lapamwamba zedi la Katolika lomwe lingagulidwe. Ndipo likuti mmenemu, "Ngati pali Mkatolika atalembetsa pa mpikisano palimodzi ndi Mprotestanti, ngati Mkatolika wina aponyera voti Mprotestanti amachotsedwa mu chiyanjano cha mpingo wa Katolika." Zolondola! Ndipo ngati pali Akatolika awiri akukanganira udindo umodzi, iwo azisankhapo Mkatolika amene ali wodzipereka kwambiri kwa "manthu wa mpingo" ndi kuwavotera iwo.

Mukuona momwe icho nchinyengo? Kodi iwo akuyesa kuchita chiyani? Kupereka ndalama kuti agule chiyani?_iwo akuyesa kuliphwasula ilo_ndipo akuchita izo, ndipo ilo laphwasuka. Ndi chiyani? Ziri pa muyeso wa golide, ndipo Mpingo wa Katolika (wolowezana ufumu) ndiwo mwiniwake wa golide mu dziko_\$168,000,000,000. Ndi zimenezotu.

155 Kuliponyera dziko lathuli pa muyeso wa golide ndipo anthu inu gwiritsitsani nyumba zanu ndi zinthu, koma inu ndinu a mpingo wa Katolika. Fukoli mwini wake ndi mpingo wa Katolika. Zinthu zonse zagwidwa mmenemo chotero kupyolera mu ndalama zawo.

Kodi Baibulo silimanena za izo? Ndicho chithunzi chomwe Baibulo limatijambulira ife? Chomwe ine ndikuyesa kunena, M'bale, lero iwo akuti, "Uwo udzakhala mpingo wabwino. Iwo udzagwirizansitsa Chiprotestanti." Izo zikuwoneka bwino kwa maso a chilengedwe, koma chidziwitso cha mdziko ili ndi chopusa kwa Mulungu ndipo zinamukomera Mulungu kuti kupyolera mu kupusa kwa kulalikira kuti apulumutse iwo amene ali otayika mwa udindo wauzimu umene iye anawukhazikitsa mu Mpingo Wake kuti amange Mpingo pa zikhalidwe zauzimu izi osati pa chinthu chinachake chimene chiri cha kwa dziko.

156 Petro anati, "Ndipo chifukwa inu mwathawa chivundi cha mdziko kupyolera mu kukhumba ndalama, ndi kukhumba nthawi zazikulu, zosangalatsa, kudya, kumwa, ndi kukhumba komwe ife tiri nako, inu mwathawa izo, tsopano inu mwamangidwa mu umoyo weniweni." "Ine ndikulankhula izi kwa Mpingo," iye anatero. Ndi zimenezo. Kodi inu munawerengapo izo? Kodi munamvetsa izo? Kodi inu munazimva izi pamene timawerenga izo poyamba paja? Mu 2 Petro, ingomverani zimene iye akunena apa; momwe zinalembedwa mokongola apa, momwe iye akuzifotokoza. Chabwino, mvereni iye tsopano, pamene akulankhula. Chabwino.

"Petro_Simoni Petro, wantchito ndi mtumwi wa Yesu Khristu, kwa iwo amene alandira chikhulupiro chofanana chopambana ndi ife kupyolera mu chilungamo cha Mulungu ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu:

^ mtendere ukhale kwa inu uchulukitsidwire kwa inu kupyolera mu chidziwitso cha Mulungu, ndi cha Yesu Ambuye wathu.

Monga momwe_momwe mphamvu zake zaumulungu zatipatsa ife zinthu zonse." (Ndi ndani amene ati adzalandire dziko, ndi zinthu zonse? Zedi zokhudza^ inde, chabwino) "zimene zikukhudza za moyo ndi umulungu, kupyolera mu chidziwitso cha iye amene watiyitanira ife ku ulemerero mpaka ku ulemerero.

Pamene kwapatsidwa kwa ife malonjezo aakulu zedi opambana: kuti mwa iwowa inu mukhoze kukhala ogawana nawo khalidwe laumulungu mutathawa chivundi" (mverani kwa icho) "chimene chiri mu dziko kupyolera mu kukhumba."

157 Kukhumba ndalama. Kukhumba zinthu zazikulu. Kukhumba kutchuka. Zinthu izi zafa kwa okhulupirira! Ife sitikusamala_hema kapena khumbi! Ndisamala chifukwa chiyani? Moyo kapena kufa; kutitimira kapena kumira; ichi ndi chinthu chimene ine ndikukondweretsedwa mwa icho: Ufumu wa Mulungu. Kaya nditsala ndi nyumba yanga; kaya nditsalabe ndi banja langa; kaya nditsalabe ndi chirichonse chomwe chiri; ndiroleni kuti nditsalebe ndi Khristu, chiyembekezero cha ulemerero!

Ndimangeni ine, o Ambuye mpaka apa. Lolani Khristu akhale Mutu wanga." Lolani kuti azigwira ntchito kupyolera mwa ine pa maziko anga achikhulupiriro changa chiri mwa Iye. Lolani ukoma, chidziwitso, kudziletsa, chipiriro, umulungu, ndi chikondi cha pa abale, zizigwira ntchito mwa ine, o Ambuye, ndiro pemphero langa. Ine sindikusamala_moyo kapena kufa; kutitimira kapena kumira; chipembedzo kapena osakhala chipembedzo, bwenzi kapena sibwenzi, lolani izo zigwire ntchito mwa ine. Lolani ukoma wa Khristu, chidziwitso Chake, zikhuthukire kuti ine ndikhoze kuphunzitsa izo, pakuti Mulungu wayika mu mpingo atomwi, aneneri, aphunzitsi, abusa, ndi alaliki, onse kuti afikitse ungwiro ndi kubweretsa mphamvu zonse izi kwa iwo_ku ungwiro uwo wa kudza kwa Mwana wa Mulungu.

158 Uliwonse wa miyala iyi ndi banthu lochokera ku umodzi uwo. Ili ndi banthu la uwu. Iliyonse ya mphamvu izi ndi za Iye, ndipo izo zikutsanulidwa kuchokera mwa Iye nkumatsika kupyola monsemo. Amen!

Ndi 12 koloko. Zonsezo zimapita kuti? Amen.

Kodi inu mumamkonda Iye? Kodi inu mukukhulupirira izo? Mverani aang'ono inu^Mlongo Kidd anatero mmawa uno, "M'bale Bill, sindikudziwa ngati nditi ndidzawonane nanunso." Izo zinali ngati zindiphe ine. Iye akuganiza kuti akukalamba; iye alidi. Ine ndikupemphera kuti Mulungu asunge moyo wake ndi M'bale Kidd nthawi yaitali. Dikirani ine ndikuwuzeni inu, ife sitikudziwa kutalika kotani titi tikhale wina ndi mzake. Ine sindikudziwa kuti ndikhala nanu kotalika chotani. Mulungu akhoza kundichotsa ine mudziko. Iye akhoza kundiyitanira ku munda wina wa ntchito. Iye akhoza kukuyitanirani inu kwinakwake. Ife sitikudziwa, koma tiyeni_tiyeni tipitirize, tisalole izi kuti izi zingopita pamwamba. Tiyeni titenge izo. Ndi izo ziri mu Baibulo. Apa izi, zikugwirizana ndi chirichonse, ndipo ngati ine ndikanangokhala ndi nthawi yozichita_sungazichite izo mu tsiku limodzi, inu mukudziwa izo_ine ndikanangomangiriza zonse palimodzi. Onani pamene titi titsirize ndi uthenga uja uko, muone chomwe Mzimu Woyera unachita pa khoma, sichoncho inu? Ndi angati amene anali pano nthawiyo? Anadza pansu pomwe nadzajambula chinthu chomwecho_Mngelo wa Ambuye.

159 Mwaona, ndi Choonadi. Musalole izo zikupulumukeni inu. Gwiritsitsani kwa icho, ananu. Gwiritsitsani kwa icho. Kumbukirani, mangani pa chikhulupiriro chanu: ukoma, chidziwitso, chipiriro^

Tsopano apa ndikuganiza ndiri ndi kachidutswa ka pepala apa, ngati ndisanakagwetse kwinakwake pamene ndimalalikira. Ndi ichi apa. (Zikomo, M'bale, zikomo kwambiri.) Ngati inu mukufuna kuyang'anapo ndi kuwona ngati pali chinthu china apa choti inu mungakhoze_mwina ndi kadongosolo kabwinoko kusiyana ndi kamene kalipo, kuti mukhoze kulemba powonera pa ichi. Ine ndingochiphatika apa ndipo inu mukhoza kumayang'anapo ndi kulemba mofanana.

160 Tsopano, ine ndikufuna inu muchitenge, nimukawerenge icho, ndi kufanizira icho,_ndiyeno NKUCHITAPO kanthu. Osangochiwerenga icho, kuchifanizira icho_koma CHITANIPO kanthu, pamene mutero. Muchitenge moona mtima kwa inu nokha.

Musati, "Chabwino, ine zinandikomera kwambiri kumvera izo." Ine ndinateronso. Koma kumvera izo ndiyeno kulandira izo ndi zosiyana. Mwaona? Mwaona, ndi zosiyana. Mwaona? Pali ziyeneretso zisanu ndi ziwiri kuti tipange thunthu la Mulungu. Pali Mibadwo ya Mpingo Isanu ndi iwiri imene Mulungu wabweretsera Mpingo ku ziyeneretso izi, ndipo iye anali ndi atomiki asanu ndi awiri kuti achite izo. Pali zisanu ndi ziwiri, zisanu ndi ziwiri, zisanu ndi ziwiri. Mwaona? Zisanu ndi ziwiri ndi nambala ya Mulungu ya kutsiriza, ndipo zitatu ndi nambala ya Mulungu yangwiro. Kotero pali zitatu ndi zisanu ndi ziwiri zitatu. Kotero mwamasamu, mwauzimu, mwa Mawu, mwa umboni wa Mzimu Woyera, zonsezo zatsiriza chinthuchi pamodzi.

161 Tiyeni tziwerenge izo. Tiyeni tionjezere ku chikhulupiriro chathu zinthu izi, ndiye, kuti tifike mu thunthu lonse la Khristu_pokhala olumikizidwa pamodzi ndi chikondi cha umulungu, kuwopa kwa Mulungu, ulemu mmitima yathu kwa wina ndi mzake, kulemekeza kwakuya kwa wina ndi mzake, chikondi cha pa abale ndi alongo_osati zonyansa. Popanda kalikonse koma khalidwe la ungwiro wa Mzimu Woyera; kukhala limodzi, kukhala Akhristu; kuyenda ndi chikhulupiriro; kulola ukoma wa Mulungu uziyenderera mwa inu. Lolani chidziwitso cha Mulungu pamene zifika pa chabwino ndi cholakwika^Pamene mdierekezi apereka chinthu china chomwe sichiri mofanana mwa Malembo, chokani kwa icho. Nzoona zedi izo.

162 Ine ndikhoza kulingalira atumwi aja sankachita monga ife. Iwo anapita ponseponse, mwina anthu a mawu pang'ono mpaka iwo atafika paguwa. Iwo analowa mkati, iwo amachita zomwe amayenera kuchita, natuluka panja. Inde, bwana, iwo anali ndi mphamvu. Iwo anali ndi ukoma. Iwo anali opanda zotsutsana ndi munthu; ankadziwa pomwe anayima. Ndizo zonse, iwo ankadziwa yemwe anamukhulupirira. Iwo anapitirira kuyenda mwa Mzimu kuchita zokhazo^Monga momwe ndinanena usiku wina, "Kugwedeza mutu pang'ono kumodzi. Ndi zokhazo zomwe Mulungu ankasowa kuchita ndiye palibe zomwe zikanawaleketsa iwo." Iwo analibe funso, kuwerenga, ha-nha, ndi kutopa monga momwe ife tichitira, kaya achite ichi kapena icho. Iwo amangopita nakachichita basi. Kugwedeza mutu pang'ono pokha kuchokera kwa Mulungu. Izo zimachititsa. Izi ndizo. Motani? Iwo akanadziwa bwanji kuti kunali kugwedeza kuchokera kwa Mulungu? Iwo anali ndi mphamvu zonse izi mmenemo, ziyeneretso zonse izi, ndipo kugwedeza kwakung'ono koyamba kwa Mulungu kukafanana ndi kalikonse ka izi ndi Mawu Ake; iwo ankadziwa kuti anali Mawu a Mulungu ndipo iwo anali kupita. Iwo sanasowe kudandawula za kanthu kalikonse pamene Mulungu anena, iwo amapita.

163 Ife timalankhula^Mulungu amalankhula kwa ife; ife timati, "Chabwino, ife tiyambapo. Tiwona ngati tingamakhale Moyo uwu." Chinthu choyamba mukudziwa wina akakukhumudwitsani inu. Chabwino ndithu, uyo ndi mdierekezi!

Inu mukanamuwona iye momwe amayesera kundilepheletsa ine kuti ndisadze ku msonkhano uwu mmawa uno. Mukanakhala nazo izo nthawi imodzi. O chifundo, ine ndimasowa kumenyera nthawi iliyonse pamene ine nditchula msonkhano. Ndipo ngati ine nditi ndikapempherere odwala ndipo wina akamafa wosapulumsidwa, pakhala matelefoni makumi atatu ondiyitana pa maminiti khumi (ngati angathe kuyankhidwa mofulumira chotero,) kuti andilepheretse ine kwa icho. "O M'bale Branham, inu muyenera kuchita ichi," koma nkutitu pali moyo woti ungatayike.

164 Usiku wina ine ndinayitanidwira ku malo. Mnyamata wamng'ono^Ine ndinalankhula naye konkuno momwe mumamutcha (msika wapamwamba) zaka zingapo zapitazo. Iye anakhala chidakhwa. Ine ndinkamudziwa mnyamatayo, mnyamata wabwino zedi; koma iye anali wochimwa. Ndipo kotero amayi ake anandiyitana. Ndikuganiza kuti iwo anamuyitana Doc kangapo nayitana_amuyitana Billy, ndipo potsiriza ndinalandira uthengawo. Ndipo pamene ine ndinalandira uthengawo, mowona kwa ubwino sindinamenyepo nkondo mmoyo wanga kuti ndikafike kwa mnyamata ameneyo. Ndipo pamene ine ndinafika kumeneko mnyamata wosaukayo anapitirira pakuti angandidziwe ine. Anali atagona pamenepo, chikomokere. Ndi kumangochita zambiri. Abambo amayesa kumamusisita ndikumati, "Wokonedwa," ndipo bambowo anali a zaka makumi asanu ndi chimodzi. Namati, "Wokonedwa wanga izi," ndipo, "Gona phee." Iye akuyesa kuti adzuke; timikono taketo tokula chotere paliponse. Mnyamatayo anali ndi khansara kwambiri mpakana kuti iye sanali kalikonse koma khansara kwathunthu. Ziwalo zonse za thupi lake zinali ndi khansara. Ngakhale misempha ya magazi ake inali khansara. Chirichonse. Ndipo iye anali pamenepo akumayesa kuwuka nkumangopitirira kuchita motero.

165 Ine ndinamugwira iye padzanja; ndinati, "Woodrow, Woodrow ine ndi M'bale Branham."

Bambo ake anati, "Kodi sukudziwa, awa ndi M'bale Bill, Woodrow, awa ndi M'bale Bill."

Iye anati, "Haa, Haa, Haa, Haa," chotero.

Ndipo abambo ake anayang'ana nati "Billy, mwabwera mochedwerapo."

Ine ndinati, "Sizimakhala ndi kuchedwa kwambiri. Iye ali pompano. Ine ndinali ndi nkondo, ndiyeno anyamata ena, ena mwa anyamata (ochimwa) anali atayima pamenepo_ena mwa abale ake. Ine ndinati, "Mukuona, anyamata konzekerani, chifukwa inu mukubwera pa malo awa. Inu muyenera kufika mpaka pomwe apa. Mukuona? Mwina osati kupyolera mwa khansara; mukhoza kudza kupyolera mu chinthu china uko pa msewu mukukhetsa magazi kwa imfa, kapena chinachake. Inu muyenera kubwera kwa ichi." Ife tinalankhula kwa iwo. Ine ndinkayembekezera kuti ndiwone chomwe Mzimu akanati ndichite. Kuyembekezera.

Chinthu choyamba ine kuchidziwa, ine ndinamverera kugwedeza kwakung'onoko. "Ika manja ako pa iye." Ine ndinayandikira ndi kuti, "Nonse inu weramitsani mitu yanu." Iwo onse anaweramitsa mitu yawo (anyamata awiri kapena atatu ali mmenemo.) ine ndinayika manja anga pa iye. Ndinati, "Ambuye Mulungu, lolani mnyamata atsitsimuke kuti adziwe chomwe ati achite, pakuti iye ayenera kukumana nacho chinthu ichi. Iye akufa. Satana wamuzengeleza iye, ndipo akupita. Wadzimwetsa yekha kwa imfa. Tsopano ndi uyu mchikhalidwe ichi, ine ndikupemphera Inu mukhale achifundo kwa iye." Ndipo pamene ndinamupempherera iye, mmawa wake anakhala pansu namalankhula kwa abambo ake.

166 Busty Rodgers, pamene iwo anandiyitanira ine ku chitapala sikale ayi. Ine ndinali uko tsiku lotsatira nditalalikira ku Middletown kumene mwana uja George Carter anachiritsidwa_nonse inu mukukumbukira. Kunali M'bale Smith, mlaliki wa Methodisti anati, "Ngati munthu wina anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu pano, tuluka pansu pa hema yanga!" Chotero, ku Tottensford kuja pochititsa msonkhano. O, kumangondinyozetsa ine pa chifukwa chirichonse inu mungachiganizire. Ine sindinalankhule liwu limodzi.

Kungopitirira. Ine ndinali ndi utumiki. Ambuye anandiwonetsa ine masomphenya panali mwanawankhosa kumeneko atakodwa kwinakwake mchipululu. Inu nonse mukukumbukira masomphenyawo nonse inu. Ndikulingalira choncho; kodi mukuwakumbukira iwo?

167 Chabwino, ndiye ine ndinkapita mchipululu kumeneko kuyisaka iyo. Ndinapita ku Tottensford. M'bale Wright

kumeneko akudziwa tinapita uko, sanadziwe choti achite. Ine ndinagula kabokosi ka sopo pa mtengo wa daimu. Ine ndimapita kumeneko, kuyimba pamenepo, nkumalalikira nditakwera pamenepo. Iye anati ankapita pamwamba pa phiri kukachita malonda. Ine ndinapita naye. Kunali tchalitchi cha Baptisti chakale kumeneko, mopanda anthu. Ambuye anati kwa ine, "Yima pamenepo."

Ine ndinati, "Nditsitse pomwe pano, M'bale Wright," Ndipo ine ndinayima. Iye anapitirira kumtunda nakabwerako. Ine ndinapita apo ndipo sindimakhoza kutsegula chitseko. Ine ndinati, "Ambuye, ngati Inu muli mu ichi ndipo Inu mukufuna ine kuti ndilowe mu tchalitchi, nditsegulireni ine chitseko."

Ine ndinakhala pansu pamenepo ndipo ndinali kuganiza. Ndinamva wina akubwera_anabwera apo, ndipo iye anati, "Muli bwanji." Iye anati, "Kodi mumafuna kulowa mu tchalitchi umu?"

Ine ndinati, "Inde, Bwana."

Iye anati, "Ine ndiri ndi mafungulo pano." Ndinayambitsa msonkhano. Sabata loyamba, popanda kalikonse. Usiku woyamba ndinali ndi osonkhana_M'bale Wright ndi banja lake. Chinthu choyamba mukudziwa, pakutha pa sabata iwo amalephera ngakhale kuyima pa bwalo ku nyumba zawo nkomwe. Komabe mwanawankhosa anali asanabwere. M'bale Hall anapulumsidwa nthawi imeneyo_m'busa kumeneko tsopano. Sindimapeza komwe mwanawankhosayo anali. Patapita nthawi, kuchokera ku Mpingo wa Khristu, mmusi mwa phirilo, kunali msungwana wamng'ono kwa zaka zisanu ndi zinayi ndi miyezi isanu ndi itatu sanasunthe, atangogona pamenepo_apo iye anali. Inu nonse mukudziwa nkhaniyo.

168 Inde, bwana, madzulo amenewo pamene Busty Rodgers (wamkulu zedi wankhondo wakale wazimawu) atayima apo, ine ndinapita kumeneko, ndipo uko kunayima gulu la M'bale Smith kuti adzandiseke ine, kundinyoza ine pobatiza mu Dzina la Yesu. Ine ndinalowa mu madzi amatope a ku Tottensford kumene kunali kakhwawa kamene kankakukuma momwe kakanathera. Madikoni angapo anapita nane. Ine ndinati, "Ine ndayima pano madzulo ano moyimira Malembo Oyera a Mulungu." Ine ndinati, "Ine ndikuwerenga mu Baibulo apa pamene Petro anati, "Lapani aliyense wa inu, batizidwani mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu!" Ine ndinapotoloka, ndinapereka bukhulo kwa

mmodzi wa madikoni, ndinapita komweko, ndipo ndinati, "Aliyense amene akufuna kuti alape machimo ake ali wololedwa kubwera," Ndinayenda nkulowa mmadzi aja, ndipo ine ndinati, "Zikuwoneka kwa ine ngati angelo akhala pa nthambi iliyonse," ndiye ndinalowamo.

169 O, mai, pa nthawi imene ndinabatiza awiri kapena atatu, mpingo wake wonse_akazi amenewo ovala zovala za silika wabwino_kulowa mu madzi amenewo, akufuula mokweza mawu awo. Ine ndinabatiza mpingo wake wonse mu Dzina la Yesu Khristu." Inu mukudziwa izo. Ine ndiri ndi chithunzi chake.

Uko zinalipo. Chinali chiyani? Kuwonjezera kwa ukoma wanu, mwaona. Kuzisiya zokha. Mulungu amadziwa kuzichita kwake izo. Mulungu amadziwa kuzikwaniritsa kwake zinthu izi. Asiyeni azinena zomwe akufuna. Sizisitha kanthu. Zingopitirirani.

Busty Rodgers, atayima pamenepo, pamene anawona izo, iye anati, "Ndiye inenso ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse," ndipo kumka mmadzimo iye anabwera atavala zovala zake zabwino ndipo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu.

170 Pafupi zaka zitatu kapena zinayi zapitazo iwo anandiyitanira kuno ku chipatala mu New Albany. Kumeneko iye anali kufa ndi khansara; atamudya kwathunthu. Madokotala anamupatsa iye mpaka mmawa wotsatirawo kuti akhale moyo. Iye anati, "Uyu, akufa pa nthawi yomweyo, bwerani msanga.

Ine ndinapita ku chipindacho. Pamene ndinatero, nditayima pamenepo kupemphera. Iye anati, "Billy, pali utawaleza ukunyezimira pakona apo."

Ine ndinapotoloka kuti ndiyang'ane. Ine ndinati, Bus_ Busty, ndi pangano. Iwe siufa. Pangano la magazi lakupulumutsa iwe." Ine ndinayika manja anga pa iye ndinati, "Ambuye Mulungu, mwa masomphenya aja apo zatsimikizika kuti Inu muli pano, pangano Lanu latero: ndi mikwingwirima Yake ife tachiritsidwa." Ndinasanjika manja anga pa iye, ndipo pamenepo iye anakhala bwino. Anamtumiza iye kunyumba.

171 Pafupi zaka zinayi kapena zisanu_pafupi zaka zinayi_ akuweza kukwera ndi kutsika mtsinje ndi chirichonse chikumachitika ndipo pamene khansara inali itazengereza mmelo wa mimba zinafika powuma, zinali m'bulu waukulu wowuma. Madokotala, akatswiri a ku chipatala anamuwuzi iye

kuti iwo anali ndi mankhwala a cobalt amene akanawongola pamenepo, kulola kuti azimeza chakudya chambiri nthawi iliyonse (iye anali ndi vuto lalikulu pakudya; amayenera kumadya mosafulumira chotero) Iye anapita kumeneko kuti zikachitidwe. Ine sindinkadziwa kuti iye anali uko.

Ndiye pamene iwo anamupanga opereshoni, anapeza kuti zinamuyambitsa njirinjiri ndipo magazi anayima. Zinapuwalitsa mbali yake mpaka pansi chotero; ndipo chinthu chokha iye akanakhoza kuchita ndi kulira pang'ono pokha. Iye anali ndi changati pensulo chotere ndipo ankangoti "Uwa uwa uwa" ndipo iye anali kuyesa kuti alembe, akunjenjemera chotero, ndi dzanja lake labwinolo. Mbali yake ya kumanzere itayima magazi mpakana pansi. Dzanja lake "Yesu anandipulumutsa, 19 chinachake," ndipo sankakhoza kukwanitsa.

Kotero tsopano pamene mkazi wake anati, "M'bale Branham, ine sindikudziwa chimene akutanthawuza mwa izo."

Ine ndinati akazi a Rodgers, chimene iye akutanthawuza ndi chakuti inali 19 chinachake pamene iye anapulumsidwa nabatizidwa mu Dzina la Yesu kumsi uko. Ndicho chomwe chiri dipo tsopano. Iye sakuwopa kufa." Ine ndinati, "Ambuye Mulungu, msiyireni moyo wake! Ine ndikupemphera mu Dzina la Yesu kuti Inu mumusiyire moyo wake." Ndinayika manja anga pa iye. Kuyima kwa magazi kunatha, njirinjiri zinatha, ndipo iye ananyamuka pa bedi ndipo akumayima tsopano namachitira umboni.

172 Onjezerani kwa chikhulupiriro, chanu ukoma; onjezerani kwa ukoma, wanu chidziwitso; kwa chidziwitso, chanu, kudziletsa, kwa kudziletsa kwanu, chipiriro; kwa chipiriro chanu, umulungu; kwa umulungu wanu, chikondi cha pa abale; kwa chikondi cha pa abale chanu, Mzimu Woyera, ndipo Khristu adzabwera. Chifukwa pansi pa Iye chabe, Mzimu Woyera, ndi Mzimu wa Yesu Khristu mu Mpingo kuti ukwaniritse mphamvu izo.

O, mai, pano ili kotala pasiti thwelofu.

"Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye,

Chifukwa anayamba kundikonda^ (pansi apa iwe usanakhale chirichonse)

Nagula (Iye anachita chiyani?) Chipulumutso changa

Pa mtengo wa Kalvari."

Kodi ine ndikudziwa bwanji izi?_chifukwa Iye anandikonda ine choyamba.

"Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye Chifukwa anayamba kundikonda^

(Ndicho chifukwa)

Nagula chipulumutso changa Pa mtengo wa Kalvari."

173 Ine ndikulonjeza mmawa uno kwa Iye ndi mtima wanga wonse kuti mwa chithandizo Chake ndipo mwa chisomo Chake, ine ndikupemphera kuti ndifunafuna tsiku ndi tsiku mosalekeza mpaka nditamverera chirichonse cha zofunikira zonsezi zikuyenderera mu kanthunthu kokalamba kangaka. Mpaka nditakhala kuwonekera kwa Khristu Wamoyo, pakuti Iye anasandulika tchimo monga ine, kuti ine ndikhoze kukhala chilungamo cha Mulungu monga Iye. Iye, anatenga malo anga. Ambuye ndiroleni ine nditenge Ake, tsopano, chifukwa icho ndi cholinga chomwe Iye anafera.

Ndi angati amene angalonjeze chinthu chomwechi mwa chisomo cha Mulungu. Ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano ndi manja athu mmwamba.

"Ndimkonda Iye;^(Ine ndikulonjeza izi, Ambuye. Mpingo uwu ukulonjeza izi. Thunthu lonse la Yesu Khristu)

Chifukwa, anayamba kundikonda. Nagula chipulumutso changa

Pa mtengo wa Kalvari."



www.messagehub.info

Maulaliki wolalikidawa ndi
William Marrion Branham
"...mu masiku a liwu..." Chivumbulutso 10:7